Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa mphindi yokha tsopano.

2 Ambuye, ife tikusonkhananso kachiwiri chifukwa cha utumiki. Ndipo ife tikuganiza za nthawi, mmasiku oyambirira, pamene iwo onse ankabwera ku Shilo kudzafuna madalitso a Ambuye. Ndipo tsopano, usikuuno, ife tasonkhana pano kuti tidzamvetsere ku Mawu Anu. Ndipo monga ife takhala tikuphunzira mu gawo lina ili la Lemba, kuti Mwanawankhosa anali Mmodzi yekhayo amene akanakhoza kutsegula Zisindikizo, kapena kuzimasula Izo. Ndipo tikupemphera kuti usikuuno, pamene ife tiri nacho pansi pa kulingalira Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chopambana ichi, ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Mwanawankhosa atsegule Icho kwa ife usikuuno. Pakuti, ife tiri pano kuti tidzachimvetse Icho. Ndipo pamene panalibe munthu pa dziko lapansi, kapena Kumwamba, anali wokwanira, Mwanawankhosa yekhayo anapezeka wokwanira. Kotero mulole kuti Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo abwere ndi kudzatsegula Chisindikizochi kwa ife usikuuno, kuti tingokhoza kuyang'ana kudutsa katani la nthawi. Icho chingatithandize ife, ife tikukhulupirira, Atate; tsiku lalikulu ili, lamdima, lodzaza ndi tchimo limene ife tikukhalamo; chingatithandize ife ndi kutipatsa ife kulimbikira. Ife tikudalira tsopano kuti tipeza chisomo pamaso Panu. Ife tikudzipereka tokha, limodzi ndi Mawu, kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Mukhoza kukhala pansi.

3 Usiku wabwino, abwenzi. Ndi chamwayi kudzakhalanso pano usikuuno, kudzakhala mu msonkhano wa Ambuye. Ine ndinachedwerako pang'ono. Ine ndinangopita ku. . .pa chochitika chadzidzidzi, cha munthu akumwalira, membala wa mpingo uno; amayi ake ndi, kapena amabwera kuno. Ndipo iwo anati mnyamatayo anali akumwalira pa nthawi imeneyo. Kotero ine—ine ndinapita kumeneko kukawona basi m—mthunzi wa munthu atagona pa bedi, akumwalira, mwamuna wa pafupifupi usinkhu wangawu. Ndipo mu kamphindi chabe ka nthawi, ine ndinamuwona mwamuna akuimirira pa mapazi ake, akupereka matamando kwa Ambuye. Ndipo kotero, Mulungu, ngati ife tingakhale ololera kuvomereza machimo athu ndi kuchita chimene chiri cholondola, kupempha chifundo, kuyitanira pa Iye, Mulungu ndi wololera ndipo akuyembekezera kuti apereke izo kwa ife.

4 Ndipo, tsopano, ine ndikudziwa kuti mukutentha muno usikuuno. Ndipo—ndipo ndi . . . Ayi, ine ndikuganiza kuti kutenthako kwatsekeredwa. Ndipo—ndipo ife tiri . . .

5 Ine ndinazindikira usiku wathawu, kapena lero, kuti ili ndi tsiku langa lachiseveni ndiri mu chipinda chopanda kuwala, nyali zamagetsi zokha basi, mwaona; ndikuwerenga, ndi kupemphera kuti Mulungu atsegule Zisindikizo izi.

6 Ndipo panali ambiri amene analemba, mu gulu limenelo la ofunsa la- . . . kapena mafunso usiku wathawu, anali, mochuluka kapena pang'ono, osati mochuluka monga mafunso. Iwo anali ofuna kukhala ndi msonkhano wa machiritso, mulimonse; ndinkafuna kukhala ndi tsiku lowonjezera, kuti tidzakhale ndi . . . kuti tidzakhale ndi msonkhano wamachiritso Lolemba. Kotero ine—ine—ine ndikanati, ndikanakhoza, ine makamaka ndikanakhoza kuchita chimenecho ngati icho chikanakhala—chifuniro cha anthu kuti iwo akufuna kuchita zimenezo. Inu mukhoza kuchiganizira icho bwino bwino ndipo mundidziwitse ine, koma ngati inu mukungofuna kuti ndidzakhale ndi kupempherera odwala.

7 Chifukwa, ine ndayipereka nthawi yonse iyi, kwathunthu, kwa Zisindikizo izi, ndipo ndangodzipatulira ndekha kwa Zisindikizo izi.

8 Kotero inu mukhoza kuchiganiziranso icho, ndi kuchipempherera icho, ndipo kenako mundidziwitse ine. Ndipo ndidzatero, ngati Ambuye alola, ine ndikhoza. Utumiki wanga wotsatira ukakhala ku Albuquerque, New Mexico, ndipo uwo ukakhala—masiku pang'ono panobe. Ndipo ine ndiyenera kupita kwathu kukachita ntchito inayake, kukakonzekera msonkhano wina waukulu mu Arizona. Ndipo kotero, ndiye, ngati icho chitakhala chifuniro cha Ambuye! Inu muchipempherere icho, ndipo ine ndichita chomwecho, ndiye ife tidzadziwa zambiri za icho mtsogolo pang'ono.

9 Ndipo ine ndikungozindikira. Tsopano ine ndikuwona . . . Iwe ukayamba kuyankhula za matenda, pamenepo iwo amabwera, mwaona. Ine ndikumuwona dona uyu wakhala pomwe apa. Ngati chinachake sichimuthandiza iye, iye sakhala pano koma kwa kanthawi pang'ono. Kotero, ndiye, mwaona, ife—ife tingopemphera kuti Mulungu alole. Ndicho chimene inu mwabwerera pano, mwabwera kuchokera kutali. Kotero, mwaona, a—Mzimu Woyera umangodziwa chirichonse, mukuona. Kotero Iye . . .

10 Koma, mwaona, ine ndayesetsa kuyipereka nthawi iyi kwa Zisindikizo izi, chifukwa ife tinaiyikira iyo kwa zimenezo, mukuona. Koma ngati pali . . .

11 Ndi odwala angati amene ali muno, mulimonse, amene abwera kuti adzapemphereredwe? Tiyeni tiwone manja anu, ponse pozungulira, konsekonse. Oh, mai! Hum! Chabwino,

ndi angati angaganize kuti icho chingakhale chabwino, chifuniro cha Ambuye, kuti titsalire ndi kudzakhala nazo izi, kudzatenga usiku wa Lolemba, kuti tidzangopempherera odwala, kudzakhala ndi msonkhano wa machiritso Lolemba usiku? Kodi inu mungakonde mutadzachita zimenezo? Inu mungadzachite zimenezo? Chabwino, Ambuye akalola, ife tidzachita zimenezo ndiye. Mukuona? Ife tidza—ife tidzakhala nawo msonkhano wopempherera odwala, Lachitatu, kapena, Lamlungu usiku, kapena, Lolemba usiku, ndi kudzapempherera odwala.

12 Tsopano, ine ndikuyembekeza kuti izo sizikusokoneza gulu lija lomwe ine ndikubwerera nalo, kubwerera ku Arizona. M'bale Norman, kodi iye ali pano paliponse? Kodi izo zikusokoneza dongosolo lanu, M'bale Norman, chirichonse? [M'bale Gene Norman akuti, "Ayi."—Mkonzi]. M'bale Fred ndi ena nonse a inu, kodi izo ziri bwino bwino? [Enawo akuti, "Zabwino."] Mukuona? Ziri bwino. Chabwino.

13 Ndiye, Ambuye akalola, Lolemba usiku ife tidzapempherera odwala, usiku umodzi wokha basi wopatulidwira ku zimenezo, palimodzi, kudzangopempherera odwala. Tsopano, izo sizidzakhala zirinso za Zisindikizo. Ngati Ambuye akangotsegula Zisindikizo izi, kenako ife tidzapempherera odwala, Lolemba usiku.

14 Tsopano, oh, ine ndakhala kwenikweni ndikusangalala nazo izi, mopambana, pa kutumikira Ambuye pansi pa Izi! Kodi inu mwasangalala nazo Izi, kutsegula kwa Zisindikizo? [Osonkhana akuti, "Ameni!"—Mkonzi].

15 Tsopano, ife tsopano tikuyankhula kuchokera ku Chisindikizo Chachisanu kapena, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, kani. Ndipo icho chikutitengera ife tsopano kuchokera—pa ndime ya 12 ya mutu wa 6, kutsika mpaka ku ya 17. Ndi chimodzi cha Zisindikizo zazitali. Ndizo zinthu zambiri ndithu zikuchitika apa. Ndipo tsopano . . .

16 Tinene mobwereza pang'ono za usiku wathawu, kukhala ngati kuyika maziko pang'ono, nthawi iliyonse.

17 Ndipo, titi, ine—ine ndikufuna kunena chinachake, apanso. Ine ndinapeza, mu bokosi ilo, zinthu foro kapena faivi zofunika kwambiri kwa ine. Ine ndinauzidwa kuti . . . Ndipo ine ndithudi ndikufuna kupepesa. Kodi matepi ayatsidwa? Tepi yayatsidwa? Ine ndikufuna kupepesa kwa abale anga otumikira ndi kwa anthu inu pano. Iwo akuti, usiku wina pamene ine ndinali kuyankhula za—za Eliya, pa ora ilo pamene iwo anali . . . Iye ankaganiza kuti anali mmodzi yekhayo akanati adzakhale mu Mkwatulo, kapena kuti iye anali mmodzi yekhayo akanadzapulumutsidwa. Ine—ine ndinati seveni handiredi mmalo mwa seveni sauzande. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino, ine ndikutsimikiza

ndikupepesa chifukwa cha chimenecho, anthunu. Ine—ine—ine ndimadziwa bwinoko kuposa izo. Iko kunangokhala kuphonyetsa kwa kuyankhula, chifukwa ine ndimadziwa kuti anali seveni sauzande. Ine sindinachiyankhule icho molondola basi. Ine . . . Ndipo ine—ine ndikukuthokozani inu. Ndipo icho chikutanthauza kuti . . . ndine wokondwa kuti mukusamalitsa zimene ine ndikunena. Ndipo inu mukuona, ndiye, ndicho . . . Chifukwa, iwo, ndi—ndi seveni sauzande.

18 Ine ndiri nazo zolemba ziwiri kapena zitatu pa izo, zimene zinati, "M'bale Branham, ine ndikukhulupirira kuti inu munalakwitsa." Izo zinati, "Kodi iwo sanali seveni sauzande m'malo mwa seveni handiredi?"

19 Ine ndinaganiza, "Ndithudi ine sindinati seveni handiredi." Mukuona? Icho, ndiyeno ine . . . Billy . . .

20 Ndiyeno ine, chinthu choyamba inu mukudziwa, ine ndinanyamula cholemba china. Icho chinati, "M'bale Branham, inu munali . . . ine ndikukhulupirira kuti munati seveni handiredi."

21 Ndipo munthu wina anati, "M'bale Branham, kodi awo anali—masomphenya auzimu kuti—kuti kudzangokhala choyimira, ndipo inu mukufanizitsa icho ndi seveni . . . ?" Zimawayika anthu pamphepete pamene iwe uyamba kuganiza zinthu zimenezi, mwaona. Ndipo ndi zokwanira, kuti, izo zimandiyika ine pamphepete.

22 Chinachake chinachitika lero pamene Chisindikizo ichi chimawululidwa, mwakuti ine ndinachita kukayenda kwathunthu kunja ku bwalo, kumangoyendayenda ndikuzungulira, kunja ku bwalo kwa kanthawi pang'ono. Uko nkulondola. Icho basi mophweka chinali pafupifupi kundilanda mpweya wanga pomwepo kuwuchotsa kwa ine. Mukuona? Kotero inu mukanena, za manjenje? Oh, mai! Mwaona?

23 Chinthu china, mwaona, inu mukutsamira kumene pa chimene ine ndikukuwuzani inu. Ndipo Mulungu adzandifunsa ine pa chimene ine ndikukuwuzani inu. Mukuona? Ndipo kotero ine—ine ndiyenera kukhala wotsimikiza mwamtheradi basi monga kutsimikiza konse kungakhalire kotsimikizika, mwaona, za zinthu izi, chifukwa iyi ndi—nthawi yopambana kwambiri yomwe ife tikukhalamo. Eya.

24 Ine ndinali kuganizira za msonkhano wa machiritso wa Lolemba usiku. Umenewo ungadzakhoze kukusokonezani inu, M'bale Neville paliponse? [M'bale Neville akuti, "Palibe kanthu. Ndidzakhala komwe kuno."—Mkonzi]. Izo ziri bwino.

25 M'bale Neville wofunika! Ine ndikukuuzani inu, iwo basi—iwo anangopanga mmodzi, ine ndikuganiza, kenako anataya mapangidwe ake. Ndiye . . . Iye ndithudi wakhala ali—bwanawe weniweni ndi mzanga kwa ine, ndikukuuzani inu.

26 Kachisiyu tsopano wamangidwa, ndipo ali nazo zipinda za Sande sukulu ndi chirichonse chokonzeka, mu dongosolo pano. Ndipo ena a anthu inu amene muli kozungulira kuno, kozungulira Jeffersonville, amene mungafune kubwera ku tchalitchi, inu muli nawo malo abwino, ndi malo oti muzibwerako, zipinda za Sande sukulu.

27 Mphunzitsi wabwino, ndi M'bale Neville pano, kwa kalasi ya akulu, ndipo m'busa weniweni. Ine sindikunena zimenezo ngati maluwa pa iye, koma kuli bwino kuti ndimupatse iye duwa laling'ono tsopano kusiyana ndi kudzampatsa nkhata yonse iye atapita kale. Ndipo M'bale—M'bale Neville, ine ndamudziwa iye kuyambira ndiri mnyamata chabe. Tsopano, iye sanasinthe mpang'ono pomwe. Iye akadali Orman Neville, basi monga momwe iye wakhala akukhalira nthawizonse.

28 Ine ndikukumbukira ndikukacheza. Ngakhalenso iye anali nacho chisomo chokwanira kundipempha ine kuti ndipite ku guwa lake pamene iye anali mlaliki wa Methodisti kumusi kuno mu mzinda. Ndipo ife tinali ndi gulu labwino kumusi kumeneko ku Clarksville, a . . . ine ndikuganiza kuti kumeneko kumatchedwa Howard Park, Harrison Avenue Methodist church. Ine ndikuganiza kuti ndi kumene iye ayenera kuti anakupezani inu, kumusi uko, Mlongo Neville. Kumusi uko, chifukwa iye anali memba- . . .

29 Ine ndinabwererako, ndipo ndinadzanena kwa mpingo kuno, ine ndinati, "Uyo anali . . . Ndiye mmodzi wa anthu abwino kwambiri! Ndipo limodzi la masiku awa ine ndidzamubatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu." Izo zinachitika.

30 Ndi uyu apa. Ndipo tsopano iye ndi bwanawe wanga, amakhala pambali panga. Ndipo munthu waulemu chotero, wolemekezeka! Iye nthawizonse wakhala akuyima pambali panga monga ngati . . . moyandikira basi monga momwe iye angakhoze kuyimira. Chirichonse chimene ine ndinganene, iye amangokhala nane ndi kukangamira basi akutsatira. Ngakhale pamene iye anabwera muno koyamba, iye samawumvetsa Uthengawu panthawiyo, koma ankawukhulupirira Iwo ndi nkumakhala nawobe Iwo. Umenewo ndi ulemu, ndiko kulemekeza, kwa m'bale monga ameneyo. Ine sindinganene zokwanira za iye. Ndipo tsopano Ambuye amudalitse iye. Chabwino.

31 Tsopano kubwereza pang'ono za usiku wathawu, mu kumatula kwa Chisindikizo Chachisanu. Ife sitibwerera njira yonse mmbuyo usikuuno, tingobwerera utali wokwanira kuti titenge—Chisindikizo Chachisanu.

32 Tsopano, ife tikupeza kuti panali wotsutsakhristu amene anakwera, ndi kudzadzitsirizitsa yekha, kuchokera ku mphamvu zitatu. Zonse zinadzalowa mu mphamvu imodzi, ndipo anakwera kavalo wotumbululuka, "Imfa," mpaka

kuphompho lopanda malire, mpaka ku chiwonongeko, kumene iye anachokerako. Ndiyeno ife tikudzapeza pamene a . . .

33 Lemba limati, "Pamene mdaniyo alowa mkati monga kusefukira, Mzimu wa Mulungu umakweza muyezo momutsutsa iye." Ndipo ife tinaziwona izo zikutsimikiziridwa mwangwiro mu Mawu usiku wathawu, pakuti panali Zamoyo zinayi zomwe—zomwe zinayankhira kwa—nthawi zinayi zomwe wokwera uyu ankakwera.

34 Ndipo iye amakwera kavalo wosiyana nthawi iliyonse, kavalo woyera, ndipo kenako kavalo wofiira, ndi kavalo wakuda, ndipo kenako kavalo wotumbululuka. Ndipo ife tinapeza, mitundu imeneyo, ndi chimene iyo inali ndi chimene iyo inachita. Kenako tinazitengera izo kubwerera mmbuyo momwe mmibadwo ya mipingo, ndipo ndendende ndicho chimene iyo inachita, mwangwiro basi.

35 Chotero, mukuona, pamene Mawu a Mulungu akulumikizana pamodzi, izo zimatanthauza kuti Iwo akulondola, mukuona. Eya. Ine ndikukhulupirira, chirichonse chimene chimagwirizana ndi Mawu a Mulungu nthawizonse chimakhala "ameni." Mukuona?

36 Tsopano, monga munthu atati anali nawo masomphenya, ndipo nkunena kuti iwo anali. Oh, iwo amadziwa kuti Ambuye anawapereka iwo, chifukwa iwo anabwera ndi mphamvu yaikulu. Chabwino, masomphenyawo akhoza kukhala abwino bwino. Koma ngati iwo sakhala limodzi ndi Mawu, ndipo nkumatsutsana ndi Mawu, basi iwo si olondola. Mukuona?

37 Tsopano, tsopano akhoza kukhala kuti ali pompano, abale ena kapena mlongo a Mormon. Ndipo akhoza kukhalapo ena amene ati adzatenge matepi awa, tsopano. Ndipo ine sindikufuna kunena zimenezo . . . Ena a anthu abwino kwambiri omwe ine ndi inu tingafune kukumana nawo, akhoza kudzakhala—kukhala mwa anthu a Mormon; anthu a mtundu wabwino kwambiri. Ndiyeno wawo—mneneri wawo, Joseph Smith, yemwe anthu Amethodisti anamupha kuno ku Illinois, pa ulendo wawo kumeneko. Ndipo kotero ndiye uyo—munthu wabwino uyo, ndipo masomphenyawo, ine sindikukaikira konse koma kuti iye anali nawo masomphenyawo. Ine ndikukhulupirira kuti iye anali munthu woonamtima. Koma masomphenya omwe iye anali nawo anali otsutsana ndi Lemba. Mukuona? Chotero, iwo ankayenera kukhala ndi Baibulo la Mormon, kuti—kuti azipange zimenezo. Mukuona?

38 *Ili* ndi Limenelo apa, kwa ine. Ndi limenelo. Ndi chifukwa chake, Mawu okha basi. Ndi Amenewo. Mukuona?

39 Nthawi ina, a—a—mtumiki anabwera kuno kuchokera ku dziko lakunja, ndipo iye . . . Ndipo ine ndinamuwona iye akutuluka ndi a—a . . . akukwera nkumazungulira mu galimoto, ali ndi yemwe sanali . . . ali ndi a—dona. Ndipo iwo anabwera ku

msonkhano. Ndipo ine ndinapeza kuti, iwo anali atayendetsa kwa masiku awiri kapena atatu, okha iye ndi mkaziyo, mu msonkhano, kubwera ku msonkhano, limodzi. Ndipo mkaziyo anali atakwatiwa, nthawi zitatu kapena zinayi zosiyanasiyana.

40 Ndipo mtumiki uyu analowa nafika pofikira ku hotelo kumene ine ndinali, ndipo anathamanga nadzagwirana nane chanza. Ndipo ine ndinagwira dzanja lake, ndinadzuka ndipo ndinali kuyankhula ndi iye. Ine ndinamufunsa iye, ndinati, "Mukadzati muli nayo nthawi, kodi ndingadzakhoze kuyankhula nanu mchipinda changa kwamphindi chabe?"

Iye anati, "Ndithudi, M'bale Branham."

41 Ine ndinamutengera iye ku chipindacho. Ndipo ine ndinati kwa mtumikiyo, ine ndinati, "Abusa, abwana, ndinu mlendo mdziko lino." Ine ndinati, "Koma dona uyu ndi wodziwika ndithu." Ine ndinati, "Kodi, kapena, inu mwabwera njira yonse kuchokera ku malo *akuti-ndi-akuti*, mpaka kudzafika ku malo *akuti-ndi-akuti* awa?"

Anati, "Inde, bwana."

42 Ndipo ine ndinati, "Kodi inu simukuwopa kuti icho chikhala ngati . . . ? Ine—ine sindikutero . . . sindikukukaikirani inu, koma kodi inu simukuganiza kuti icho chinyezimiritsa pa mbiri yanu monga mtumiki? Kodi inu simukuganiza kuti ife tiyenera kuyika chitsanzo chabwinoko pang'ono kuposa chimenecho?"

Ndipo iye anati, "Oh, dona uyu ndi woyera mtima."

43 Ine ndinati, "Ine—ine sindikukaikira zimenezo." Koma ndinati, "Koma, m'bale, chinthu chake ndi chakuti, aliyense amene akuyang'ana pa iye si woyeramtima, mwaona, omwe akuyang'ana pa zimene inu mukuchita." Ndipo ndinati, "Ine ndikukhulupirira kuti inu muyenera kukhala wosamalitsa. Chimenecho chinali basi m'bale mmodzi kwa mzake." Ndipo iye anati . . . Ine ndinati, "Donayo wakwatiwapo kanayi kapena kasanu tsopano."

Ndipo anati, "Inde, ine ndikuzidziwa zimenezo." Anati, "Inu mukudziwa, ine—ine . . . "

44 Ine ndinati, "Inu simumaphunzitsa zimenezo mu mpingo wanu kwanu, sichoncho inu, pa zimenezo?"

45 Kotero anati, "Ayi. Koma," anati, "inu mukudziwa, ine ndinali ndi masomphenya a zimenezo, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Chabwino, zimenezo nzabwino." Ine ndinati . . .

46 Iye anati, "Kodi inu mukusamala?" Ndinati, "Ine ndikukhulupirira kuti ndikhoza kukuwongolani inu pang'ono pokha pa kuphunzitsa kwanu kokhudza zimenezo."

47 Ndipo ndinati, “Chabwino.” Ndipo iye. . .ine ndinati, “Ine—ine—ine ndingakhale wokondwa kuti ndidziwe zimenezo, bwana.”

48 Ndipo iye anati, “Chabwino,” anati, “inu mukudziwa, mmasomphenya awa,” iye anati, “Ine ndinali nditagona.”

Ndipo ine ndinati, “Eya.” Ine ndinawona, pamenepo, kuti anali maloto. Mukuona?

49 Ndipo iye anati, “Wanga—mkazi wanga,” anati, “iye anali akukhala ndi mwamuna wina,” ndipo anati, “ndi kumathamanga kuzembera pa ine.” Ndipo anati, “Kenako iye anabwera kwa ine, ndipo iye anati kwa ine, ‘Oh, wokondedwa, undikhululukire ine, undikhululukire ine!’ Anati, ‘Ine—ine—ine—ndikupepesa chifukwa chochita zimenezo. Ine ndikhala woona kuchokera tsopano mpaka mtsogolo.’” Anati, “Zedi, ine ndinkamukonda iye kwambiri, ine ndinangomukhululukira iye, ndinati, ‘Chabwino.’” Ndipo anati, “Ndiye. . . ”

50 Ndipo anati, “Kodi inu mukudziwa chiyani? Ndiye ine ndinapeza tanthauzo la masomphenya awa.” Ndinati, “Mkazi wake anali ameneyo.” Anati, “Zedi, iye wakhala akukwatiwa, ndi—ndi zina zotero, ndipo nthawi zonse izi.” Ndipo ananena, kuti, “Ndi zabwino bwino kwa iye kuti akwatiwe, chifukwa Ambuye amamukonda iye mochuluka kwambiri. Iye akhoza kukwatiwa nthawi zochuluka monga mmene iye akufunira, malingana ngati. . . ”

51 Ine ndinati, “Masomphenya anu anali okoma mwamphamvu, koma iwo anali kutali ndi Njira yeniyeniyo apa.” Ine ndinati, “Ndizo—izo ndi zolakwika, mwaona. Inu simukuyenera kumachita zimenezo.” Kotero kuti. . .Mukuona?

52 Koma pamene inu muwona Lemba likulumikizana ndi Lemba, kuchipangitsa icho kupitirizika mosasintha pamene iwo abwera pamodzi. Malembawo, pamene Awa akulekezera apa, Enawa apa amabwera ndi kudzalumikiza mmenemo, ndi kudzajambula chithunzi chonsecho.

53 Monga kuyika mawu opingasa pamodzi, chomwecho. Mukapeza chidutswa chomwe chikukwaniramo. Pamene palibenso china chomwe chingakwanemo. Ndiye inu mukukonza chithunzicho.

54 Ndipo alipo Mmodzi yekha amene angachite zimenezo, ndiye Mwanawankhosa, ndipo kotero ife tikuyang’anira kwa Iye.

55 Koma ife tikupeza kuti pamene awa, wokwera uyu, iye anali wokwera mmodzi yemwe ankakwera akavalo awa. Ndiyeno ife tinamutsatira iye mpaka mmusi, tinawona zomwe iye anachita ndi chirichonse, ndipo tinadzapeza, mmbuyomo mmibadwo ya mpingo kuti ndizo ndendende zimene iye anachita.

56 Ndiyeno pamene iye anatuluka pa chirombo chinachake ndi kukachita chinthu chinachake, ife tinapeza kuti apo panali

china chomwe chinatumizidwa kukamenyana ndi chimene iye anachitacho.

57 Panali chimodzi chomwe chinatumizidwa kwa m'badwo woyamba, cha mwanawankhosa . . . cha mkango. Amenewo anali Mawu, ndithudi, Khristu.

58 Chotsatira chinali ng'ombe, mu nthawi ya m'badwo wa mdima, pamene—pamene a—mpingo unali utachita bungwe ndipo unali utavomereza miyambo mmalo mwa Mawu.

59 Ndipo kumbukirani, chinthu chonsecho chakhazikika pa zinthu ziwiri: chimodzi, wotsutsakhristu; chinacho, cha Khristu.

60 Chikadali chinthu chomwecho lero. Palibe Akhristu a theka. Palibe munthu woledzera-wosaledzera; palibe mbalame zakuda-zoyera; ayi, ayi; palibe wochimwa-woyera. Ayi. Ndiwe mwinamwake wochimwa kapena woyeramtima. Mukuona? Palibe kungokhala pakatikati. Ndiwe mwina wobadwa kachiwiri kapena ndiwe wosabadwa kachiwiri. Ndiwe mwina wodzazidwa ndi Mzimu Woyera kapena ndiwe wosadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ziribe kanthu kaya iwe unakhala ndi zogirigisha zingati, ngati iwe sunadzazidwe nawo Mzimu Woyera, ndiwe wosadzazidwa nawo Iwo. Mukuona? Ndipo ngati iwe wadzazidwa nawo Iwo, moyo wako umawonetsera izo, umapita mpaka mmwamba kwa Iwo. Mukuona? Palibe aliyense amene ayenera kumuuza aliyense za izo. Iwo amaziwona izo, mwaona, chifukwa Ndi Chisindikizo.

61 Tsopano, ndipo ife tikuzipeza zirombo zimenezo, momwe izo zinkakwerera nthawi iliyonse. Chimodzi chitatumizidwa pa utumiki wake, mu mphamvu zandale, kulumikizitsa mphamvu zachipembedzo ndi—ndi mphamvu zandale, pamodzi. Ife tikupeza kuti, Mulungu anatumiza mphamvu Yake kukamenyana nacho icho. Ife tinapita mmbuyo momwe ndi kuwona chomwe m'badwo wa mpingo unali, ndi kuyang'ana mmbuyo; ndipo apo izo zinali, ndendende basi mwanjira imeneyo.

62 Kenako ife tinapeza kuti, m'badwo wina unabwera motsatira, ndipo mdaniyo anatumiza wotsutsakhristu pansi pa dzina la chipembedzo, pansi pa Dzina la Khristu, pansi pa dzina la Mpingo. Inde, bwana. Anatuluka kunja pansi pa dzina la Mpingo, mpakana. "Umenewo unali Mpingo weniweni," iye anatero. Mukuona?

Wotsutsakhristu si Russia. Wotsutsakhristu si zimenezo.

63 Wotsutsakhristu ndi woyandikira kwambiri ndi Chikhristu chenicheni, mpaka, Baibulo linati, "Iye akanadzapusitsa chirichonse chomwe sichinakonzedweretu." Uko nkulondola. Baibulo linanena kuti, "Mmasiku otsiriza, chirichonse chimene sichinakonzedweretu, Osankhidwa." Ilo limati, "Osankhidwa!" Tsopano, aliyense, atengeni mawu amenewo ndi kubwerera nawo iwo mmphepete mwanu, muwona chomwe iwo

amatanthauza. Ilo limati, "Osankhidwawo, okonzedweratu." Mukuona? "Iye adzapusitsa aliyense wa iwo amene maina awo sanali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuchokera ku maziko a dziko lapansi."

64 Pamene Mwanawankhosa anaphedwa, maina analembedwa pa Bukhu. Iye akuyima mu Malo Woyera usikuuno, mu Ulemelero, monga Wopembedzera, kupembedzera mmodzi aliyense wa miyoyo iyo yomwe maina awo ali pa Bukhu limenelo. Ndipo palibe aliyense akulidziwa dzina limenelo koma Iye. Iye ndi Mmodziyo amene ali nalo Bukhulo mu dzanja Lake, ndipo Iye akudziwa. Pamene mmodzi wotsirizayo adzalowa mmenemo, ndiye masiku Ake opembedzera adzatha. Iye adzatulukira pamenepo kudzatenga zomwe Iye wazipembedzera. Iye akuchita ntchito ya Muwomboli Wachibale tsopano; ndipo akubwera kudzalandira Ake Omwe. Oh, mai!

65 Icho chiyenera kumupangitsa Mkhristu aliyense ku—kuyamba kudzifufuza yekha, ndi kukwezera manja ake pamaso pa Mulungu, ndi kumati, "Ndiyeretseni ine, O Ambuye! Muyang'ane mmoyo mwanga, ndipo—ndipo mundilole ine—mundilole ine ndiwone kumene kuli mbali yanga yoipa. Mundilole ine ndiyichotse iyo pa njirayi, mwamsanga kumene." "Pakuti ngati wolungama adzapulumutsidwe movutikira, nanga wochimwa ndi wopanda umulungu adzawonekera pati?" Ndi nthawi yodzifufuza.

66 Ndipo ngati mukanachiyika icho, ndi kufuna kutero . . . ndi kupereka Mawu awa. (Tsopano, ine sindikufuna kuti, kuti andifunse ine funso pa izi, chifukwa izo zimandifikitsa ine pa china; ine ndikutanthauza, polemba mafunso anu. Ine ndikuganiza kuti mafunsowo alembedwa kale, mulimonse.) Iyi ndi nthawi yofufuza chiweruzo. Uko nkulondola. Tsopano, ife tidzazipeza izo pa—pa Malipenga pamene tidzafike ku zimenezo, pamene Ambuye adzapereke, kapena Mbale, ndipo ife tidzazipeza pa kufufuza chiweruzo uko, pamene basi Matsokawo asanapite. Ndipo—ndipo ife tikuwona kuti izo ndi zoona. Ndipo Angelo atatuwo amene anakantha dziko lapansi, akufuula, inu mukudziwa, "Tsoka! Tsoka! Tsoka kwa okhala mdziko lapansi!"

Ndipo ife tikukhala mu nthawi yowopsya, nthawi imene . . .

67 Inu mukuona, zinthu izi zomwe ife tirimo tsopano, zomwe tikuziphunzira pakali pano, zikuchitika Mpingo utapita kale, mwaona, zinthu izi mu nthawi ya Chisautso. Ndipo ine ndikuganiza kuti izo ziyenera kukhazikika moona mu mtima wa wokhulupirira aliyense, kuti Mpingo uwu sudzadutsa konse mu nthawi ya Chisautso. Inu simungawuyike, paliponse, Mpingo mu Chisautso. Ine . . . Inu muwuyike mpingo mmenemo, koma osati Mkwatibwi. Mwaona, Mkwatibwi wapita kale.

68 Chifukwa, mwaona, Iye, Iye alibe tchimo limodzi, palibe kanthu komutsutsa Iye. Chisomo cha Mulungu chamuphimba

Iye. Ndipo bulitchi yatengera tchimo lirilonse kutali kwambiri, palibe ngakhale kukumbukirika kwa ilo nkomwe; palibe kanthu koma chiyero, wangwiro, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Oh, izo ziyenera kumupangitsa Mkwatibwi kugwada pa mawondo Ake ndi kulirira kwa Mulungu!

69 Ine ndikuganiza za kankhani kakang'ono; ngati ine sindikutenga nthawi yanu yochuluka kwambiri tsopano, mu zoyambirira izi. Ndiri . . . Ine—ine ndimachita izi kwa cholinga, kuti ndimverere, mpaka ine nditamverera Mzimu moyenera basi, kuti ndiyambepo.

70 Ichi ndi—ichi ndi chinthu chopatulika. Mukuona? Ndicho, mwaona, ndani amene akudziwa zinthu zimenezo uko? Palibe koma Mulungu. Ndipo izo sizinkayenera kuti ziwululidwe, ndipo ndizotsimikiziridwa mu Baibulo kuti izo sizikanadzawululidwa, mpaka tsiku lino. Uko nkulondola ndendende. Mukuona? Izo zinali—izo zimapenekeredwa; koma tsopano ife tiyenera kuzitenga izo ndendende, Choonadi, Choonadi chotsimikiziridwa. Mukuona? Zindikirani.

71 Tsopano, uko kunali a—mtsikanana wamng'ono kumadzulo, yemwe anali—iye anagwa mchikondi ndi . . . Mwamuna anagwa mchikondi ndi iye. Monga wogula ng'ombe, anabwera kumeneko mmalo mwa Armour Company. Ndipo—ndipo iwo anali ndi—wamkulu . . .

72 Bwanayo anabwera tsiku lina, mwana wa bwanayo kuchokera ku Chicago, ndipo, zedi, iwo anali atavala mwachizolowezi, zovala zakumadzulo. A—atsikanawo kumeneko, iwo anavala; aliyense ankafuna kuti amutenge mnyamata uyu, ndithudi, inu mukudziwa, chifukwa ameneyo anali mnyamata weniweni wa bamboyo. Kotero, iwo anavala zovala zawo zakumadzulo.

73 Ndipo—ndipo iwo amachita zimenezo kumadzulo uko. Iwo angotsiriza kumene umodzi wa zochitika zimenezo. Ndipo M'bale Maguire, ine ndikuganiza kuti iye ali pano tsopano, iwo anamugwira iye kumusi kwa mzinda alibe zovala zake za kumadzulo, ndipo iwo anamuponyera iye mu—mu ndende. Ndipo anamuyimba iye mulandu mosalongosoka, ndi kumulipiritsa iye chifukwa cha izo, ndipo kenako anampangitsa iye kupita kukagula chovala chakumadzulo. Ndipo ine ndinawawona ena onse a iwo akuyenda ndi mifuti pafupifupi yayitali *chonchi*, itapachikika pa iwo. Iwo amangokhala ngati mbadwa zakumeneko. Iwo akuyesetsa kukhala moyo wa chinachake cha mmasiku ammbuyo apitawo, apitawo. Mukuona?

74 Ndiyeno, mu Kentucky, inu mukuyesetsa kukhala moyo wa mmasiku ammbuyo wa akummawa kuno, akubwererabe mu Chigwa cha Renfro ndi zinthu. Inu mumakonda kubwerera ku masiku akale. Pali chinachake chikuyambitsa zimenezo.

75 Koma pamene zibwerera mmbuyo, kuti mubwerere ku Uthenga wa pachiyambi, inu simukufuna kuchita zimenezo. Inu mukufuna chinachake chamakono, mukuona. Zimangosonyeza kuti, mwaona, inu—inu . . . pali . . .

76 Ndipo nchiyani chimamupangitsa a—munthu kuchita cholakwika? Nchiyani chimamupangitsa iye kumwa ndi kumapitirirabe, kapena mkazi kuchita cholakwika? Ndi chifukwa chakuti iye akuyesetsa kuti . . . Muli chinachake mwa iye, chikuchita ludzu. Muli chinachake mwa iye, chikuchita ludzu. Ndipo iwo akuyesetsa kuthetsa ludzu loyera ilo ndi zinthu za mdziko. Pamene, Mulungu anayenera kukhala chothetsa ludzucho. Iye anakupangani inu mwanjira imeneyo, kuti muzimva ludzu. Ndi chifukwa chake inu mumamva ludzu la chinachake. Mulungu anakupangani inu mwanjira imeneyo, kuchitira kuti mudzathetsere ludzu loyera ilo kwa Iye. Mukuona? Koma pamene inu muyesetsa kuthetsa ludzu ilo . . . Angakhumbe bwanji aliyense kuchita zimenezo! Inu mulibe ufulu wochitira zimenezo, kuyesetsa kuti muthetse ludzu lopatulika ilo lomwe inu mumamverera ludzu la chinachake, ndipo, kenako, ndipo inu nkulitembenuzira ilo kwa dziko lapansi, kuyesetsa kulikhutitsa ilo ndi dziko lapansi. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Pali chinthu chimodzi chokha chimene chidzakhutitse ilo, ndipo ndicho Mulungu. Ndipo Iye anakupangani inu mwanjira imeneyo.

77 Kotero, awa—atsikana aang'ono awa anavala a—zovala zachizolowezi zakumadzulo chifukwa cha mnyamata uyu pamene iye—iye anatulukira. Ndipo aliyense wa iwo anali wotsimikiza kuti amutenga mnyamata uyu.

78 Kunali msuweni wamng'ono kumeneko kodyetsera ziwetoko, ndipo iye anali wamasiye, ndipo kotero iye ankangochita zonse a—ntchito zonse za awa. Chifukwa, iwo ankayenera kukonza zikhadabo zawo, inu mukudziwa, ndipo iwo sakanakhoza kutsuka mbale chifukwa cha manja ndi zinthu. Ndipo iye anali akugwira ntchito yeniyeni yonse yolemetsa.

79 Ndiyeno, potsiriza, pamene mnyamatayo anabwera, iwo anapita kumeneko ndipo anakamutenga iye pa ngolo yachikale, yakumadzulo. Ndipo iwo analowa mmenemo, akuwomba mifuti yawo ndi kumapitirira, inu mukudziwa, ndi kumachita mwasewero. Ndipo usiku umenewo iwo anali ndi kuvina kwakukulu kumeneko, pa—pa kavinidwe kachikale, ndipo onse osamalira ziweto ali pamenepo, pafupifupi, ndi kumabwera mmenemo ndi mavinidwe awo, ndi zina zotero. Ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, bwanji, izi zinkapitirira, chinali chisangalalo cha masiku awiri kapena atatu.

80 Kenako, usiku wina, mnyamata uyu anatuluka panja, mpaka . . . pa malowo, kukangopumulira pang'ono ku kuvinako,

ndipo anachoka kwa atsikana awa. Ndipo iye anapezeka kuti wayang'ana, akupita mmusi cha ku khola. Uko kunadutsa mtsikana wamng'ono, wowoneka ngati wamasanza. Ndipo iye anali ndi beseni lodzaza ndi madzi, iye amatsuka mbale. Ndipo iye anaganiza, "Ine sindinamuwone iye poyamba. Ine—ine ndikudabwa kuti iye wachokera kuti?" Kotero iye anangoziyika izo moyenera kuti apite chozungulira ku mbali ya nyumba ya—antchito, ndipo anapita kumusi uko ndi kubwereranso, ku mbali ya khola, ndi kukakumana naye iye.

81 Iye anali wosavala nsapato. Iye anayima. Iye anaweramitsa mutu wake pansi. Iye anawona yemwe iye anali, ndipo iye anali wamanyazi kwambiri. Iye ankamudziwa munthu wamkulu uyu. Ndipo iye anali msuweni chabe kwa atsikana ena awo. Bambo wawo anali woyang'anira wa pa malo akunja aakulu a Armour awa, kotero iwo anapitiriza . . . Iye anapitiriza kuyang'ana pansi. Iye anali wamanyazi chifukwa chosavala nsapato.

82 Iye anati, "Dzina lako ndi ndani?" Iye anamuuza iye. Anati, "Bwanji iwe sunapite kunja uko ku . . . kumene ena onse a iwo ali?" Ndipo iye anakhala ngati anawiringula.

83 Ndipo kotero, usiku wotsatira, iye anamupenyanso iye kachiwiri. Potsiriza . . . Iye anali atakhala kunja uko. Ndipo iwo onse anali akumapitirirabe, chirichonse. Iye—iye anadzakhala pa mpanda wa khola ndikumamuyang'anira iye kuti abwere, kudzataya madzi otsukira mbale kunjako. Ndipo iye ankamuyang'anira iye. Ndipo iye anati kwa iye, iye anati, "Iwe ukudziwa cholinga changa chenicheni chobwerera kuno?"

Iye anati, "Ayi, bwana, ine sindikudziwa."

84 Anati, "Cholinga changa chobwerera kuno ndicho kudzasaka mkazi." Iye anati, "Ine ndapeza khalidwe mwa iwe limene enawo alibe." Ine ndinali kuganiza za Mpingo, inu mukuona. Anati, "Kodi iwe ungakwatirane nane?"

Iye anati, "Ine? Ine? Ine—ine sindingakhoze kuganiza za chinthu choterocho, ine."

85 Mwaona, ameneyo ndi mwana weniweni wa abwanawo. Iye anali mwini wa makampani onse ndi malo owetera ziweto kuzungulira kumeneko, ndi chirichonse, mukuona. Anati, anati "Inde." Anati, "Ine—ine sindinakhoze kumupeza mmodzi ku Chicago. Ine—ine ndikufuna mkazi weniweni. Ine ndikufuna mkazi wakhalidwe. Ndipo chinthu chimene ine ndikuchifunafuna, ine ndachiwona icho mwa iwe." Anati, "Kodi iwe ungakwatiwe ndi ine?"

Iye anati, "Chabwino . . ." Icho chinamunyumwitsa iye. Ndipo iye anati, "Inde."

86 Ndipo iye anati, "Chabwino . . ." Anamuuza iye kuti akanadzabwereranso. Anati, "Tsopano, iwe udzingokonzeka, ndipo chikatha chaka kuchokera lero ine ndidzabwereranso.

Chabwino . . . Ndipo ine ndidzakutenga iwe, ndipo ine ndidzakutengera iwe kutali kuchoka kuno. Iwe sumakagwiranso ntchito monga chonchi. Ine ndidzakutenga iwe. Ndipo ine ndidzapita ku Chicago, ndipo ndikakumangira iwe nyumba yonga yomwe sunaiwonepo konse."

87 Iye anati, "Ine ndiribe, nkomwe—sindinakhalepo ndi nyumba. Ndine wamasiye," iye anatero.

88 Iye anati, "Ine ndidzakumangira iwe nyumba, yeniyeni." Anati, "Ine ndidzabweranso."

89 Iye ankalumikizana naye mkaziyo, mu nthawi iyo, ya chaka. Iye anagwira ntchito iliyonse imene iye akanakhoza kugwira, kuti asunge ndalama zake zokwanira dola pa tsiku, kapena chirichonse chimene iye ankakhala nacho ndi gulu lake, kuti agulire diresi lake la chikwati. Choyimira changwiro cha Mpingo! Mukuona? Mukuona? Iye anakonzekera zovala zake.

90 Ndipo, inu mukudziwa, pamene iye anawonetsera chovala chaukwati ichi, ake—asuwani ake anati, "Bwanji, iwe mwana wosauka, wopusa. Iwe ukutanthauza kuganiza kuti mwamuna ngati amene uja angakhale ndi chochita chirichonse ndi iwe?"

91 Iye anati, "Koma iye anandilonjeza ine." Ameni. Anati, "Iye wandilonjeza." Anati, "Ine ndikukhulupirira mawu ake."

92 "Oh, iye amangokupusitsa iwe." Anati, "Ngati iye akanatenga winawake, iye akanatenga mmodzi wa iwo."

93 "Inde," anati, "koma iye anandilonjeza ine. Ine ndikuyembekezera chimenecho." Ameni. Ine ndikutero, nanenso.

94 Kotero, nthawi inayamba kuyandikira ndi kuyandikira. Potsiriza tsikulo linafika, ora linalake iye anali woti afika kumeneko, kotero iye anadziveka mu chovala chake. Ndipo iye anali asanamve konse kuchokera kwa iye. Koma iye ankadziwa kuti iye akanadzakhala kumeneko, kotero iye anadziveka mu zovala zake za chikwati, anakonzekera zinthu.

95 Chabwino, ndiye iwo anaseka kwenikweni pamenepo. Chifukwa, bwana wamkuluyo anali atatumiza kwa—kwa woyang'anirayo, kapena—kapena kwa . . . Atsikana ena onsewo sanamve kanthu za icho, kotero icho chonse chinali chinthu chachinsinsi kwa iwo. Icho chiri, panonso. Icho ndithudi chiri.

96 Koma mtsikana uyu, pamaso pa zonse zimenezo, anakhazikika pa maziko a mawu ake kuti iye akanadzabwerera iye.

97 Kotero, iwo anayamba kuseka. Ndi kukolowekana manja awo wina ndi mzake, ndi kumavina momuzungulira iye. Anati, "Ha!" Kumamuseka, inu mukudziwa, monga choncho, anati, "Mwana wosauka, wamng'ono, wopusa!"

98 Iye anangoyima pamenepo, wopanda manyazi nkomwe mwa iye. Iye anali atagwirizira maluwa ake. Ndipo chovala chake chaukwati chonse chitakonzedwa; iye anali atavutikira, inu mukudziwa. "Mkwatibwi Wake wadzikonzekeretsa Yekha." Mukuona? Iye anangogwirizirabe maluwa ake, akuyembekezera.

99 Iwo anati, "Tsopano, ine ndinakuwuza iwe kuti izo zinali zolakwika. Ukuwona, iye sakubwera."

Anati, "Ine ndiri ndi maminiti asanu ena." Anati, "Iye akhala ali pano."

Oh, iwo amangomuseka!

100 Ndipo basi pafupifupi nthawi imene koloko yakaleyo imagunda mpaka maminiti asanu, iwo anamva akavalo akuthamanga, mchenga ukugudubuzika pansi pa magudumu. Ngolo yakaleyo inayima.

101 Iye analumpha kuchoka pakati pa iwo, ndi kutuluka pa khomo. Ndipo iye analumpha kuchokera mu ngolo, ndipo iye anawulukira mmikono mwake. Iye anati, "Zonse zatha tsopano, wokondedwa." Anawasiya asuweni ake akale aang'ono a zipembedzo atakhala pamenepo, akuyang'ana. Iye—iye anapita ku Chicago, kunyumba yake.

102 Ine ndikudziwa za lonjezo lina lalikulu longa limenelo, nalonso, panobe. "Ine ndapita kukakukonzerani inu malo; ndidzabweranso kudzakulandirani inu." Iwo akhoza kumanena kuti ife ndi openga. Koma, m'bale, kwa ine, pakali pano, ndipo Zisindikizo izi zikumatulika monga chonchi, pansi pa chinthu chauzimu ichi, ine ndikukhoza pafupifupi kumva mkokomo, pamene koloko ya nthawi iyo ikugundira kulowa mu Muyaya uko. Ine ndikukhoza pafupifupi kumuwona Mngelo ameneyo atayima pamenepo ndi kumati, pamapeto a Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri uyo, "Nthawi sidzakhalaponso." Mkwatibwi wamng'ono, wokhulupirika uyo adzawulukira mmikono mwa Yesu limodzi la masiku amenewa, kutengedwera ku Nyumba ya Atate. Tiyeni tiganizire za zinthu izi pamene ife tikupita motsatira tsopano.

103 Zindikirani utumiki wa mkango, Mawu; ng'ombe, kuvutikira ndi nsembe; kuthyathyalika, kwa okonzansowo; ndi—m'badwo wa mphungu, ukubwera mkati, ndiwo woti udzawulule ndi kudzatenga zinthu izi ndi kuziwonetsera izo.

104 Tsopano ife tinazipeza, mu msonkhano wa usiku wathawu, aponso, chinsinsi chachikulu chomwe chinatsegulidwa ndi Chisindikizo ichi, chimene chinali mwamtheradi mosiyana ndikumvetsa kwanga kwakale. Kumangopenekera kuti izo zinali zolondola, ine nthawizonse ndinkailola miyoyo ya pansi pa guwa imeneyo kuti ikhale Akhristu ofera oyambirira. Koma ife tinapeza, usiku wathawu, pamene Ambuye Mulungu anamatula Chisindikizo chimenecho kwa ife, izo mwamtheradi ndi zosatheka. Sanali iwowo. Iwo anali atapita ku Ulemelero,

mpaka ku mbali inayo, ndipo kumeneko iwo anali. Ife tinapeza kuti iwo anali Ayuda amene ati adzabwere mu nthawi, pamene a . . .

105 Kuchokera pa kuyitana tsopano, kwa handiredi ndi forte-foro sauzande, zomwe ife titi tilowemo usikuuno ndi mawa. Ndipo—ndipo pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri, handiredi ndi forte-foro sauzande akuitanidwa.

106 Ndiyeno ife tikupeza, kuti iwo anali ofera amene anaphedwa, ndipo komabe anali asanati . . . Anali atavala mikanjo yoyera, koma maina awo anali ali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndipo iwo anapatsidwa mikanjo yoyera, mmodzi aliyense wa iwo. Ndipo ife tinazitenga zimenezo. Ndipo si kanthu mdziko, ine sindikukhulupirira, koma gulu limenelo la—la Ayuda limene linadutsa mu nthawi ya chisautso choyambirira. Pamene, mu nthawi ya nkhondo zotsiriza izi, iwo anali . . . iwo atero . . . Iwo ankayenera kudedwa ndi aliyense. Ndipo Eichmann anapha mamillioni a iwo mu Germany. Inu mwangoumva kumene mlanduwo. Mamillioni a anthu osalakwa anaphedwa, Ayuda, basi chifukwa chakuti iwo anali Ayuda; popanda chifukwa china.

107 Baibulo linanena apa, kuti, "Iwo anaphedwa chifukwa cha umboni wawo wa Mulungu, chifukwa—cha Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anagwirizira." Tsopano ife tinapeza kuti Mkwatibwi anali Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu. Awa analibe umboni wa Yesu Khristu.

108 Ndipo ife tinapeza kuti Baibulo limanena, kuti, "Israeli yense, Israeli wokonzedweratu, adzapulumutsidwa," Aroma 11. Tsopano ife tikudziwa zimenezo. Ndipo pamenepo ife tinawona miyoyo imeneyo.

109 Tsopano penyani kuyandikira kwake. Nchifukwa chiyani izi sizikanakhala mmbuyomo? Chifukwa izo zinali zisanachitikepo kale. Tsopano inu mukukhoza kuziwona izo, mwaona. Mwaona, Mzimu Woyera waukulu, powona zinthu zimenezo zikubwera mmusi kudutsa a—mibadwo ndi nthawi. Ndipo tsopano izo zikuwululidwa, ndiyeno iwe ukuyang'ana mmenemo ndi kuwona kuti ndicho Choonadi. Apo ndi pamene izo ziri.

110 Tsopano, iwo anali—iwo anali ofera mu chisautso, kapena chisautso choyambirira, cha Eichmann. Tsopano, iwo akungoimira chabe ofera a handiredi ndi forte-foro sauzande, amene ife tikulowamo, pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri. Mukuona?

111 Ndipo Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ndi chinthu chimodzi chabe, ndizo zonse, ndipo ichi, "Kunali chete Kumwamba kwa danga la theka la ora." Ndipo tsopano Mulungu yekha akhoza kuwulula chimenecho. Icho

sichinaphiphiritsidwe nkomwe, paliponse. Limenelo ndi mawa usiku. Mundipempherere ine. Mukuona?

112 Tsopano, ife tikuzindikira tsopano, pamene ife tikupita mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Tsopano Atate Akumwamba atithandize ife pamene ife tikukhazikika tsopano ku Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Tsopano ndime ya 12 iyi ya mutu wa 6.

> *Ndipo ndinawona pamene iye . . . anatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, ndipo, taonani, kunali chivomezi chachikulu; ndipo dzuwa linakhala lakuda monga chiguduli cha ubweya, ndipo mwezi unakhala ngati magazi;*
>
> *Ndipo nyenyezi zakumwamba zinagwera pa . . . dziko lapansi, ngakhale monga mkuyu* utaya *nkhuyu zake zosapsya, pamene iwo ugwedezeka ndi mphepo yamphamvu.*
>
> *Ndipo* miyamba *inakanganuka ngati mpukutu pamene* iwo *ukukulungidwa pamodzi; ndipo phiri lirilonse ndi chisumbu* chirichonse *zinasuntha kuchoka mmalo awo.*
>
> *Ndipo mafumu a dziko lapansi, ndi anthu aakulu, ndi anthu olemera, ndi akulu oyang'anira, ndi anthu amphamvu, ndi aliyense wansi- . . . ndi munthu wamfulu aliyense, anadzibisa okha mmapanga ndi mmatanthwe a mmapiri;*

113 Mwazindikira pamenepo? Tayang'anani pa iwo, "anthu amphamvu," mwaona. Kodi iwo anali atachita chiyani? "Iwo anali atalandira vinyo wa mkwiyo wa chiwerewere cha hule." Mukuona? Ndiro ndendende gulu lomwelo lomwe linamwa za vinyo wake. Mukuona?

> *Ndipo ananena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife kwa nkhope ya iye amene wakhala pa mpandowachifumu, ndi kwa mkwiyo wa Mwanawankhosa:*
>
> *Pakuti tsiku lalikulu la mkwiyo wake labwera; ndipo ndi ndani angakwanitse kuyima?*

114 Ndi malonje otani kwa . . . Mwaona, wokwerayo tsopano, zirombo za wokwerazo, ndi Zamoyo zoyankhazo, zafika pakutha. Kenako, ife tinatengedwera mmwamba, ife tinawona ofera pansi pa Mpandowachifumu. Tsopano ichi, kuchokera pa nthawi, ofera awa ndi Ayuda owona a Orthodox amene anafa mu chikhulupiriro Chachikhristu . . . kapena mu—mu chikhulupiriro chachipembedzo, chifukwa iwo sakanakhoza kukhala Akhristu.

115 Kumbukirani, Mulungu anachititsa khungu maso awo. Ndipo iwo akhala ali akhungu kwa nthawi yaitali, kufikira

Mpingo wa Amitundu utadzachotsedwa pa njirapo. Chifukwa, Mulungu samachita ndi anthu awiri awo pa nthawi imodzi, chifukwa izo nzosiyana kwambiri ndi Mawu Ake.

116 Kumbukirani, Iye amachita naye Israeli monga fuko, nthawizonse. Ndi fuko la Israeli.

117 Amitundu, monga munthu payekhapayekha, "anthu otengedwa kuchokera kwa Amitundu." Ndipo zinkayenera kutero, Amitundu, ankayenera kupanga . . . amapangidwa ndi anthu onse a mdziko, kotero tsopano ndiyeno pali Myuda amene akulowa mu chimenecho. Mukuona? Monga ngati—monga wa Chiluya, ndi wachi Irish, ndi Mmwenye, ndi ena otero, onsewo ndi anthu a mdziko, amene akupanga mpukutu wa maluwa uwu wa Mkwatibwi. Mukuona?

118 Koma, tsopano, pamene izo zifika pochita naye Israeli ndiye, mu gawo lotsiriza ili la sabata la chisevente, Iye akuchita nawo iwo ngati fuko, Amitundu atha. Oralo posachedwapa likufika, ndipo mwinamwake uno womwe—usiku womwe uno, kuti Mulungu atembenuka kwathunthu kuchoka kwa Amitundu, palimodzi. Ndendende! Iye ananena chomwecho. "Iwo adzapondereza pa makoma a Yerusalemu kufikira nyengo ya Amitundu itatsirizika, nthawizo zatha." Inde, bwana!

119 Ndipo zikadzatero, "Musiyeni iye amene ali woyipa akhalebe chiyipire; msiyeni iye amene ali wolungama akhalebe wolungama." Mukuona?

120 Palibenso Magazi pa mpando wa—wa—wa mmalo- . . . mmalo opatulika, nkomwe. Palibenso Magazi pa guwa. Nsembe yachotsedwapo, ndipo mulibenso kanthu koma utsi ndi mphezi ndi chiweruzo mmenemo. Ndipo ndicho ndendende basi chimene chikutsanuliridwa apa usikuuno. Mwaona, Mwanawankhosa wasiya kale . . . Ntchito yake ya umkhalapakati. Ntchito ya umkhalapakati yatsirizika, kuchokera pa Mpandowachifumu. Ndipo Nsembeyo, monga ife tamufanizitsira Iye mwangwiro, Muwomboli Wachibale, Mwanawankhosa wamagazi amene anabwera. Mwanawankhosa yemwe anali ataphedwa, Mmodzi wamagaziyo, ataphedwa, atatunduzidwa, anabwera ndi kudzatenga Bukhu kuchokera mdzanja Lake. Ndiko kuti, masiku atsirizika. Tsopano Iye akubwera kudzatenga zomwe Iye waziwombola. Ameni! Izo zimangotumiza chinachake kudutsa mwa ine!

121 Ife tikupeza tsopano kuti, Yohane anati, "Ine ndinawona pamene Iye anatsegula Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, kunali chivomezi chachikulu," ndiye chirengedwe chonse chinasokonezedwa. Mukuona?

122 Mulungu wakhala akuchita zinthu zazikulu, monga kuchiritsa odwala, ndi kutsegula maso a akhungu, ndi kuchita ntchito zazikulu.

123 Koma ife tikupeza, apa, kuti chirengedwe chinapunthwa, inde, chirengedwe chonse. Penyani chimene chinachitika, "Chi—chivomezi; dzuwa linada, ndipo mwezi sunakhoze kupereka kuwala kwake; ndipo nyenyezi zinagwedezeka ndipo zinagwa." Ndipo, bwanji, chirichonse chinachitika, mwaona, pa nthawi kumene ya kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi. Ndi pamene izo zikuchitika, mofulumira kumene kutatha kuchitika kulengeza kwa ofera awo, mwaona. Oferawo anali atatsirizika.

124 Tsopano inu mukuona ife tiri pafupi kumene kulowa mu ora limenelo tsopano. Ife tikhoza kutero, pa nthawi iliyonse, mwaona, chifukwa Mpingo uli chabe pafupi kukonzekera kutenga kuwuluka Kwake. Koma kumbukirani, pamene zinthu izi zizidzachitika, Mkwatibwi sadzakhala ali kuno. Ingokumbukirani, Mkwatibwi adzakhala atapita, Iye sadzasowa kudutsa mu chirichonse cha zimenezo. Iyi ndi nthawi ya Chisautso, ya kuyeretsedwa kwa a—kwa mpingo; zayikidwa pa iye, kuti iye adzadutse mu icho, osati Mkwatibwi. Iye akumutenga wokondedwa Wake kumuchotsa panjirapo. Inde, bwana! Iye, wamuwombola kale Iye. Mwaona, ziri ngati . . . Ndiko kusankha Kwa Iye Mwini, kusankha Kwake Komwe, monga mwamuna aliyense amamutengera mkwatibwi wake. Mukuona? Tsopano, chivomezi . . .

125 Tiyeni tifanizitse Malemba tsopano. Ine—ine ndikufuna . . . Kodi inu muli nayo pensulo ndi pepala? Ine ndikufuna kuti inu mundichitire ine chinachake. Pamene inu mukufuna kulemba, lembani izi, chifukwa, pokhapokha ngati inu muti mutenge tepiyi. Tsopano ife . . . Ine ndikufuna kuti inu muwerenge ndi ine, pamene inu mukutero.

126 Kufanizitsa Malemba a chochitika chachikulu ichi, kuti ife tiwone chobisika chachikulu ichi, kapena chinsinsi, chimene chinali pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi cha Bukhu la Chiwombolo. Tsopano kumbukirani, izi ndi zinsinsi zobisika. Ndipo Zisindikizo sikisi izi, zonse palimodzi, ndi Bukhu limodzi lalikulu, mipukutu sikisi basi itakulungidwa pamodzi, ndipo ichi chikufunyulula Bukhu lonse la Chiwombolo. Umo ndi momwe dziko lapansi lonse linawomboledwera.

127 Ndi chifukwa chake Yohane analira, chifukwa, ngati panalibe mmodzi aliyense amene akanakhoza kutenga Bukhu limenelo, chirengedwe chonse, chirichonse chikanakhala chitatayika. Icho chikanangobwerera mophweka ku—ku—ku ma atomu ndi mamolekyulu, ndi zina zotero, ndi kuwala kwa dziko, ndipo nkusakhalaponso ngakhale chirengedwe, munthu, popanda kalikonse. Chifukwa, Adamu anataya maufulu a Bukhu limenelo. Iye analilanditsa ilo pamene anamvetsera kwa mkazi wake, ndipo iye anamvetsera ku kulingalira kwa Satana, mmalo mwa Mawu a Mulungu. Mukuona? Ilo linalanditsidwa.

128 Ndiye, ilo silikanakhoza kubwerera m'manja mwakuda mwa Satana, amene anamuyesa iye nkumuchotsa pa njirapo, chotero choncho ilo linabwerera kwa mwini wake wapachiyambi, monga chikalata chaumwini chamtheradi chirichonse chikanachitira, mwaona. Linabwerera komwe kwa mwini wake wapachiyambi, ndipo ameneyo anali Mulungu, Mlengi, Yemwe analipanga ilo. Ndipo Iye akuligwirizira ilo.

129 Ndipo pali mtengo, ndipo ndiwo chiwombolo. Pamakhala mtengo winawake wa chiwombolo, ndipo panalibe aliyense akanakhoza kuchita chimenecho. Kotero, Iye anati, anapanga malamulo Ake, malamulo Ake Omwe a Muwomboli Wachibale. Ndiye, iwo sanakhoze kumpeza aliyense. Munthu aliyense anabadwa mwa kugonana, anabadwa mwa kukhumbirana kwa kugonana; iye anali mu tchimo lapachiyambi, Satana ndi Eva, kotero iye sakanakhoza kuchita chimenecho. Mulibe chirichonse mwa iye. Palibe papa woyera, wansembe, Dokotala Wauzimu, aliyense yemwe angakhale ali, iye sakanakhala woyenera. Ndipo iye sakanakhoza kukhala Mngelo, chifukwa iye ankayenera kukhala Wachibale. Iye ankayenera kukhala munthu.

130 Kenako Mulungu Mwiniwake anadzakhala Wachibale, povala thupi la munthu, kudzera mu kubadwa kwa namwali. Ndipo Iye anakhetsa Magazi Ake. Amenewo sanali magazi a Myuda. Awo sanali magazi a Wamitundu. Iwo anali Magazi a Mulungu. Mukuona? Baibulo linati, "Ife timapulumutsidwa kupyolera m'Magazi a Mulungu."

131 Mwana amatenga magazi a bambo ake. Ife tikuzidziwa zimenezo. Chirichonse mwa umuna chimatulutsa magazi amoyo. Kotero ife tikupeza kuti, monga thadzi kuyikira dzira; iyo ikhoza kuyikira dzira, koma ngati tambala, kapena wogona naye, sanakhale nalo ilo, ilo silimaswa. Limakhala lopanda chonde. Mkaziyo amangokhala chofungatira chimene chimanyamula dzira. Koma dziralo limabwera . . . Nyongolosiyo imachokera kwa champhongo.

132 Ndipo, mu nkhani iyi, champhongocho chinali Mulungu Mwiniwake. Umo ndi momwe ine ndikunenera, momwe kumwamba kuliri pansi, ndi—ndi momwe chachikulu chimakhalira chaching'ono. Mulungu anali wamkulu kwambiri mpaka Iye anadzakhala, ngakhale kudziwumba Yekha mu kanthu kakang'ono chotero, ku kanyongolosi kakang'ono kwambiri mu chiberekero cha namwali. Ndipo mozungulira iko Iye anayambitsa makhungu ndi Magazi. Ndipo anabadwa, ndi kuleredwa pa dziko lapansi. Ndipo kuchokera pa chiyambi cha mtundu umenewo, wosakhudzidwa, popanda chikhumbo chogonana kwa icho, nkomwe.

133 Ndipo kenako Iye anapereka Magazi amenewo, chifukwa Iye anadzakhala wachibale kwa ife. Ndipo Iye anali Muwomboli Wachibale. Ndipo Iye anakhetsa Magazi amenewo, mwaulere.

Iye sanasowe kutero. Iye anawapereka Iwo kwawulere, kuti awombole.

134 Kenako Iye anapita pa guwa la Mulungu, ndipo akuyembekezera pamenepo, pamene Mulungu akugwirizira Bukhu la Chiwombolo mmanja Mwake. Ndipo Mwanawankhosa wamagazi akuyima pa guwa la nsembe. Ndi ameneyo Mwanawankhosa, kuti apange chiwombolo, kupembedzera.

135 Ndiye, wina angayerekeze bwanji kunena kuti Maria, kapena Yosefe, kapena wachivundi wina aliyense, angakhoze kukhala—kukhala wopembedzera! Inu simungakhoze kupembedzera pokhapokha ngati pali Magazi pamenepo. Inde, bwana. "Alipo Mkhalapakati mmodzi pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo ndiye Khristu Yesu." Ndicho chimene Lemba limanena. Apo Iye akuyima, ndipo kufikira moyo wotsirizawo utawomboledwa; ndipo kenako Iye nkubwera kudzatenga zomwe Iye waziwombola. Oh, ndi—ndi Atate wamkulu bwanji Iye!

136 Tsopano kumbukirani, tsopano, ine nthawizonse ndakhala ndikuphunzitsa, kuti, "Mkamwa mwa mboni ziwiri kapena zitatu, mulole mawu aliwonse akhazikitsidwe." Ndipo, Lemba, basi monga ngati inu simungatenge Lemba limodzi ndi kutsimikizira kanthu pokhapokha patakhala chinachakenso choti chipite nalo ilo. Mukuona?

137 Mwaona, ine ndikhoza kutenga Lemba limodzi ndi kuti, "Yudasi anapita nakadzipachika yekha," kutenga lina ndi kuti, "Inu mupite mukachite chimodzimodzi." Mukuona? Koma, mwaona, icho sichingalumikizane ndi ena onse a Iwo.

138 Ndipo ine ndinaganiza, pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, pamene Mzimu Woyera unachimatula Icho pamenepo, ndipo nkuwona chimene icho chinali, ndiye ine ndinaganiza kuti icho chikanakhala chinthu chabwino kuti ndipereke kwa kalasi chinachake chosiyana pang'ono usikuuno. Mukuona? Chifukwa, izo zikhoza kukhala zotopetsa, pomangomvetsera kwa ine ndikuyankhula nthawi zonse, kotero ine ndinaganiza kuti ife tichite chinachake chosiyana.

139 Tsopano zindikirani. Chochitika chachikulu ichi chinasindikizidwa pansi pa Bukhu la chinsinsi, la chiwombolo. Tsopano Mwanawankhosa ali nalo Ilo mdzanja Lake, kuti alimatule Ilo.

140 Tsopano tiyeni tiyang'ane ku Mateyu mutu wa 24, Mwanawankhosa Mwiniwake akuyankhula. Tsopano, aliyense akudziwa kuti Khristu ndi Mlembi wa Bukhu lonse, monga momwe izo zikukhudzidwira. Koma uku ndi Kwake—kuyankhula Kwake apa, kapena Wake—Ulaliki wake kwa a—anthu, chabwino, kwa Ayuda.

141 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muligwire Bukhu lanu monga *chonchi*, Mateyu 24 ndi Chivumbulutso 6, monga *chonchi*.

[M'bale Branham wagwira Baibulo lake atatsegula pa mitu iwiri iyi—Mkonzi]. Ndipo tiyeni tifanizitse chinachake apa pang'ono pokha.

142 Tsopano, penyani ichi tsopano, ndipo inu mukhoza kuzipeza chabe momwe—momwe izo zikukhalira. Mwaona, chimene Mwanawankhosa *apa* akuwonetsa, ndendende mophiphiritsa, chimene Iye ananena *apa* mu Mawu. Kuchita ndendende, kotero kuti izo zikupanga icho kukhala cholondola. Tsopano, ndizo—ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo. Apa pali . . . *Apa* pali chimodzi, Iye akuyankhula za icho, ndipo *apa* ndi pamene icho chinachitika. Mukuona? Iko ndi kutsimikizira chabe kwangwiro.

143 Tsopano, tsopano tiyeni tiyang'ane pa mutu wa 24 wa Mateyu Woyera, ndi Chivumbulutso 6, ndipo tifanizitse ndi mutu wa 24 wa Mateyu. Ife tonse tikudziwa kuti umenewo unali mutu umene wophunzira aliyense, munthu aliyense amapitapo ku—kukayankhula za nthawi ya Chisautso. Izo zimachokera pa mutu wa 24 wa Mateyu. Ndipo tsopano tiyeni . . . Ngati izo ziri chomwecho, tsopano ife . . . Pakuti, ife tikudziwa kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi ndicho Chisindikizo Chachiweruzo. Ndi Chisindikizo Chachiweruzo, ndendende chomwe Icho chiri.

144 Tsopano, onani, ife takhala nako—kukwera kwa wotsutsakhristu. Tauwona Mpingo ukupita; tsopano Iwo watsirizika, wapita mmwamba. Kenako ife tinawona ofera, a Ayuda amenewo kumbuyo uko, pansi pa guwa. Tsopano apa pali kutsanuliridwa kwa chiweruzo, pa anthu amene ali . . .

145 Kuchokera mu chiweruzo cha Chisautso ichi mudzatuluka handiredi ndi forte-foro sauzande Ayuda owomboledwa. Ine nditsimikizira kwa inu kuti iwo ndi Ayuda, ndipo osati Amitundu. Iwo alibe chochita ndi Mkwatibwi, palibepo kanthu. Mkwatibwi, ife tamuwona kale Mkwatibwi kuti wapita. Inu simungachiyike icho pena paliponse; sakubwereranso mpaka pa mutu wa 19 wa Bukhu la chivumbulutso.

146 Tsopano zindikirani, pakuti, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chisindikizo chachiweruzo cha Mawu.

147 Tsopano, apa, tiyeni tiyambe tsopano ndipo tiyeni tiwerenge Mateyu Woyera, mutu wa 24. Tsopano ine ndikungofuna kukupatsani inu chinachake apa chimene ndangochiyang'ana, kuti ndichipeze. Tsopano, Mateyu Woyera, kuchokera pa 1 mpaka pa 3, chabwino, ndi pamene ife titi tiwerenge poyamba.

> *Ndipo Yesu anatuluka, nachoka ku kachisi: ndipo ophunzira ake anadza kwa iye kuti* adzamuwonetse *iye* chimango *cha kachisiyo.*
>
> *Ndipo* iye *ananena kwa iwo, Kodi inu simukuwona zinthu zonse izi? Indetu Ine ndinena kwa inu, Sipadzakhala* umodzi . . . *Kukhala utasiyidwa apa*

mwala umodzi pamwamba pa umzake, umene sudzagwetsedwa pansi.

Tsopano, *ndipo* (ndime ya 3) *pamene iye anakhala pa . . . phiri . . . la Azitona, ophunzirawo anabwera* kwa *iye mwapadera, nkudzati, Tiuzeni ife,* zinthu izi *zidzachitika liti? . . . chidzakhala chiyani chizindikiro cha kudza kwanu, ndi cha mathero a dziko lapansi?*

148 Tsopano tiyeni tiyime pamenepo. Ndime zitatu izi, izo zinachitika, kwenikweni, Lachiwiri masana, pa foro Epulo, A.D. 30. Ndipo ndime ziwiri zoyambirirazo zinachitika masana a . . . a Epulo pa foro, mu A.D. 30. Ndipo ndime yachitatuyo inachitika Lachiwiri madzulo wa tsiku lomwelo. Mukuona?

149 Iwo anabwera ku kachisi, ndipo iwo anadzamufunsa Iye zinthu izi. "Nanga bwanji *ichi*? Nanga bwanji *ichi*? Tayang'anani pa kachisi wamkulu uyu! Kodi iye si wodabwitsa?"

Iye anati, "Apo sipadzakhala mwala umodzi udzasiyidwe pa umzake."

150 Kenako Iye anapita pamwamba pa phiri ndi kukakhala pansi, mukuona. Kuti apo, apo Iye akuyamba; ndi masana. Ndiyeno pamene iwo anatero, iwo anamufunsa Iye pamwamba apo, anati, "Ife tikufuna kudziwa za zinthu zina."

151 Tsopano zindikirani, apa pali—apa pali mafunso atatu amene akufunsidwa ndi Ayuda, ophunzira Ake. Mafunso atatu akufunsidwa. Ndipo penyani. "Chiyani," loyamba, loyamba, "Chiyani . . . ? Zidzachitika liti zinthu izi, pamene, 'Sipadzakhala mwala umodzi pamwamba pa umzake'?" "Chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu?" funso lachiwiri. "Ndi cha kutha kwa dziko lapansi?" Mukuona zimenezo? Apo pali mafunso atatu.

152 Tsopano, apo ndi pamene anthu ambiri amapanga kulakwitsa kwawo. Iwo amaziyika zinthu izi apa kwa m'badwo wina ndiye, pamene, inu mukuona, Iye akuyankha mafunso atatu. Iwo . . .

153 Yang'anani tsopano momwe—momwe ziriri zokongola, ndime ya 3, onani, ganizo lotsirizalo pamenepo mu ndime ya 3. "Ndipo chidzakhala chiyani . . . ?" Poyamba, iwo anamuyitanira Iye ku phiri la Azitona apa, mwapadera. "Tiuzeni ife, zidzachitika liti zinthu izi?" funso loyamba. "Chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu?" funso lachiwiri. "Ndi cha matsiriziro a dziko lapansi?" funso lachitatu. Mukuona? Apo pali mafunso atatu osiyanasiyana amene anafunsidwa. Tsopano, tsopano ine ndikufuna kuti inu mutembenuze ndi kuyang'ana momwe Yesu apa akuwauzira iwo za zinthu izi.

154 Oh, ndi zokongola kwambiri! Ine . . . Zimangondipangitsa ine . . . Ine—ine—ine ndikupeza . . . Anali ati mawu aja omwe tinawagwiritsa ntchito usiku wina? [Osonkhana akuti,

"Kukondoweza."—Mkonzi]. Kukondoweza kochokera ku vumbulutso! Zindikirani.

155 Tsopano tiyeni titsegule tsopano ku Chisindikizo Choyamba cha—Zisindikizo za Bukhu ili, ndipo tifanizitse Chisindikizo Choyamba ichi ndi funso loyamba ili.

156 Ndipo funso lirilonse, kulifanizitsa ilo mpaka mmusi, ndi kuwona ngati sizikuyenda limodzi, basi monga momwe ife tinachitira mu zinthu zina zonse izi zikutseguka, kwa mibadwo ya mpingo ndi chirichonse, ndendende momwemo. Ndi chimenecho Chisindikizocho, kutsegulidwa mwangwiro, ndiye. Zindikirani, tsopano. Tsopano ife tiwerenga, poyamba, kwa . . . "Kenako Iye anawayankha iwo . . . " Ndipo—ndipo kenako Iye—Iye akuyamba kuwayankha tsopano, ndipo ife tikufuna kufanizitsa izo ndi Zisindikizo.

157 Tsopano penyani. Chisindikizo Choyamba chiri pa Chivumbulutso 6:1 ndi 2. Tsopano ife tiwerenge 6:1 ndi 2.

> *Ndipo—ndipo ine ndinawona . . . Mwanawankhosa* pamene iye *anatsegula chimodzi cha zisindikizo, ndipo ine ndinamva, ngati kuti* linali *phokoso la bingu, chimodzi cha zamoyo zinayi chikuti, Bwera ndipo udzawone.*
>
> *Ndipo ine ndinawona, ndipo taonani kavalo woyera: ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo uta; ndipo korona anapatsidwa kwa iye: ndipo iye anapita akugonjetsa, ndi kukagonjetsa.*

158 Munthu ameneyu tinampeza kut anali ndani? [Osonkhana akuti, " Wotsutsakhristu."—Mkonzi]. Wotsutsakhristu. Mateyu 24, tsopano, 4 ndi 5.

> *Ndipo Yesu anayankha ndipo anati kwa iwo—kwa iwo, Samalani kuti munthu asakunyengeni inu.*
>
> *Pakuti ambiri adzabwera mu dzina langa, nkumati, Ine ndine Khristu; ndipo adzanyenga ambiri.*

159 Mukuziwona zimenezo? Wotsutsakhristu. Ndi chimenecho Chisindikizo chanu. Mukuona? Mukuona? Iye anachiyankhula icho *apa*; ndipo apa *iwo* akutsegula Chisindikizo, ndipo apa iye anali, mwangwiro basi.

160 Tsopano Chisindikizo Chachiwiri, Mateyu 24:6, Chivumbulutso 6:3 ndi 4. Tsopano penyani, Mateyu 24:6. Tsopano ndiroleni ine ndiwone chimene iyo ikunena.

> *Ndipo inu mudzamva za nkhondo ndi mphekesera za nkhondo: onani kuti* inu *musakhale osawutsika: pakuti zinthu zonse izi ziyenera kuchitika, koma chitsiriziro sichinafikebe.*

161 Chabwino, tiyeni titenge Chisindikizo Chachiwiri, Chivumbulutso 6:3 ndi . . . Thuu. Penyani zomwe Iye akunena tsopano.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachiwiri, ndipo *ine ndinamva chamoyo chachiwiri chikuti, Bwera . . . udzawone.*

Ndipo pamenepo panapita *kavalo wina yemwe anali wofiira: ndipo mphamvu inapatsidwa* kwa *iye amene anakhala pamenepo kuti akachotse mtendere pa dziko lapansi, ndipo kuti iwo aziphana wina ndi mzake: ndipo kunapatsidwa* kwa *iye lupanga lalikulu.*

162 Mwangwiro, ndendende basi! Oh, ine ndimakonda kulipanga Lemba lizidziyankha Lokha. Kodi inu simutero? Mzimu Woyera unawalemba Iwo wonse, koma Iye ali wokhoza kuwaulula Iwo.

163 Tsopano tiyeni tizindikire Chisindikizo Chachitatu. Tsopano, iyi ndi njala. Tsopano, Mateyu 24:7 ndi 8. Tiyeni titenge 7 ndi 8, mu Mateyu.

Ndipo *fuko lidzawukira motsutsa fuko lina, ndi ufumu kutsutsa ufumu: ndipo kudzakhala njala, . . . miliri, . . . zivomezi, mmalo osiyanasiyana.*

Zinthu *zonsezi ndizo chiyambi cha* chisoni.

164 Mwaona, inu mukubwera mmwamba momwe tsopano. Tsopano, Chivumbulutso, mu wa 6, tsopano ife titsegula Chisindikizo Chachitatu. Icho chikupezeka mu Chivumbulutso 6:5 ndi 6.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachitatu, ine—ine ndinaona *chamoyo chachitatu chikuti, Bwera ndipo udzawone. Ndipo ine ndinawona, ndipo tawonani kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo masikero awiri mdzanja lake.*

Ndipo ndinamva liwu kuchokera mkati mwa zamoyo zinayizo likuti, *Muyezo . . . ndalama . . . Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama, ndi miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama; ndipo onetsetsa kuti usapweteke mafuta ndi . . . vinyo.*

165 Njala! Mwaona, ndendende Chisindikizo chomwecho, chinthu chomwecho chimene Yesu ananena. Chabwino.

166 Chisindikizo Chachinayi, "miliri" ndi "imfa." Zindikirani, Mateyu 24. Ife tiwerenga a—ndime ya 8, ya 7 ndi ya 8, ine ndikukhulupirira izo ziri, pa Chisindikizo Chachinayi ichi, ine ndiri nazo apa. Chabwino.

167 Tsopano, ndinawerenga chiyani pambuyo apa? Kodi ine ndinawerenga chinachake cholakwika? Eya, ine ndachilemba icho. Eya, apo ife tiri. Tsopano ife tikupita. Tsopano ife tipite. Chabwino, bwana.

168 Tsopano tiyeni tiyambire apa pa ya 7, pa ichi, Chisindikizo Chachinayi; ndi pa 6:7 ndi 8, pa chimodzi chinacho, pa Chivumbulutso.

169 Tsopano tiyeni tiwone ya 7 ndi ya 8 ya Mateyu 24. Chabwino, tsopano.

> Ndipo *fuko lidzawukira motsutsa fuko limzake, ndi ufumu kutsutsana ndi ufumu umzake: ndipo kudzakhala njala,. . .miliri,. . .zivomezi, mmalo osiyanasiyana.*
>
> Zinthu *zonsezi ndizo chiyambi cha* chisoni.

170 Tsopano Chisindikizo Chachinayi, pamene ife tikuwerenga icho cha apa, chinali. . .Chisindikizo Chachinayi, chinali kuyambira pa ya 7 ndi ya 8, pa china ichi tsopano.

> *Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachinayi,* ndipo taonani. . .*chamoyo chachinayi* chinati, *Bwera ndipo udzawone.*
>
> *Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo taonani kavalo wotumbululuka:. . .*

171 Tsopano dikirani. Ine ndinalemba izi molakwitsa. Eya. Eya. Tsopano miniti yokha, tsopano, 7 ndi 8.

172 Tsopano tiyeni tiwone, Mateyu 24:7 ndi 8. Tsopano tiyeni tiwone. Ife tizipeza izo. Ndicho Chachitatu, chikutseguka, sichoncho icho? Mateyu 24:7 ndi 8. Ine ndikupepesa. Tsopano, icho chikutsegula mvula, kapena, njala, chikutsegula njala. Chabwino.

173 Tsopano, "miliri" ndi "imfa." Inde, bwana. Tsopano ife tikupita kwa icho, 7 ndi 8. Tsopano, icho chingakhale Chisindikizo Chachinayi. Tiyeni tiwone pamene ife tinapeza Chisindikizo Chachinayi. "Ndipo pamene iye anatsegula Chachinayi—Chisindikizo Chachinayi. . ." Eya, ndi wokwera pa kavalo wotumbululuka, "Imfa," mwaona.

> *Ndipo—ndipo ine ndinayang'ana, ndipo taonani kavalo wotumbululuka: ndipo* iye. . .*kavalo wotumbululuka: ndipo dzina la amene anakhala pa iye* linkatchedwa *Imfa, ndipo Gehena inatsatira. . .iye. Ndipo mphamvu inapatsidwa kwa* iye *pa* zigawo-. . . zigawo zinayi *za dziko lapansi, kuti akaphe ndi lupanga, ndi njala, ndi imfa, ndi zinyama za mdziko lapansi.*

174 Tsopano, mwaona, imeneyo inali "Imfa."

175 Tsopano, Chisindikizo Chachisanu, Mateyu 24:9-13. Tiyeni tiwone ngati ndapeza izi molondola, tsopano, kachiwiri. Mukuona?

> Ndipo *kenako iwo adzakuperekani inu kuti mukazunzidwe, ndipo adzakuphani inu* (ndi zimenezotu): *ndipo inu mudzadedwa ndi mafuko onse chifukwa cha dzina langa.* Ndipo pamene. . .

Ndipo kenako ambiri adzakuperekani. . . ambiri *adzakhumudwa, ndipo adzaperekana wina ndi mzake, ndipo adzadana wina ndi mzake.*

Ndipo aneneri abodza ambiri adzawuka, ndipo. . . adzanyenga ambiri.

Ndipo chifukwa kusaweruzika kudzachuluka, chikondi cha ambiri chidzazirala.

Koma iye amene. . . adzapirira mpaka kumapeto, yemweyo adzapulumutsidwa.

176 Tsopano, ife tiri pa Chisindikizo Chachisanu tsopano. Ndipo icho chinali usiku wathawu, mwaona. "Iwo adzakuperekani inu, kuperekana wina ndi mzake," ndi zina zotero.

177 Tsopano penyani apa pa ya 6, Chisindikizo, 6:9 mpaka 11. Tsopano tiyeni tipeze chimenecho, Chivumbulutso 6:9 mpaka 11.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansi pa guwa la nsembe miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anawugwira:

Ndipo iwo anafuula ndi mawu aakulu, kunena, Mpakana liti,. . . Ambuye, woyera. . . woona, muti inu. . . mukaweruze ndi kukatibwezerera magazi athu pa iwo akukhala pa dziko lapansi?

Tsopano, *ndipo mikanjo yoyera inapatsidwa* kwa *aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti iwo apumulebe kwa kanthawi pang'ono, mpaka antchito amzawo nawonso ndi abale awo,. . . kuti aphedwe monga iwo anachitira, zikwaniritsidwe.*

178 Tsopano, mukuona, pansi pa Chisindikizo Chachisanu, ife tikupeza—ife tikupeza apa kufera.

179 Ndipo pansi pa 24:9 cha apa, ife. . . mpaka 13, ife tikupeza aponso kuti anali wofera. "Iwo adzakuperekani inu, ndi kudzakuphani inu," ndi zina zotero. Mwaona, Chisindikizo chomwecho chikutsegulidwa.

180 Tsopano, mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, ndi chomwe ife tikubwerako tsopano, Mateyu 24:29 ndi 30. 24, ndipo tiyeni titenge 29 ndi—ndi 30. Apa ife tiri.

Tsopano, tsopano ife titenga, aponso, Chivumbulutso 6:12 mpaka 17.

181 Ndizo ndendende zomwe ife tangowerenga kumene. Tsopano mvetserani kwa ichi, tsopano, chimene Yesu ananena mu Mateyu. . . :29, 24:29 ndi 30.

Mwamsanga chitatha chisautso cha masiku amenewo. . .

182 Chiyani? Pamene chi . . . chisautso ichi, chisautso chaching'ono ichi chimene iwo adutsamo apa, mwaona.

> *. . . dzuwa lidzadetsedwa, ndipo mwezi sudzapereka kuwala kwake, ndi nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndipo zimphamvu za . . . mmiyamba zidzagwedezeka:*
>
> *Ndipo kenako chidzawonekera chizindikiro cha Mwana wa munthu mmwamba: ndiyeno mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzalira, ndipo iwo adzamuwona Mwana wa munthu akubwera mmitambo ya mmwamba ndi mphamvu ndi ulemelero waukulu.*

183 Tsopano, werengani cha apa mu Chivumbulutso tsopano, chi—Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, chimene ife tiripo tsopano.

> *Ndipo . . .* taonani *pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, ndipo, taonani, kunali chivomezi chachikulu; ndipo dzuwa linada ngati chiguduli* (mukuona?) *cha ubweya, ndipo mwezi unasanduka magazi;*
>
> *Ndipo nyenyezi za kumwamba zinagwera padziko lapansi, ngakhale monga mkuyu* utaya *nkhuyu zake zosacha, pamene iwo . . . wagwedezeka ndi mphepo yamphamvu.*
>
> *Ndipo* miyamba *inakanganuka monga mpukutu pamene iwo ukulungidwa pamodzi; ndipo phiri lirilonse ndi chisumbu* chirichonse . . . *zinasuntha kuchoka* mmalo *mwake.*
>
> *Ndipo mafumu a dziko lapansi, ndi anthu opambana, ndi anthu olemera, ndi akazembe aakulu, ndi anthu amphamvu, ndi munthu* wamsinga *aliyense, . . . munthu wa ufulu aliyense, anadzibisa okha mu mapanga . . . mmatanthwe a* phiri;
>
> *Ndipo ananena* kwa *mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya iye* amene wakhala *pa mpandowachifumu, ndi ku mkwiyo—mkwiyo wa Mwanawankhosa:*
>
> *Pakuti tsiku lalikulu la mkwiyo wake lafika; . . . ndani angakhoze kuyima?*

184 Mwangwiro basi, bwererani mmbuyo momwe, onani chimene Yesu ananena apa tsopano mu Mateyu 24:29. Mvetserani. "Zitatha," zochitika za Eichmann izi, ndi zina zotero.

> *Mwamsanga chitatha kuchitika chisautso cha mmasiku amenewo dzuwa lidzadetsedwa, . . . mwezi sudzatero—sudzapereka kuwala kwake, . . . nyenyezi*

zidzagwa kuchokera kumwamba,. . .zimphamvu za. . . kumwamba *zidzagwedezeka:*

Tsopano penyani.

Ndiye kenako chidzawonekera chizindikiro cha Mwana wa munthu mmwamba: ndipo iwo adzawona, ndipo iwo. . .*ndiyeno mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzalira, ndipo iwo adzamuwona Mwana wa munthu akubwera mmitambo ya kumwamba ndi* mphamvu yaikulu ndi *ulemelero*.

Ndipo. . .adzatumiza angelo ake, ndi zina zotero, ndipo *ndi. . .ndi liwu la lipenga, ndipo. . . adzawasonkhanitsa* iwo *pamodzi. . .mphepo zinayi,. . .* zinalimbana pamodzi.

185 Mwaona, ndendende basi, kufanizitsa zimene Yesu ananena mu Mateyu 24, ndi chimene mvumbulutsiyu apa anatsegula mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, ndizo ndendende basi. Ndipo Yesu anali kuyankhula za nthawi ya Chisautso. Mukuona?

186 Poyamba, iye anafunsa nthawi yomwe zinthu izi zikanati zidzachitike, pamene kachisi akanati adzachotsedwepo. Iye anayankha ilo. Chinthu chotsatira iye anafunsa, za nthawi imene ikanadzafika. . .Apo panabwera m'badwo wa ofera. Ndi nthawi imene *izi* zikanati zidzachitike, pamene wotsutsakhristu akanadzawuka; ndi pamene wotsutsakhristu akanati adzachotsepo kachisiyo.

187 Daniele, momwe ife tikanakhozera kupita mmbuyo ndi kukamutenga Daniele kumeneko, pamene iye ananena zimenezo, kalonga uyu amene akanadzabwera. Inu owerenga mukudziwa zimenezo. Ndipo iye akanadzachita chiyani? Iye akanadzachotsa nsembe za tsiku ndi tsiku, ndi zonse zomwe zikanadzachitika pa nthawiyo. Anati. . .

188 Yesu, ngakhale, kuyankhula za izo apa, anatsimikizira zimenezo. Anati, "Pamene inu mudzawona choyipa chopanga chipasuko, choyankhulidwa ndi mneneri Daniele, chikuyima mmalo oyera." Ndi chiyani chimenecho? Mzikiti wa Omar, unayima mmalo a kachisi pamene iwo anamuwotcha iye. Anati, "Aloleni iwo amene ali mmapiri. . .Aloleni iwo amene ali pa denga la nyumba, asabwere pansi kudzatenga zinthu m'nyumba, kapena iye amene ali mmunda asabwererenso. Pakuti kudzakhala nthawi ya mavuto!" Inu mukuona? Ndipo zinthu zonse izi zikanadzachitika, tinazisuntha izo mpaka mmusi tsopano ndi kutsimikizira izo, kubwerera ku kutsegula uku kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

189 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire. Yesu. . . Tsopano, za mawa usiku, pa Ichi, Yesu analumpha kuphunzitsa kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Icho sichiri apa. Penyani, Iye akupitirira ndi mafanizo tsopano, zitatha zimenezo. Ndipo Yohane analumpha Chisindikizo Chachisanu Ndi

Chiwiri. Chachisanu Ndi Chiwiri, chotsiriza, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, icho chidzakhala chinthu chachikulu. Icho sichinalembedwe nkomwe, mwaona. Analumpha Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri; onse a iwo anatero. Ndipo mvumbulutsiyu, pamene Mulungu anangoti apo panali . . . Yohane anati, "Kunangokhala chete Kumwamba." Yesu sananene liwu lokhudza Icho.

190 Zindikirani tsopano, kubwerera ku ndime ya 12, zindikirani, palibe Chamoyo. Ndiyo ndime ya 12, kuyambira pa Chisindikizo chathu, kuti tichiwone icho chitatsegulidwa. Palibe Chamoyo, chonga, Zolengedwa zamoyo, zikuimiridwa apa, nkomwe, monga zinakhalira pa Chisindikizo Chachisanu. Chifukwa chiyani? Izi zinachitika, ku mbali ina ya m'badwo wa Uthenga, mu nthawi ya Chisautso. Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi ndi nthawi ya Chisautso. Ndicho chimene chikuchitika. Mkwatibwi wapita. Mukuona? Apo palibe cholengedwa Chamoyo kapena chinthu pamenepo kuti chinene izo. Pali basi . . . Tsopano, Mulungu sakuchitanso ndi Mpingo nkomwe; Iwo wapita.

191 Iye akuchita ndi Israeli, mwaona. Mwaona, iyi ndi mbali inayo, apa ndi pamene Israeli analandira Uthenga wa ufumu, mwa aneneri awiri a Chivumbulutso 11. Kumbukirani, Israeli ndi fuko, wantchito wa Mulungu, fuko. Ndipo pamene—pamene—pamene Israeli adzabweretsedwa mkati, icho chidzakhala—chochitika cha fuko.

192 Israeli, m'badwo wa ufumu, ndiko kumene Davide . . . Mwana wa Davide, akukhala pa mpandowachifumu. Ndi chifukwa chake mkazi uja anafuula, "Inu Mwana wa Davide!" Ndipo Davide ndi kwa . . . Mwana wa Davide! Mulungu analumbira pa Iye, kwa Davide, kuti Iye adzawutsa Mwana Wake yemwe ati adzatenge mpandowachifumu wake. Iwo ukanadzakhala mpandowachifumu wa nthawizonse. Mukuona? Iwo sukanadzakhala ndi mapeto. Solomoni anawupereka iwo, mwa choyimira, mu kachisi. Ndipo Yesu anangowauza iwo apa, ndicho, "Apo sipadzakhala mwala wotsalira pamwamba pa umodzi wa iyo." Koma Iye akuyesetsa kuwauza iwo apa, chimene . . . Iye akubwereranso.

"Kodi Inu mudzabweranso liti?"

193 "Zinthu izi zidzachitika Ine ndisanabwerere." Ndipo apa izo ziri!

Tsopano ife tiri pa nthawi ya Chisautso.

Kumbukirani, pamene ufumuwo udzakhazikitsidwa, pa dziko lapansi . . .

194 Tsopano, ichi chikhoza kukhala chodzidzimutsa pang'ono. Ndipo ngati pali funso, ndipo inu—mukhoza kundifunsabe ine; ngati mukufuna kuti muyike funsolo, izo zitatha

kutchulidwa kale, ndipo kungozigunda izo; ngati simunatero, inu simumazidziwa kale izo.

195 Mu nthawi ya Zakachikwi, ndi Israeli amene ali fuko, mafuko thwelovu monga fuko.

196 Koma Mkwatibwi ali mnyumba yachifumu. Iye ndi Mfumukazi tsopano. Iye wakwatiwa. Ndipo onse a mdziko lapansi adzabwera mu mzinda uwu, Yerusalemu, ndipo adzabweretsa ulemelero wa iwo mmenemo. "Ndipo zipata sizimadzatsekedwa, u—u—usiku, chifukwa uko sikudzakhala konse usiku." Mukuona? Zipata zizidzakhala zotsegulidwa nthawizonse. "Ndipo mafumu a dziko lapansi," Chivumbulutso . . .:22, "azidzabweretsa ulemu ndi ulemelero wawo mu mzinda uwu." Koma Mkwatibwi adzakhala ali mmenemo ndi Mwanawankhosa. Oh, mai! Inu mukhoza kuziwona zimenezo, mmenemo! Osati . . . Mkwatibwi sadzakhala ali kunja kuno akugwira ntchito mminda ya mpesa. Ayi, bwana. Iye ndi Mkwatibwi. Iye ndi Mfumukazi kwa Mfumu. Ndi enawo amene azidzagwira ntchito kunjako, fukolo, osati Mkwatibwi. Ameni. Chabwino.

197 Zindikirani atumiki awa tsopano, atumiki awa a Chivumbulutso . . .:12, aneneri awiri awa, iwo akalalikira, "Ufumu wayandikira!" Mukuona? Ufumu wa Kumwamba uli woti udzakhazikitsidwe. Nthawi, zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata la chisevente la Daniele, zinalonjezedwa kwa Ayuda, anthu ake. Kumbukirani tsopano, kuti, kuti titsimikizire zimenezo, kuti ili ndi gawo lotsiriza la sabata la chisevente la Daniele. Ine ndiri nalo funso pa izo la mawa. Mukuona?

198 Tsopano, masabata sevente analonjezedwa, zimene zinali zaka seveni. Ndipo mkati mwa masabata seventewo, Mesiya anali woti adzadulidwa, kuti adzapangidwe nsembe. Iye akanadzanenera kwa zaka zitatu ndi theka, ndipo kenako iye akanadzadulidwa, kuti apangidwe nsembe kwa anthu. Ndipo apo pakadali kutsimikizira, kuti zaka zitatu ndi theka zikadali zotsimikizika kwa Israeli. Ndiye, pamene Mesiya anadulidwa, Myuda anachititsidwa khungu kuchitira kuti iye asakhoze kuwona kuti uyo anali Mesiya.

199 Ndipo, kenako, pamene Mesiya anadzadulidwa, ndiye Uthenga ndi m'badwo wa chisomo zinabwera kwa Amitundu. Ndipo iwo anabwera kumeneko, ndipo Mulungu anakokera mmodzi kuchokera *apa* ndi *apo*, ndi *apa* ndi *apo*, ndi kudzawaika iwo pambali pansi pa atumikiwo; ndi *apa* ndi *apo*, ndi *apa* ndi *apo*, ndi kudzawayika iwo pambali pansi pa atumikiwo.

200 Ndipo Iye anatumiza mtumiki woyamba, ndipo iye analalikira, ndipo lipenga linawomba; monga ife titi tidzazitengere izo, pakapita kanthawi. Ndipo, kenako, lipenga linali kulengeza nkhondo. Lipenga nthawizonse limanena za nkhondo. Mtumikiyo, mngeloyo amabwera pa dziko lapansi,

mtumiki wa ora, monga Luther, monga aliyense wa atumiki omwe ife tinawakamba. Iye amachita chiyani? Iye amafika; ndipo Chisindikizo chimatsegulidwa, kuwululidwa; lipenga limawomba, nkhondo imalengezedwa, ndipo kutali iwo amapita. Ndipo kenako mtumikiyo amamwalira. Iye amalisindikiza gulu ili; iwo amayikidwa mkati. Ndipo mliri umagwa pa iwo amene anawukana Iwo. Mukuona?

201 Ndiye zimapitirira, kenako iwo amapanga bungwe, kupanga bungwe lina. Ife tangodutsamo kumene mu zimenezo. Ndiye, apa iwo amatulukira ndi mphamvu ina, mwaona, mphamvu ina, m'badwo wina wa mpingo, utumiki wina. Ndiye, pamene iye achita zimenezo, motsatira pamabwera Mulungu ndi utumiki Wake, pamene wotsutsakhristu abwera ndi wake. Mwaona, *anti* ndi "kutsutsa." Iwo amayenda mbali ndi mbali.

202 Ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinachake chaching'ono. Pafupifupi nthawi yomwe—yomwe Kaini anabwera pa dziko lapansi, Abele anabwera pa dziko lapansi. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire, Pafupifupi nthawi yomwe—yomwe Khristu anabwera pa dziko lapansi, Yudasi anabweranso pa dziko lapansi. Pafupifupi nthawi imene Khristu anachoka pa dziko lapansi, Yudasi anadzachoka pa dziko lapansi. Basi nthawi yomwe—Mzimu Woyera unagwa, mzimu wotsutsakhristu unagwa. Basi nthawi yomwe Mzimu Woyera ukudziwulula Wokha kuno mmasiku otsiriza, wotsutsakhristu akuwonetsera mawanga ake, akubwera kudutsa mu ndale zake ndi zinthu. Ndipo basi pafupifupi nthawi yomwe wotsutsakhristu akudzisunthira yekha kwathunthu pa mse-. . . powonekera; Mulungu akudzisunthira Yekha kwathunthu pamenepo, kuti adzawombole izo zonse. Mwaona, zimangoyenda basi, zimangoyenda limodzi basi. Ndipo izo ndizo, ziwiri zonse, mbali ndi mbali. Kaini ndi Abele! Khwangwala ndi nkhunda, mchombo! Yudasi ndi Yesu! Ndipo basi mpaka mmusi, inu mukhoza kuchitenga icho. Basi . . .

203 Apa panali Moabu ndi Israeli; awiri onse amenewo. Moabu silinali fuko lachikunja. Ayi, bwana. Iwo ankapereka nsembe yomweyo yomwe Israeli anali kupereka. Iwo ankapemphera kwa Mulungu yemweyo. Chimodzimodzi. Moabu anali kutchedwa-. . . Anali mmodzi wa ana aakazi a Loti yemwe anagonana ndi abambo ake, ndipo anabereka mwana. Ndipo mwana ameneyo anatchedwa Moabu. Ndipo kuchokera mwa iye munatuluka mtundu wa Moabu, dziko la Moabu.

Ndipo pamene iwo anamuwona Israeli, m'bale wawo woomboledwa, akubwera.

204 Iwo anali achikhazikitso. Iwo anali chipembedzo chachikulu. Israeli analibe chipembedzo; iye ankangokhala mmahema ndi kulikonse kumene inu mukupita. Koma Moabu anali nawo olemekezeka, mafumu, ndi zina zotero. Ndipo iwo

anali ndi Balaamu kumeneko, a—mneneri wabodza. Ndipo iwo anali nazo zonse izi. Ndiye iwo anabwera kumusi uko kukamutemberera m'bale wawo wamng'ono yemwe anali pa ulendo wopita ku dziko lolonjezedwa, akupita ku lonjezo lake.

205 Ndipo iye anapita ndi kukawafunsa iwo, "Kodi ine ndingadutse nawo mdziko lanu? Ngati ng'ombe zanga zimwa madzi, ine ndidzalipira izo. Ngati izo zinyambita udzu, ife tidzalipira izo."

206 Iye anati, "Ayi. Inu simukhala nacho chitsitsimutso chonga chimenecho kozungulira kuno. Uko nkulondola. Inu simukhala nacho chirichonse chonga icho kozungulira kuno."

207 Ndiyeno penyani chimene iye anachita. Iye anabwerera mmbuyo kumene mmawonekedwe a Yezebeli, ndipo anabwera pansi kudzera mwa mneneri wabodza ameneyo, ndi kudzawapangitsa ana a Mulungu kulakwa. Ndipo anawakwatira akazi Achimoabu kuwalowetsa—kuwalowetsa mu Israeli, ndi kudzapangitsa chigololo.

208 Ndipo iye anachita chinthu chomwecho, mu m'badwo womwewo, pa ulendo, pa ulendo wopita ku Dziko lolonjezedwa, umene ife tirimo. Kodi iye anachita chiyani? Mneneri wabodzayo anabwera pamenepo ndipo anadzakwatira, ndipo anaitanira mu mpingo wa Chiprotestanti, ndipo anayambitsa zipembedzo, ndendende basi zomwe iwo anachita kumbuyo uko.

209 Koma Israeli wamng'ono wakale anasunthabe chitsogolo, chimodzimodzi. Iye anazungulira mchipululu kwa nthawi yayitali, ndipo onse omenyera akale aja anayenera kufa, koma iye anapitirirabe mpaka ku dziko lolonjezedwa. Eya. Inde. Penyani iwo onse akugwirana mikono, basi iwo asanawoloke Yordani. Ha-ha! Ine ndikuzikonda zimenezo. Tsopano ife tikufika ku m'badwo umenewo pakali pano, apa tsopano. Zindikirani.

210 Tsopano ife tikupeza, kuti, nthawi, yotsiriza (ine ndinati) zaka zitatu ndi theka za masabata sevente a Daniele.

211 Ndiroleni ine ndifotokoze zimenezo momveka pang'ono tsopano, chifukwa ine ndikumuwona winawake pano yemwe nthawizonse wakhala akupenyerera izo, ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndiyesetse kuzipanga ndekha kumveka; mphunzitsi.

212 Zindikirani pamene masabata sevente akubwera. Pamene Daniele anawona masomphenya a nthawi ikubwera, ndi kutsirizika kwa Ayuda, koma iye ananena pamenepo panatsimikizika masabata sevente. Ndizo zaka seveni; mkati mwa izo, bwanji, Mesiya akanadzakhala kuno, kapena, ndipo akanadzadulidwa, chifukwa cha nsembe. Tsopano, ndicho ndendende chimene chinachitika.

213 Kenako, Mulungu anachita ndi Amitundu mpaka iwo atatengako anthu kwa Dzina Lake. Mwamsanga pamene Mpingo wa Amitundu ukutengedwa, Iye anawutengera mmwamba Mpingo.

214 Ndipo pamene Iye anatero, namwali wogona, mpingo iwoeni . . . Mkwatibwi anapita mmwamba. Ndipo mpingo iwoeni unayikidwa "ku mdima wakunja, kumene kunali kulira, ndi kubuula, ndi kukukuta kwa mano." Mu nthawi yomweyo, Chisautso chikugwa pa anthu amenewo.

215 Ndipo pamene Chisautso chikugwa, mmenemo mukubwera aneneri awiri awa a Chivumbulutso 11, kudzalalikira Uthenga kwa iwo. Ndipo iwo akulalikira kwa sauzande, wani handiredi . . . ndi masiku sikisite. Mukuona? Chabwino, ndizo ndendende, ndi masiku sarte mu mwezi monga kalendala yeniyeni ili nawo, ndizo ndendende zaka zitatu ndi theka. Ndiro gawo la chisevente la Daniele, gawo lotsiriza la sabata la chisevente. Mukuona?

Mulungu sanachite ndi Israeli mkati umu. Ayi, bwana.

216 M'bale anandifunsa ine, osati kale kwambiri, anati, "Kodi ndiyenera kupita . . ." A—m'bale kuno mu tchalitchi, m'bale wofunika, wokondedwa, anati, "Ine—ine ndikufuna kupita ku Israeli. Ine ndikukhulupirira kuti kumeneko kukakhala kutsitsimuka."

217 Winawake ananena kwa ine, "M'bale Branham, inu muyenera kupita ku Israeli pakali pano. Iwo akachiwona icho." Mwaona, inu simungakhoze kuchita zimenezo.

Ine ndinaima pamenepo, ndipo ndinaganiza . . .

218 Ayuda amenewo akati, "Ngati ine . . . Chabwino, ngati uyu ali, Yesu ali—ndi Mesiya," akati, "mundilole ine ndimuwone Iye akuchita chizindikiro cha mneneri. Ife timakhulupirira aneneri athu, chifukwa ndicho chimene iwo ali—iwo akuyenera kukhala."

219 "Ndi kachikhazikitso bwanji," ine ndinaganiza. "Apa ine ndikupita!" Pamene ine ndinafika uko komwe, pafupi kumene ndi kumeneko, kulondola . . . Ine ndinali, chabwino, ine ndinali ku Cairo. Ndipo ndinali ndi tikiti yanga mdzanja langa, yopitira ku Israeli. Ndipo ndinati, "Ine, ine ndipita, ndikawona ngati iwo akafunse izo, ngati iwo angakakhoze kuwona chizindikiro cha mneneri. Ife tikawona ngati iwo ati akamulandire Khristu."

220 Lewi Pethrus, wa mpingo wa ku Stockholm, anawatumizira iwo ma Baibulo millioni.

221 Ndipo Ayuda awo akubwera kumeneko! Inu mwachiwonapo chithunzicho. Ine ndiri nacho icho pa filimu, kumbuyo komwe kuno tsopano, *Maminiti Atatu Isanakwane Pakati Pa Usiku.* Ndipo Ayuda amenewo akubwera mmenemo, kuchokera konse konse mdziko, kulikonseko, anayamba kusonkhana kumeneko.

222 England atatha kupita kale kumeneko, mu nthawi ya General Allenby, mu *Kutha Kwa Nkhondo Yadziko Lonse,* mu bukhu lachiwiri, ine ndikuganiza ndi limenelo, ndipo iwo anagonja, ma Turks anagonja, kenako iye analibwezera ilo kwa Israeli. Ndipo iye wakhala akukula monga fuko, ndipo tsopano iye ndi fuko langwiro: ndalama zakezake, ndalama, mbendera, ankhondo, ndi china chirichonse. Mukuona?

223 Ndipo Ayuda awa, akubwereranso ku dziko la kwawo, iwo anali . . . Chinthu choyamba, pamene iwo anapita mpaka mu Iran, ndi kumusi uko, kukawatenga iwo, iwo anafunsa . . . Iwo anati . . . iye anati . . . Iwo akufuna kuwatenga iwo kubwerera ku Israeli, kukawapatsa iwo malo awo; kuwatengera iwo kubwerera mdziko lawo, Palestina, kumene iwo akuyenera kukakhala ali.

224 Ndipo, kumbukirani, malingana ngati Israeli ali kunja kwa dziko limenelo, iye ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu; monga Abrahamu, kwa yemwe ilo linapatsidwa. Ndipo pamene . . .

225 Iwo sakanakwera mu ndege imeneyo. Iwo anali asanawonepo chirichonse chonga chimenecho. Apo panali rabbi wachikulire amene anabwera pamenepo, anati, "Mneneri wathu anatiuza ife, kuti, pamene Israeli azidzapita kwawo, iye akanadzapita 'pa mapiko a mphungu,'" pa ndege, kupita kwawo.

226 Ndi ameneyo uko tsopano, akumanga. Mtengo wa mkuyu ukubwezeretsedwa! Ameni! Mbendera yakale ya nyenyezi ya nsonga sikisi ya Davide ikuwuluka!

227 "Masiku a Amitundu akwanira, zovuta zikuchuluka!" Nthawi ya Chisautso yayandikira kumene!

228 Ndipo ndaimirira pomwe pano, ndipo Zisindikizo zikutsegulidwa, Mpingo wakonzekera kuti utenge kuwuluka Kwake kupita mu mlengalenga!

229 Ndipo Chisautso chikuyambika, kenako Mulungu akubwera pansi ndi kudzasolola handiredi ndi forte-foro sauzande kuchokera kumeneko. Ameni! Kumeneko, oh, ndi zangwiro! Inu mukuona pamene Zisindikizo zikuzitulutsira izo tsopano, mwaona, kuzitsegula izo? Tsopano, izi ndi zaka zitatu ndi theka zotsiriza kwa anthu. Ndiponso, ngati inu mungazindikire, ndi nthawi yomwe Mulungu ati adzayitane Ayuda handiredi ndi forte-foro sauzande, mu zaka zitatu izi ndi theka-limodzi.

230 Mwaona, Iye sanachitenso ndi iwo, nkomwe. Iwo sanakhale naye mneneri. Iwo sangakhulupirire kanthu kalikonse koma mneneri. Inu simungawapusitse iwo. Kotero, iwo adzamumva mneneri, inde, bwana, ndipo ndizo zonse. Kuti, Mulungu anawauza iwo izo pachiyambi, ndipo iwo amakhala nachobe icho.

231 Iye anati, "Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa Mneneri pakati panu, wonga ine." Mose ananena zimenezo. Ndipo anati,

"Iyeyo inu mudzamumvere. Ndipo yense amene sadzamumvera Mneneri ameneyo, adzadulidwa kuchoka kwa anthu." Uko nkulondola.

232 Ndipo, inu mukuona, maso awo ankayenera kuchititsidwa khungu, apo ayi iwo akanamuzindikira Iye. Mmalo mwa icho, pochititsidwa khungu, iwo anali. . . Icho chinamulola Satana kufika pa iwo, ndipo iwo anati, "Iye ndi wam'bwebwe, Belezebule. Mulole magazi ake akhale pa ife. Ife tikudziwa kuti palibe kanthu kwa Iye." Mukuona?

233 Ndipo anthu osaukawo anachititsidwa khungu. Ndi chifukwa chake gulu la Eichmann ndi gulu lonse ilo linaphedwa kumbuyo uko. Anali nawo ufulu wobwera mmenemo; Atate awo omwe anachita kuwachititsa khungu maso awo kuchitira kuti Iye akakhoze kutitenga ife.

234 Ndicho chinthu chomvetsa chisoni kwambiri m'Malemba, pafupifupi. Tangoganizani za kumeneko, Ayuda, akuyitanitsa Magazi a Atate awo omwe, Mulungu wawo yemwe atapachikidwa pamenepo, akuwukha magazi. Penyani, "Kumeneko iwo anampachika Iye," Baibulo linatero. Ndiwo foro a mawu aakulu kwambiri. Taonani. "Kumeneko," Yerusalemu, mzinda woyera kwambiri mdziko lapansi. "Iwo," anthu oyera kwambiri mdziko lapansi. "Anampachika," imfa yankhanza kwambiri padziko lapansi. "Iye," Munthu wofunikira kwambiri padziko lapansi. Mukuona? Chifukwa chiyani? Anthu achipembedzo, chipembedzo chachikulu kwambiri padziko lapansi, chipembedzo choona chokhacho padziko lapansi, chinali kuyima pamenepo, chikumupachika Mulungu yemwe amene Baibulo lawo linati akanadzabwera.

235 Ndi chifukwa chiyani iwo sanachiwone icho? Baibulo limatiuza ife kuti Mulungu anawachititsa iwo khungu kotero iwo sanakhoze kuchiwona icho. Iwo. . . Iye anati, "Ndani mwa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo?" Mwa kuyankhula kwina, "Ngati Ine sindinachite ndendende zomwe zinanenedweratu kwa Ine kuti ndichite, ndiye inu mundiuze Ine." *Tchimo* ndi "kusakhulupirira." Iye anachita ndendende zomwe Mulungu anamuuza Iye, koma iwo sanakhoze kuziwona izo.

236 Tsopano pamene iwe uyankhula kwa anthu, zimangokhala ngati kukhuthulira madzi pansana wa bakha. Kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Icho ndi chinthu chomvetsa chisoni, pamene iwe uwona mafuko awa ndi anthu, momwe iwo amachitira, okhuthala kwambiri ndi chipembedzo! Koma kodi Mzimu Woyera sumatiuza ife zimenezo? "Iwo adzakhala a mmutu, otukumuka mmalingaliro, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu, osayanjanitsika, otsutsa mwabodza, osadzigwira, ndi onyoza iwo amene ali abwino. Iwo akanadzakhala nawo mawonekedwe aumulungu,

koma akanadzakana Mphamvu ya Uthenga." Anati, "Kwa oterewo, chokanikoni."

237 Apa ife tiri, zipembedzo izi zikuchipotoza Icho. Iwo akutenga ulemelero wonse ndi Mphamvu, akuziyika Izo mmbuyo kwa atumwi, ndipo zina zonse za Izo uko mu Zakachikwi. Izo ziri basi monga munthu, monga ine ndinanenera mmbuyomu; munthu nthawizonse amapereka matamando kwa Mulungu pa chifukwa cha zomwe Iye anachita, nkumayang'ana mtsogolo ku zomwe Iye ati adzachite, ndi kumanyalanyaza zomwe Iye akuchita pakali pano. Ndizo ndendende. Munthu akadali chinthu chomwecho.

238 Panali Ayuda amenewo atayima pamenepo, akuti, "Ulemelero kwa Mulungu! Bwanji," pa mutu wa 6 wa Yohane Woyera, anati, "makolo athu anadya mana mchipululu!"

Ndipo Yesu anati, "Iwo ali, aliyense, anafa."

239 "Iwo anamwa madzi kuchokera pa Thanthwe mu chipululu, ndi chirichonse."

240 Iye anati, "Ine ndine Thanthwe limenelo." Uko nkulondola. Ameni. Iye anati, "Koma Ine ndine Mkate wa Moyo umene ukuchokera kwa Mulungu Kumwamba, Mtengo wa Moyo uja kuchokera ku Edeni kumbuyo uko. Ngati munthu adya Mkate uwu, iye sadzafa; Ine ndidzamuwutsa iye kachiwiri pa masiku otsiriza." Ndipo apobe sanakhoze kuchiwona icho! Uko nkulondola.

241 Mesiya amene atayima pamenepo, akuyankhula mawu omwewo a mu mtima mwawo, ndi zinthu monga zimenezo, kuwonetsera kuti Iye anali Mesiya, basi chimene Mesiya ankayenera kudzachita!

242 Ndipo iwo atayima pamenepo ndi manja awo ali kumbuyo kwawo, ndipo, "Huh! Sizingakhale chomwecho. Ayi, ayi. Iye—iye—iye sanabwere mwanjira yolondola. Mwaona, iye anachokera ku Betelehemu. Ndipo iye—iye si kanthu koma mwana wapathengo. Ndipo uyo ndi mdierekezi akugwira ntchito pa iye. Ife—ife tikudziwa kuti iye ndi wamisala. Iye ndi wopenga. Iye ali ndi mdierekezi." Mukuona? Maso awo kwenikweni anachititsidwa khungu kwa icho.

243 Tsopano, koma iwo akuyembekezera mneneri wawo. Ndipo iwo adzamulandira iye, adzalandira awiri a iwo. Uko nkulondola.

244 Tsopano zindikirani, kachiwiri, tsopano, ndiponso, pamene Ayuda awa . . . Ine ndikupatsani inu choyimira china chaching'ono, kuchitira kuti mukhoze kuzindikira kuti ndi Ayuda cha apa tsopano, ku mbali iyi ya Mkwatulo. Penyani zimene zikuchitika. Icho chikuimiridwanso . . . Ife sititenga nthawi kuti tichite icho, chifukwa ikutithera—ikutithera apa. Icho chayimiridwanso mu . . . mu chomwe chimatchedwa "vuto

la Yakobo." Tsopano penyani. Ayuda awa apa ali . . . Zindikirani. Oh, ndicho . . .

245 Ine—ine—ine ndingotenga nthawi pang'ono pokha apa, mwaona. Zimandipangitsa ine manjenje pamene ndiyamba kulumpha chozungulira monga choncho. Ndipo . . . Mukuona? Zindikirani. Ine ndikufuna kuti inu muchiwone icho. Ndipo ine—ine—ine basi . . . Chabwino, Mulungu akuwonetsani inu icho, ine ndikutsimikiza. Penyani.

246 Yakobo anali ndi ufulu woyambakubadwa. Nkulondola uko? Koma iye ndithudi anali shasha pang'ono ndi iwo. Mukuona? Iye anapita uko ndipo anakawanyenga abambo ake. Iye anamunyenga mchimwene wake. Iye anachita chirichonse. Koma, apobe, mwamalamulo, mpaka mmusi, iye anali nawo iwo, chifukwa Esau anali atawugulitsa iwo. Komano pamene iye anapita kumeneko kukawagwirira ntchito apongozi ake aamuna, iye anayika mitengo ya popula iyo mmadzi, kuti azipange ng'ombe zabelezo ndi zinthu kubala ana amanga-manga. Ndipo, oh, inu mukudziwa chirichonse chimene iye anachita monga chomwecho, basi kuti—kuti apeze ndalama. Tsopano penyani, tsopano. Iye anachotsedwa kwa anthu ake.

247 Tsopano, icho ndi choyimira cha Myuda tsopano. Iye ndi wolanda ndalama. Ine sindikusamala momwe iye angazipezere izo, iye amazipeza izo. Iye adzakusenda iwe wamoyo, kuti azipeze izo. Tsopano, inu mukudziwa zimenezo. Iye ndi shasha pang'ono, ndizo zonse. Mnyamata, usamachite naye iye; iye—iye adzakupeza iwe, mnyamata. Inde, bwana. Chifukwa chiyani? Iye ayenera kukhala chomwecho. Ndiwo mtundu wa mzimu umene ukulamulira.

248 Chimodzimodzi basi monga okonzanso awo, samakhoza kuwamvetsa Mawu awa, chifukwa umenewo unali mzimu wa munthu wotumizidwa kwa iwo.

249 Ndi m'badwo wa mphungu umene umagwira Mawu ndi vumbulutso. Nonse amene mukumvetsa zimenezo, kwezani mmwamba manja anu, kotero ine . . . Ndizo zabwino. Izo nzabwino. Mukuona? Ndizo zabwino. Tsopano, mwaona, ngati inu mungabwerere apa pansi pa Zisindikizo izi, ngati Izo zinafikapo konse . . . Pamene Izo zatsegulidwa, inu mukhoza kuwona ndendende chimene Mulungu akuchita, chimene Iye wachita, chimene Iye ati adzachite. Apa izo ziri, ndendende.

250 Ndipo ndi chifukwa chake anthu ankachita mwanjira imeneyo, chifukwa ndiwo mzimu umene unanenedweratu kwa m'badwo umenewo, kuti udzakhala pa iwo. Iwo sakanakhoza kudzachita kanthu kena kalikonse.

251 Ine ndikuganiza za Yohane, Paulo, ndi iwo, Mzimu wa mkango uja kumeneko, m-k-a-n-g-o ukuyima pamenepo, Mawu Iwoeni.

252 Paulo anayima pomwepo ndi Mawu amenewo, ndipo anati, "Ine ndikudziwa ichi, kuti padzakhala abale abodza adzawuke pakati panu, akupita konsekonse. Ndi zomwe iwo ati adzachite, zipembedzo ndi china chirichonse, pakati panu, ndi zomwe ati adzachite. Ndipo izo zidzapitirira mpaka ku masiku otsiriza, ndi nthawi zowopsya." Bwanji? Iye anali mneneri. Apo panayima Mawu amenewo mwa iye. Momwe izo zikanati zidzathere, kutali cha kumeneko; anati, "Anthu abodza pakati panu adzawuka, ndi kumadzayankhula zinthu, ndi kudzakokera kwina abale amene ali ophunzira." Ameneyo ndi ndendende wotsutsakhristu. Icho chinachita basi ndendende zimenezo.

253 Zindikirani atatha iwo kupita mu m'badwo wa mdima wa chisautso. Chinali chiyani icho? Panalibe kanthu kamene iwo akanakhoza kuchita. Roma anali mwini wa . . . Iye anali nayo mphamvu yachipembedzo, ndipo iye anali nayo mphamvu yandale. Panalibe kanthu komwe iwo akanachita, koma kumangovutikira kuti akhale moyo, ndi kudzipereka okha ngati nsembe. Iyo inali ng'ombe. Ndizo zonse zomwe iwo akanakhoza kuchita. Ndiwo mtundu wa Mzimu womwe iwo anali nawo, Mzimu wa Mulungu, ng'ombe.

254 Kenako, apa panadzabwera okonzanso, mutu wa munthu, wothyathyalika, wanzeru; Martin Luther, John Wesley, ndi ena otero, Calvin, Finney, Knox, ena onse a iwo. Apa iwo anatulukira, ndipo, pamene iwo anatero, iwo anali okonzanso. Iwo anatulukira, akukonzanso, akuwatulutsira panja anthuwo.

255 Ndipo anatembenukiranso mmbuyo momwe, chimodzimodzi monga iwo anachitira kumbuyo uko, ndi kukwatiwanso molunjika kumene mmbuyo kwa iye kachiwiri, pa kachitidwe kawo kachipembedzo, chimodzimodzi basi. Baibulo linanena chomwecho. Iye anali "hule," ndipo kenako iye anali ndi "timahule," ana aakazi, ndendende basi.

256 Ndipo Mulungu anati, "Ine—ine ndinamupatsa iye danga kuti alape, ndipo iye sanachite zimenezo. Kotero ine ndimutenga iye ndi ana ake, ndi kuwaponyera iwo kumeneko kumene iwo akuyenera kukakhalako." Ndizo ndendende. Tsopano, izo, Mulungu ananena chomwecho, pansi pa ichi, mwaona, pansi pa Chisindikizo. Tsopano, apo iye anali. Ife tikupeza kuti Iye akuchita zimenezo, ndipo Iye adzachita zimenezo. Ndipo iwo, aliyense, akulunjika njira imeneyo.

257 Koma, kwa onse amene ali nawo maina awo pa Bukhu la Moyo, Mulungu adzawayitana. Iwo adzalimva Ilo. "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa," Yesu anatero. Chinthu chokhacho chimene ife tiyenera kuchita ndicho kupanga kuyitana kwa nkhosa. Mbuzi sizimakudziwa Iko. Zindikirani. Koma, inu mukuona, kuyitana kwa nkhosa, "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa." Chifukwa chiyani? Kodi Liwulo ndi chiyani? Ine

ndikufuna ndikuwuzeni inu chomwe Liwu liri. Liwu ndi—ndi chizindikiro chauzimu.

258 Iye anati kwa Mose, "Ngati iwo sakamva Liwu la chizindikiro choyamba, iwo akamva Liwu la chizindikiro chachiwiri."

259 "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa." Pamene zinthu izi zikuyenera kumachitika mmasiku otsiriza, nkhosa za Mulungu zikulizindikira Ilo. Inde, bwana. Mukuona? Izo—izo zikulizindikira Ilo. "Nkhosa Zanga zimandidziwa Ine." Mukuona? "Mlendo izo sizingamutsatire." Musamawatsatire alendo amenewo. Icho chiyenera kukhala chizindikiro chotsimikiziridwa cha tsiku lino, ndipo izo zimachiwona Icho. Tsopano, tsopano zindikirani.

260 Tsopano, Yakobo, pamene iye ankabwera tsopano, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye anakhala nacho chikhumbo chopita (kuti?) kubwerera ku dziko la kwawo.

261 Oh, ndicho ndendende chimene Israeli wachita! Ndicho—ndicho . . . Ameneyo ndi Israeli. Yakobo ndi Israeli. Iye anangosinthidwa dzina lake, inu mukudziwa. Mukuona? Ndipo iye ali . . .

262 Iye anakafika kumeneko, ndipo iye anakatenga ndalama zonse zomwe akanatenga, ndipo iye anakazipeza, ndipo anazitenga izo mwanjira iliyonse yomwe iye akanakhoza, kuchokera kwa abale ake kapena wina aliyense. Kotero, kunyenga, kuba, kunama, njira iliyonse yomwe iye akanakhoza kuzitengera izo, iye anazitenga izo. Mukuona? Iye anatero.

263 Ndiyeno pamene anayamba kubwerera kwawo, iye anayamba kumverera kufuna kwawo mu mtima mwake. Koma pamene iye anayamba kubwerera, ali panjira yake akubwerera, iye anakumana ndi Mulungu, ndiye dzina lake linasinthidwa. Mukuona? Koma, mu nthawi iyi, iye anali wodandaula kwambiri, chifukwa iye ankachita mantha kuti Esau anali akumulondola iye. Mukuona?

264 Ndipo—ndipo penyani, penyani ndalama, dongosolo la ndalama. Basi monga momwe Myuda adzayesere kupanga pangano ili ndi—ndi Roma, mwaona, mu dongosolo lawo la ndalama. Zindikirani izi. Esau ameneyo sanafune ndalama zake; ngakhalenso Roma. Iye ali nacho chuma cha dziko lapansi mdzanja lake. Mukuona? Koma izo sizinagwire ntchito.

265 Koma ife tikupeza tsopano, kuti Israeli, mu nthawi imeneyo ya vuto, pamene iye anali Yakobo, iye analimbana ndi . . . izo zinagwira Chinachake chimene chinali chenicheni. Apo panali Munthu amene anabwera pamenepo. Yakobo anamukumbatira Iye ndi manja ake, ndipo iye anakhala pamenepo. Ndipo a—ndipo a—Munthuyo anati, "Ine ndiyenera kumapita tsopano. Kukuyamba kucha." Oh, kucha-kwa-tsiku uko! Mukuona? Kumakonzekera kuti kuche.

266 Koma Yakobo anati, "Ine—ine sindikusiyani Inu. Inu, Inu simungapite. Ine ndikhala nanu basi Inu." Mukuona? "Ine ndikufuna zinthu zisinthe pano."

267 Ndiwo handiredi ndi forte-foro sauzande, gulu lolanda ndalama lija, ndi zinthu monga choncho, pamene iwo adzawona choona, chinthu chenicheni choti achigwire. Apo payima Mose, ndipo apo payima Eliya. Ameni! Iwo adzalimbana naye Mulungu mpakana handiredi ndi forte-foro sauzande a mafuko a Israeli atayitanidwa kuti atuluke pomwe apo.

268 Izo zidzachitika basi isanafike nthawi ya Chisautso, mwaona, (oh nzodabwitsa bwanji) aponso, "vuto la Yakobo."

269 Apa ndi pamene handiredi ndi forte-foro sauzande akuyitanidwa kuti atuluke. Iwo, a—alalikiwo, aneneri awiri amenewo, iwo adzalalikira monga Yohane M'batizi. "Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Lapani, Israeli!" Alape chiyani? "Lapani muchoke ku machimo anu, kusakhulupirira kwanu, ndipo mubwererenso kwa Mulungu!"

270 Tsopano tiyeni ife tikumbukire chinachake apa. Zochitika zazikulu izi, kwa chirengedwe, zinachitikapo kale. Mu ndime ya 12 iyi apa, mwaona, "Dzuwa linada ngati chiguduli cha ubweya." Tsopano fanizitsani izi.

271 Tsopano, kumbukirani, izo sizikuchitika mwa Amitundu. Ndi Israeli. Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu. Tsopano, kumbukirani, ine ndinati ndiko kuyitana kwa handiredi ndi forte-foro sauzande. Mukuona? Nthawi iyi tsopano, ndi pamene Chisautso, chimene chiri choti chidzachite zimenezo. Ndipo ichi chikunena zomwe ziti zidzachitike mu Chisautso ichi.

272 Tsopano tiyeni titembenuzire ku Eksodo 10:21-23. Ndipo muwone apa pamene. . . Eksodo ndi pamene, ndithudi, Israeli anali akutuluka, akupita kuti akatulutsidwe. Eksodo, mutu wa 10, ndi ya 21, ndime ya 23. Ine ndimakhala wokondwa kwambiri ndi kumafuula, pamene ndikulemba zolemba izi, mwakuti nthawizina ine ndimatha kuzisokoneza izo. Chabwino, Eksodo 10:21-23. Chabwino, apa ife tikupita, 21 ndi 23.

> *Ndipo* Ambuye *anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako* moloza *kumwamba, kuti pakhale mdima pa dziko la Igupto, ngakhale mdima umene ukhoza kukhudzika.*
>
> *Ndipo Mose anatambasulira dzanja lake* moloza *kumwamba; ndipo uko* kunabwera *mdima wokandapala pa dziko lonse la Igupto kwa masiku atatu:* (Mukuona?)
>
> Tsopano, *iwo sankawonana wina ndi mzake, ngakhalenso sanathe kuwuka aliyense kuchokera pa malo ake kwa masiku atatu: koma. . . ana a Israeli anali ndi kuwala mokhala mwawo.*

273 Zindikirani, chimodzimodzi basi, tsopano bwerani cha apa, "Ndipo dzuwa linada bii ngati chiguduli." Mwaona, chinthu chomwecho! Zochitika za chirengedwe izi, chinali chiyani icho? Chiyani? Pamene chirengedwe chikuchitika monga chonchi, wakhala ali Mulungu akuyitana Israeli. Mukuona? Mulungu akuyitana Israeli. Tsopano, "Dzuwa kuda ngati . . . tsitsi." Tsopano, Mulungu anali pafupi kuti awombole Israeli kumeneko, chabwino, kuwabweretsa iwo kuchokera mdzanja la mdani wawo, yemwe anali Igupto, pa nthawi imeneyo.

274 Tsopano, apa, Iye akuwabweretsa iwo kuchokera mdzanja la Roma, kumene iwo anali atapanga pangano lawo. Chinthu chomwecho chikuchitika. Ndiyo miliriyo, a—nthawi imene miliri iyi idzayitane imene idzagwere gulu ili la Amitundu. Ngati ife tikanakhala nayo nthawi, ine ndikanakhoza kuwonetsa chimene chiti chidzachitike kwa mpingo wa Amitundu umenewo.

275 Baibulo linanena, kuti, "A—chinjokacho, Satana, anakwiya (ndiko, kukwiya) limodzi ndi mkaziyo (Myuda, Israeli), ndipo iye analavula madzi kuchokera mkamwa mwake, unyinji ndi makamu a anthu, amene anapita kukachita nkhondo ndi otsalira a mbewu ya mkazi." Chivumbulutso 13. Tsopano, mukuona pamenepo, ife tiri nazo izo. Ndipo apo ndi pamene Israeli akutumiza ake . . . Ine ndikutanthauza, Roma akutumiza ankhondo ake pambuyo pa otsalirawo, otsalira a mbewu ya mkazi.

276 Tsopano penyani. Nthawi yoyamba, manja a mdani wake, pamene Iye anali kuwawombola iwo kuti atuluke, dzuwa linasanduka chigudu- . . . linada ngati chiguduli. Tsopano, iyi ndi nthawi yachiwiri, kutha kwa nthawi ya Chisautso.

277 Tsopano, mu Daniele 12. Ngati ife tikanakhala ndi nthawi, ife tikanakhoza kuwerenga izo. Mu Daniele, ya 12—ndime ya 12 . . . Mutu wa 12, kani. Daniele anati, "Aliyense yemwe anapezeka atalembedwa mu Bukhu adzawomboledwa." Tsopano, kumbukirani, Daniele tsopano akuyankhula za nthawi iyi pamene izi . . . zinthu izi ziyenera kudzachitika, pamene Israeli ali woti adzawomboledwe, pamene a—pamapeto pa sabata yawo ya chisevente. Ndipo ndi pamene iwo akuyenera kuti adzawomboledwe. Tsopano yang'anani. Tiyeni ife tifike ku Daniele 12 apa, miniti yokha.

> *Ndipo pa nthawi imeneyo* Mikaeli adzadzuka, *kalonga wamkulu yemwe* anayimira *ana . . . kwa—kwa ana a anthu ako* (mwaona, ndiwo Ayuda): *ndipo kudzakhala . . . vuto, longa . . . silinakhalepo kuyambira pamene kunakhala fuko ngakhale mpaka nthawi yomweyo: . . .*

278 Tsopano fanizitsani zimenezo, ndendende zomwe Yesu ananena, Mateyu 24, "Padzakhala nthawi ya mavuto, imene siyinakhalepo kuyambira pamene kunakhala fuko." Taonani

pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, mwaona, chinthu chomwecho, nthawi ya mavuto. Zindikirani.

> . . . *kuyambira pamene kunakhala fuko ngakhale mpaka nthawi yomweyo: ndipo pa nthawi imeneyo anthu ako* . . . (Tsopano, mu la chisevente ili, gawo lotsiriza la chaka cha sevente.) . . . *anthu ako adzawomboledwa, aliyense yemwe ati adzapezeke atalembedwa mu bukhu.*

279 Okonzedweratu, mukuona, amene analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, adzawomboledwa pa nthawi imeneyo.

> *Ndipo ambiri a iwo* omwe *akugona mu fumbi la dziko lapansi adzawuka,* ndipo *ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku* manyazi osatha ndi mnyozo.

> Tsopano, ndiyeno anzeru *adzawala ngati kunyezimira kwa* miyamba; *ndipo—ndipo iwo amene atembenuzira ambiri ku chirungamo* adzawala *ngati nyenyezi kwa nthawi za nthawi.*

280 Icho, kenako anapitiriza, anamuuza Daniele kuti "atseke Bukhulo," pakuti iye akanakhala akupumula mu malo ake kufikira nthawi imeneyo.

281 Tsopano, mwaona, sizimapanga kusiyana kulikonse kaya iwe ukhala moyo kapena umwalira. Iwe udzatulukira, mulimonse. Mukuona? Musati . . . Kuti, kufa, si kanthu kwa Mkhristu. Iye samafa, mulimonse. Mukuona?

282 Tsopano, Daniele 12, ananena kuti aliyense amene anapezeka atalembedwa mu Bukhu akanadzawomboledwa.

283 Apa, Mulungu ali pafupi kuti amuwombole mwana Wake wamwamuna wachiwiri, Israeli, pambuyo pa Chisautso. Mwaona, nthawi yachiwiri, Israeli, Wake . . . Israeli ndi mwana Wake wamwamuna. Inu mukudziwa zimenezo. Israeli ndi mwana wamwamuna wa Mulungu, kotero Iye akudzamuwombola iye apa mu nthawi ya Chisautso, chimodzimodzi basi momwe Iye anachitira uko ku Igupto.

284 Tsopano tiyeni tiyimire apa, kachiwiri, ndi—ndi kutenga chinachakenso, kotero, tisanazibweretse izo pachimake. Tsopano penyani apa. Aneneri awiri awa, tayang'anani zimene iwo ati akachite tsopano, chimodzimodzi basi monga momwe Mose ndi iwo anachitira kumusi uko. "Ndipo apo ndinapatsidwa ine bango . . . " Ndipo ndime ya 3 ya mutu wa 11.

> *Ndipo Ine ndidzapereka mphamvu kwa mboni zanga ziwiri,* zimene *zidzanenera kwa masiku sauzande thuu handiredi ndi sikisite, zitavala ziguduli.*

> *Zimenezo ndiyo mitengo iwiri ya azitona,* . . .

285 Inu mukukumbukira zimenezo, ndipo Zerubabele, ndi ena otero, anali woti akamangenso kachisi.

> . . . *ndi zoyikapo nyali ziwiri* zomwe zikuyima *pamaso pa Mulungu wa dziko lapansi.*

> . . . *ngati munthu aliyense . . . adzawapweteka iwo, moto udzatuluka kuchokera mkamwa mwawo,* . . .

286 Kumbukirani, kuchokera mkamwa mwa Khristu munatuluka lupanga, Mawu.

> . . . kuwononga *adani awo: ndipo ngati munthu wina* adza*wapweteka iwo, iye adzayenera kuphedwa mwanjira iyi.*

287 Tsopano, ife tikuwudziwa, "moto." Mu mutu wa 19, wa Kudza kwa Khristu, "munatuluka lupanga Lake kuchokera mkamwa Mwake," amene anali Mawu. Nkulondola uko? Mawu! Oh, ngati mungamvetse chipangizo ichi tsopano, kwa Chisindikizo icho mawa usiku! Mwaona, Mawu ndi chinthu chimene Mulungu amamudulira nacho mdani Wake. Mukuona?

288 Tsopano penyani apa. Pamene aneneri awa akunenera kumeneko, iwo . . . Ngati munthu aliyense adzawachitira iwo choyipa, kuwapweteka iwo: "moto udzatuluka kuchokera mkamwa mwawo," Moto wa Mzimu Woyera, Mawu. Mawu ndi Mulungu. Mawu ndi Moto. Mawu ndi Mzimu. Mukuona? "Udzatuluka kuchokera mkamwa mwawo."

289 Tayang'anani pa Mose. Tiyeni tiwone chimene chinatuluka kuchokera mkamwa mwake. Iwo, Israeli, anafikako, momwe iwo ankachitira kumeneko, a—a . . . Ine ndikutanthauza, Igupto, iwo anali kuwazunza Ayuda awa. Mose . . . Chabwino, iwo sankawalola iwo kuti azipita. Farao sankawalola. Mulungu anayika Mawu mkamwa mwa Mose, mwaona, ndi maganizo a Mulungu akupita mu mtima mwa Mose, iye akupita kumeneko tsopano kukawafotokoza iwo, ndiye iwo akudzakhala Mawu. Anatambasula dzanja lake, anati, "Pakhale ntchentche," ndipo apa panabwera ntchentche. Penyani apa.

> *Ndipo ngati munthu aliyense* adzawapweteka *iwo, moto udzatuluka kuchokera mkamwa mwawo, ndi kuwaononga* adani *awo:* . . .

290 Mukuona? Ndi zimenezo apo. Iwo akhoza kuyankhula chimene iwo akufuna, ndipo apo icho nkuchitika. Ameni!

> . . . *ndipo ngati munthu aliyense . . . adzawapweteka iwo,* iwo *ayenera kudzaphedwa mwanjira iyi.*

291 M'bale, Mulungu akubwera powonekera apa!

> *Iwo ali nayo mphamvu yo—mphamvu yotseka* miyamba, *kuti isavumbe mmasiku a kunenera kwawo:* . . .

292 Eliya, iye akudziwa momwe angachitire zimenezo; iye anazichitapo izo mmbuyomo. Ameni! Mose akudziwa momwe angachitire izo; iye anazichitapo izo mmbuyomo. Ndi chifukwa chake iwo anasungidwa. Tsopano . . . Ameni!

293 Ine ndikhoza kunena chinachake chabwino kwambiri pomwe pano, koma ine kulibwino—kulibwino ndichisunge icho mpaka mawa usiku. Mukuona? Chabwino.

> *. . . ndi kukhala nayo mphamvu pa madzi kuwasandutsa iwo kukhala mwazi, ndi kulikantha dziko lapansi ndi . . . miliri,* mowirikiza *momwe iwo angafunire.*

294 Ndi chiyani chimenecho? Ndi chiyani chimene chingabweretse zinthu izi koma Mawu? Iwo akhoza kuchita nacho chirengedwe mulimonse mmene iwo akufunira. Ndi izi apa. Ndi iwo amene akubweretsa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Iwo akuvundukula ndi kuchitsegula icho. Ndiyo Mphamvu ya Mulungu, kuti isokoneze chirengedwe. Mwaona, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi kwathunthu ndi kusokonezeka kwa chirengedwe. Kodi mukumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndi chimenecho Chisindikizo chanu. Ndani yemwe akuchita izo? Ndi aneneri, mbali inayo ya Mkwatulo. Ndi Mphamvu ya Mulungu, Mawu a Mulungu, iwo adzangotsutsa chirengedwe. Iwo akhoza kutumiza zivomezi, kusandutsa mwezi kukhala magazi, dzuwa likhoza kuzima, kapena chirichonse, mwa kulamula kwawo. Ameni!

295 Ndi zimenezotu pamenepo. Ndi zimenezotu pamenepo. Mukuona? Mukuona momwe Zisindikizo zinatsegukira, kumusi uko mu m'badwo wa mpingo, momwe izo zinawonetsera ofera?

296 Ndipo tsopano apa pali aneneri awiri awa ayima apa ali ndi Mawu a Mulungu, kuti akachite chirichonse chimene iwo akufuna kwa chirengedwe. Ndipo iwo akugwedeza dziko lapansi. Ndipo izo zikuwonetsa ndendende yemwe akuchita izo. Ndi Mose ndi Eliya, chifukwa apo pali utumiki wawo ukuwonetseredwa kachiwiri, ndi amuna awiri onsewo. Oh, mai! Kodi mukuzimvetsa izo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mwaona chimene Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chiri? Ndi aneneri amenewo. Tsopano zindikirani. Musalole kuti icho chikutsamweni inu. Koma, penyani chimene chinatsegula Chisindikizo chimenecho, aneneri! Mukuona? Psyii! Ameni! Ndi zimenezotu pamenepo.

297 Oh, ife tikukhala mu tsiku la mphungu, m'bale, kulunjika mmwamba pakati pa mitambo!

298 Iwo anatsegula Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chimenecho. Iwo ali nayo mphamvu yochitira zimenezo. Ameni! Ndi chimenecho Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chanu chikutseguka. Mukuona?

299 Tsopano ife tibwerere mmbuyo kumene apa, ndipo Yesu anayankhula kuti izo zikanadzachitika. Mmbuyo momwe umo mu Chipangano Chakale, mmbuyo mu Ezekieli, mmbuyo mwa aneneri akale, iwo anayankhula kuti izo zikanadzachitika.

300 Ndipo apa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chatsegulidwa, ndipo iwo akumati, "Chabwino, ndicho chinthu chachinsinsi. Ndi chiyani chinachita icho?"

301 Apa pali chinsinsi cha icho, aneneri, chifukwa Baibulo linanena chomwecho apa. Iwo akhoza kutsegula izo, nthawi iliyonse iwo . . . Iwo akhoza kuchita chirichonse chimene iwo akufuna kwa chirengedwe. Ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho chimene iwo anachita, ameni, chifukwa iwo akudziwa momwe izo zimachitidwira. Ameni! Ulemelero!

302 Pamene ndinawona zimenezo, ine ndinangonyamuka kuchoka pampando ndi kuyamba kumayendayenda. Ine ndinaganiza, "Ambuye, momwe ine ndikukuthokozerani Inu, Atate Akumwamba!"

303 Ndi izo pamenepo. Ndi zimenezotu. Iwo anatsegula Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chimenecho. Ameni! Tawawoneni amenewo, "Ngati munthu aliyense awapweteka iwo, moto ukutuluka kuchokera mkamwa mwawo," Mawu. Mzimu Woyera utabwera pa atumwi, mukuona. "Moto unkatuluka kuchokera mkamwa mwawo."

304 Tsopano zindikirani uko mu Chivumbulutso 19, ife tikuwona chinthu chomwecho, "Ndipo lupanga lalikulu likutuluka kuchokera mkamwa Mwake," Mawu. Mukuona? Kudza kwa Khristu. "Ndipo Iye anawapha adani Ake ndi Ilo." Kodi nkulondola uko? Tsopano Iye ali pa njira Yake. Muyang'aneni Iye tsopano. Chabwino.

Awa ali nayo mphamvu yotsekera miyamba, *kuti isavumbe mmasiku a uneneri wawo:* . . .

305 Mnyamata, ndiko kusokoneza chirengedwe! Tsopano, ndi kwa nthawi yotalika bwanji yomwe—yomwe munthu uyu, Eliya, anatseka miyamba? [Osonkhana akuti, "Zaka zitatu ndi theka."—Mkonzi]. Ndi zimenezotu pamenepo, ndendende. Ndi lotalika bwanji la chisevente la Daniele, gawo lotsiriza la masabata sevente? ["Zaka zitatu ndi theka."] Ndi zimenezotu pamenepo, ndendende.

306 Kodi Mose anachita chiyani? Iye—iye—iye anasandutsa a—madzi kukhala magazi. Iye anachita mitundu yonse iyi ya zozizwitsa, ndendende basi zomwe zanenedweratu apa pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi. Ndipo apa iwo ali, mu Chivumbulutso 11, akuchita chinthu chomwecho. Ameni!

307 Pali malo atatu osiyanasiyana m'Malemba, momwe umo, omwe akulumikiza chinthucho pamodzi kumene. Ndiko

kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Pomwe apo icho chiri. Ameni! Ulemelero! Tsopano zindikirani.

> *Awa ali nayo mphamvu yotseka* mmiyamba, mmasiku a uneneri wawo, kuti isavumbe: *ndi . . . mphamvu pa madzi kuwasandutsa iwo kukhala magazi, . . . kukantha dziko lapansi ndi . . . miliri,* mowirikiza *momwe iwo adzafunire.*

308 Oh, mai! Ndi zimenezotu pamenepo. Tsopano kutsegula pomwe apa ku miliri, mwaona. Chirengedwe chonse chasokonezedwa, mu Mliri uwu Wachisikisi . . . kapena Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, kuchitsegula. Ndizo ndendende zomwe zinachitika. Tsopano penyani. A . . .

309 Apa, Mulungu ali pafupi kuti amuwombole mwana Wake wamwamuna, Israeli, mwa mtundu womwewo wa chisautso chimene Iye anachita kumusi uko. Iye anamutumiza Mose kumusi uko ndipo anakamuwombola Israeli. Kodi nkulondola uko? Ndipo anakachita zinthu zomwezi. Iye anamutumiza Eliya kwa Ahabu, ndipo seveni sauzande anatuluka. Nkulondola uko? Iye akuwatumizanso iwo apa kachiwiri, mu nthawi ya Chisautso, ndipo akuyitana handiredi ndi forte-foro sauzande.

310 Tsopano, mwaona, inu mukuzindikira, pakati pa Chivumbu- . . . kapena pakati pa mutu wa 6, kapena Mliri Wachisikisi . . . Chisindikizo, mundikhululukire ine, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Mutu wa 7 wa Chivumbulutso, mwamasamu, zikukhala pamodzi molondola.

311 Monga momwe America aliri nambala sartini: anayamba ndi mayiko sartini, nyenyezi sartini pa mbendera, zigawo sartini, milozo sartini. Chirichonse ndi sartini, sartini. Ndipo akuwonekera pomwe apa pa mutu wa 13 wa Chivumbulutso. Uko nkulondola. Iye ndi sartini, ndipo mkazi.

312 Tsopano, pamene Iye anali pafupi kuti amuwombole Mwana Wake wamwamuna wobalidwa yekhayo, yemwe anali wobadwa Wake yekhayo. Yakobo ndi mwana Wake wamwamuna; koma uyu ndi Mwana Wake wobalidwa yekhayo. Mateyu 27, tiyeni tiwone chimene Iye anachita kumeneko. Mateyu, mutu wa 27. Tsopano, kumbukirani, Mwana Wake anali atamenyedwa, ndipo anali atavutitsidwa, ndipo iwo anali atamutonza Iye. Ndipo Iye anali tsopano atapachikika pa mtanda, nthawi ya firii koloko, pa Lachisanu Lapaskha masana. Ziri pafupi kuti zichitike! Mateyu, mutu wa 27 wa Mateyu, ndi a—ndime ya 45, ine ndikukhulupirira iyo ili.

> *Tsopano kuyambira ora lachisikisi kunali mdima padziko lonse* mpakana *ora lachinaini.*

313 Tsopano zindikirani chimodzimodzi basi zomwe Iye anachita mmbuyo muno tsopano, mu izi. Mukuona?

Ndipo ine ndinawona pamene anatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi,. . . taonani, kunali chivomezi chachikulu; ndi dzuwa linada monga chiguduli cha ubweya, ndi mwezi—ndipo mwezi unakhala ngati magazi;

314 Kuda, mdima! Igupto; kuda, mdima!

315 Mulungu, akumuwombola Yesu pa mtanda, basi Iye asanamudzutse Iye kuchokera ku chiwukitsiro. Choyamba, mdima; dzuwa linazima pakati pa tsiku, ndipo nyenyezi sizinathe kuwala. Masiku awiri kuchokera pamenepo, Iye amakamuwukitsa Iye ndi chigonjetso champhamvu.

316 Litatha dzuwa, ndi mwezi, ndi nyenyezi, ndi chirichonse, mu Igupto, zonse izi zomwe zinachitika, Iye anamuwombolera Israeli ku dziko lolonjezedwa.

317 Ndi izi apa, mu nthawi ya Chisautso, ndipo apa pakuyima aneneri amenewo amene ali nawo ulamuliro wa Mawu amene Mulungu amawapatsa Iwo. Iwo akhoza kuyankhula kokha pamene Mulungu akuwapatsa iwo Mawu.

318 Tsopano, iwo si milungu. Iwo ali mwakanthawi. . . Mochepa, iwo ali, chifukwa Yesu anati iwo anali. Anati, "Inu mumawatcha iwo milungu, amene Mawu a Mulungu ankafikirako." Koma, penyani, ndiwo amene Mulungu amabweretserako Mawu. Ndipo pamene iye awayankhula Iwo, izo zimachitika. Ndizo zonse.

319 Ndipo apa iye ali ndi kutuma kochokera kwa Mulungu, kuti adzakanthe dziko lapansi, chirichonse chimene iye akufuna kuchita (oh, mai), kuyimitsa miyamba. Ndipo iye akuchita. Chavuta ndi chiyani? Iye akukonzekera kuti atenge handiredi ndi forte-foro sauzande atuluke, kwa chiwombolo, kuchokera mu Bukhu la Chiwombolo. Ndipo izo ziri pansi pa Chisindikizo cha Chiwombolo, mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Ndi chimenechotu, mzanga wokondedwa. Ndicho Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chimenecho; chakhala chiri mwachinsinsi kwambiri.

320 Tiyeni tingotenga. . . Ife tiri nawo maminiti ena teni. Tiyeni tingotenga pang'ono pokha, mwaona. Ine ndiri nawo pafupifupi masamba awiri kapena atatu. Chabwino, ine ndiyenera. . . Inu mukhoza kungowona, *apa*. Ine ndikuganiza kuti pali pafupifupi. . . Pa chimodzi chimenecho, ine ndikuganiza kuti ndiri ndi pafupifupi masamba fifitini atsalirabe, ine ndikanakhoza kufika kwa iwo. Oh, pali zochuluka kwambiri pa zimenezo! Mai, iwe ukhoza kumangopitirirabe kuchoka pa malo kupita pa malo! Koma ine ndikuwopa kuti ndikusokonezani inu ndikamwaza zambiri za izo. Ndipo ine sindiri. . . Ine sindingakhoze kuziyika izo pamodzi momwe ine ndiyenera kuchitira.

321 Mu Yesaya, tiyeni titenge ichi. Yesaya, mneneri, anachiwona Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi chikutseguka,

ndipo anayankhula za Icho; monga kaya Icho nchofunikira, kapena ayi. Mukuona?

322 Chabwino, chinthu chonsecho, dongosolo lonselo la chiwombolo, lagona pansi pa Zisindikizo izi; Bukhu lonselo.

323 Tsopano kumbukirani, ife tinawona kuti Yesu anachiwona Icho. Nkulondola uko? Mukuona? Yesu anachiwona Icho. Ndipo tsopano ife tinawapeza ena amene anachiwona Icho. Ife tinachipeza Icho chikuimiridwa mwa—mwa Yakobo. Ife tinachipeza Icho chikuimiridwa mu Igupto. Ife tinachiwona Icho chikuimiridwa pa mtanda.

324 Tsopano tiyeni tibwerere ku Yesaya. Ine ndiri nawo aneneri ambiri amene ndawalemba pansi apa, nawonso. Tiyeni chabe . . . Ine ndikuzikonda izi, izi za Yesaya. Tiyeni tibwerere mmbuyo apa ku Yesaya, mutu wa 13 wa Yesaya. Ine ndimakonda . . .

325 Yesaya ali—Baibulo lathunthu, mwa Iyeyekha, inu mukudziwa. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Mwaona, Yesaya akuyamba ndi chirengedwe; mkati mwa Bukhu iye akumubweretsa Yohane; ndipo pa mapeto iye akubweretsa Zakachikwi. Ndipo muli Mabuku sikisite-sikisi mu Baibulo, ndi mitu sikisite-sikisi mu Yesaya. Liri kufotokoza kwathunthu, Palokha.

326 Zindikirani, mutu wa 13 tsopano, wa—wa Yesaya. Tiyeni tiyambire apa pa ndime ya 6.

> *Kuwani inu; pakuti tsiku la* Ambuye *liri pafupi; ilo lidzadza monga chiwonongeko chochokera kwa Wamphamvuzonse.*

327 Penyani Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi chikutseguka pamwamba apa tsopano. Mmbuyo muno apa, zaka seveni handiredi ndi sartini Khristu asanabwere, ndipo Iye wakhala zaka thuu sauzande, izo zingakhale pafupifupi seveni . . . pafupi zaka twente-seveni handiredi zapitazo. Yesaya anachiwona Chisindikizo ichi chitapachikika pamenepo. Chabwino.

> *Chotero manja onse adzafooka, ndi mtima wa munthu aliyense udzasungunuka:*

328 Kodi Yesu ananena chiyani? "Ndipo chifukwa chakuti kusaweruzika kudzachuluka, a—chikondi cha ambiri chidzazirala ndiye." "Ndipo mitima ya anthu idzakhala ikulephera, chifukwa cha mantha; nyanja ikubangula." Mwaona, mitima ya anthu idzakomoka.

> *Ndipo iwo adzawopa: kuwawa* kwa *zisoni kudzawagwira iwo; iwo adzakhala mu ululu monga mkazi yemwe akuvutika pakubala: iwo adzazizwa mmodzi pa mzake; nkhope zawo zidzakhala monga* manyazi.

329 Zindikirani za zimenezo apa, oh, "nkhope zawo, manyazi." Ife tiyenera kufika kwa zimenezo, miniti yokha. Ine ndizigwira zimenezo, mwaona.

> *Taonani, tsiku la* Ambuye *likudza, lankhanza limodzi ndi mkwiyo ndi ukali wowopsya, kuti lidzapangitse dziko kukhala bwinja: ndipo iye adzawawononga ochimwa ake mmenemo.*

330 "Dziko," ndizo zonse za ilo, za ilo mukuona. Zindikirani.

> *Pakuti nyenyezi zakumwamba ndi kuwundana kwake sizidzapereka kuwala kwawo: dzuwa lidzadetsedwa mu kutuluka kwake, ndipo mwezi sudzapangitsa* nyali *zake kuti ziwale.*
>
> *Ndipo ndidzalanga dziko lapansi chifukwa cha kuyipa kwawo, ndi* kusaeruzika, ndi kuyipa kwa *mphulupulu zawo; ndipo ndidzawachititsa amwa-. . .*

331 Ine—ine sindikudziwa momwe ndingatchulire iwo, amwa-. . .[Osonkhana akuti, "Amwano."—Mkonzi]. Ine sindingakhoze kutchula iwo, mwaona.

> *. . .a kudzikuza kusiya, ndipo ndidzatsitsira mmusi kudzikweza kwa—kwa owopysa—owopsya.*

332 Mwaona, pamenepo, chimodzimodzi basi, Yesaya anawona chinthu chomwecho chimene Yesu anayankhula za icho. Zimene Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chikuwululula. Pamene Iye akuliyeretsa dziko lapansi ndi chisautso, ndiyo nthawi ya Chisautso, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ichi. Inde, iye anali mneneri, ndipo Mawu a Mulungu anazindikirika kwa iye. Ndizo zaka twente-seveni handiredi zapitazo.

333 Mowonadi! Ine ndikungofuna kunena izi. Dziko lonse, monga Yesaya apa, "monga mkazi amavutikira," chirengedwe chonse chikuvutikira. Kodi kubuula konseku ndi kuvutikira uku ndi kwa chiyani? Monga a—a—mkazi amene akuyembekezera kubereka; dziko lapansi palokha, chirengedwe.

334 Bwanji, mzinda uwu kuno, tiyeni titenge mzinda wathu womwe; pamene, malo omwera mowa, ndi uhule, ndi uve, ndi zonyansa, monga mzinda wina uliwonse!

335 Bwanji, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akanakhala bwinoko, kumayang'ana pa ilo momwe Iye analipangira ilo, zaka masauzande zapitazo. Pamene Ohio ankapita mmusi, iwo analibe madzi obwerera ndi zosefukira. Iwo analibe tchimo mu chigwa. Njati zinkayenda kudutsa kuno, ndipo—ndipo Cherokee wakale ankazisaka izo ndi kumakhala moyo wabwino. Kunalibe vuto, nkomwe.

336 Koma, munthu anadzabwerako, apo ndi pamene tchimo likubwerapo. Pamene anthu anayamba kuchulukana pa nkhope ya dziko lapansi, ndiye tchimo ndi chisokonezo zinabweramo.

Uko nkulondola, nthawizonse munthu. Bwanji, ine ndikuganiza kuti icho ndi chamanyazi!

337 Ine ndinayima, tsiku lina, mdziko la kwathu uko, tsopano mu Arizona. Ndipo ine—ine ndinawerenga, pamene ine ndinali mwana, zokhudza Geronimo, ndi—ndi Cochise, ndi Apaches akale amenewo. Chifukwa, ine ndinalalikira kwa iwo kumeneko. Anthu abwino! Ndipo ena a anthu abwino kwambiri omwe inu mungafune kukumana nawo, ndi Amwenye achi Apache amenewo.

338 Ndiyeno ine ndinapita cha kumeneko ku—ku Tombstone, kumene iwo ali nazo zinthu zakale zonse ndi zinthu zochokera ku nkhondo. Ndipo ndinayang'ana pa . . . Iwo nthawizonse, inu mukudziwa, iwo nthawizonse akhala akumutenga Geronimo ngati—ngati chigawenga. Kwa ine, iye anali wachi Amerika wamagazi ofiira. Mwamtheradi! Iye anali kungomenyera maufulu ake, monga aliyense angachitire. Iye sankafuna chivundi chimenecho mdziko lake. Ndipo penyani chimene icho chiri tsopano; kuwasandutsa ana ake, ana ake aakazi, kukhala mahule, ndi china chirichonse; ndipo azungu anabwera mmenemo. Mzungu ndi chigawenga.

339 Mmwenyeyo anali wosamalira. Iye anali—iye anali a—wosamalira chirengedwe. Iye amakhoza kutuluka ndi kukapha njati, fuko lonselo linkadya chirichonse chotsalira cha iyo. Iwo ankagwiritsa ntchito chikopacho kupangira zovala ndi mahema, ndi china chirichonse. Ndipo mzungu anadzabwera ndi kudzawombera iyo, kukhala chandamale; bwanji, ndi chamanyazi chotero!

340 Ine ndinawerenga nkhani mu pepala, pamene, mu Afrika, malo aakulu awo odzaza ndi zinyama zakuthengo! Iwo anali nawo amuna awa, Arthur Godfrey ndi iwo, akupita kumeneko, kumakawombera njovu izi ndi zinthu, kuchokera mma helikopita ndi zinthu monga chomwecho. Chithunzi cha njovu yayikazi yokalamba ikuyesera kuti ife, ndipo misonzi, monga, ikuyenderera pansi pa nkhope yake. Ndipo zamphongo ziwiri zazikulu zikuyesetsa kuti zimugwire iye, kumutetezera . . . Bwanji, ndi tchimo. Amenewo si masewero.

341 Pamene ndinayima ku thengo kutsidyako, ndi kumene ndimakasaka ndi zinthu monga chomwecho, ndi kuwona kumene alenje achizunguwo amabwerako ndi kuwawombera agwape amenewo, ndi kudula miyendo ya kumbuyo kuyichotsa kwa iwo. Ndipo nthawizina kupha agwape aang'ono aakazi eyiti kapena teni, ndi kuwasiya iwo atagona pamenepo. Ndipo tiana tawo tikuthamanga pozungulira, tikuyesetsa kuti tiwapeze amayi awo. Ndipo kodi inu mukutanthauza kuti umenewo ndi ukatswiri? Iko ndi kupha kwangwiro, mu bukhu langa.

342 Ine ndikuyembekeza kuti Canada sayika misewu iliyonse mmenemo, malingana ngati ndiri moyo, kuti aletse zigawenga za

Chimerika zimenezo kufika kumeneko. Uko nkulondola. Iwo ndi amasewera osauka kwambiri amene ine ndinawawonapo mmoyo wanga.

343 Tsopano, osati onse a iwo. Alipo ena enieni, anthu enieni, koma ndi mmodzi pa sauzande, omwe inu mungamupeze.

344 Kuwombera chirichonse chimene iwo angakhoze kuchiwona, mulimonse momwe iwo akufuna kuchitira. Uko nkulondola. Uyo ndi wakupha. Uko nkulondola. Iye ndi wopanda mtima. Ndipo iye amawombera, isali nyengo yake.

345 Chabwino, kumtunda uko ku Alaska uko, ine ndinali pamwamba apo ndi mmodzi wa anamulondola amenewo. Iye anati, "Ine ndinatenga . . . ine ndimakhoza kupita kumeneko tsopano, ndi kukapeza magulu onse a agwape aakulu amenewo kapena . . . osati gwape, koma insa zitagona pamenepo; ziri ndi zipolopolo za mfuti ya makina ya fifty-caliber kupyoza mu nyanga zake, kumene oyendetsa ndege Achimereka awa kunja kumeneko, mu Alaska, ankawombera ndi mfuti yamakina, kuchokera mu ndege, gulu la insa." Uko ndiko kupha kwenikweni.

346 Iwo ankadziwa, kuti pamene iwo apha njati, iwo akanakhoza kuthana naye Mmwenye. Iye akanafa ndi njala. Ndi chifukwa chake Cochise anachita kudzipereka; ake, akalonga ake onse, ndi ena onse a iwo, ana ake, ndi anthu ake onse, anali kufa ndi njala. Iwo ankapita kumeneko ndi zazikulu, akatundu aakulu a zimenezo, Buffalo Bill ndi anthu akuchigwa awo, iwo anawombera njati zonse izo, forte, fifite, masana. Iwo ankadziwa, kuti pamene iwo anazimaliza izo, iwo anathana naye Mmwenye. Ndipo, oh, mai! Banga pa mbendera, momwe iwo anawachitira Amwenye amenewo. Ndi zimenezotu pamenepo.

347 Koma kumbukirani, Baibulo linati, "Ora lidzafika pamene Mulungu ati adzawawononge iwo amene akuwononga dziko lapansi." Ndi dziko lonse!

348 Tayang'anani pa zigwa zimenezo. Ine ndinali kuyima pamwamba apo, tsiku lina, ndikumayang'ana mmusi mu chigwa ku Phoenix. Ndinapita pamwamba pa Phiri Kummwera, mkazanga ndi ine tinali titakhala pamwamba pamenepo, ndipo ndinayang'ana mmusi ku Phoenix. Ndipo ine ndinati, "Kodi icho si choyipa?"

Iye anati, "Choyipa? Iwe ukutanthauza chiyani?"

349 Ine ndinati, "Tchimo. Ndi kuchuluka kotani kwa zigololo, ndi kumwa, ndi kutukwana, ndipo Dzina la Ambuye likugwiritsidwa ntchito mwachabe, mu chigwa chimenecho uko; ndi anthu pafupifupi handiredi ndi—ndi forte, fifite sauzande, kapena mwinamwake anthu thuu handiredi sauzande, mu chigwa chimenecho!"

350 Ine ndinati, "Zaka faivi handiredi zapitazo, kapena sauzande, umo munalibe kanthu koma akaloga, lijowe, ndi ankhandwe akale akuthamangathamanga mu mchenga wa mu mtsinje kumeneko, a—mmakhwawa." Ndipo ine ndinati, "Umo ndi momwe Mulungu analipangira ilo."

351 Koma, munthu anabweramo. Kodi iye anachita chiyani? Iye anadzazitsa dziko ndi uve. Misewu yadzaza ndi ndulu. Zimbudzi, a . . . Ndipo mitsinje yaipitsidwa ndi—ndi uve. Iwo sangakhoze . . . Bwanji, inu kulibwino musamwe ena a madzi amenewo; inu mungatenge chirichonse. Mukuona? Tayang'anani pa icho. Osati kuno kokha, koma, dziko lonse, chinthucho chawonongedwa!

352 Ndipo dziko, chirengedwe, (Mulungu atichitire chifundo!) dziko lonse liri mu—mu ululu wa kubala. Dziko likuyesetsa, ilo "likubuula," Yesaya anatero. Chavuta ndi chiyani? Ilo liri mu . . . likuyesetsa kubereka dziko latsopano, kwa Zakachikwi, kumene onse . . . ? . . . Kuyesetsa kubereka dziko latsopano, kwa anthu atsopano omwe sadzachimwa ndi kuliwononga ilo. Uko nkulondola. Ilo liri mu ululu. Ndicho chifukwa chake i—i . . . Ife tiri mu kubuula, Khristu, kuti abereke Mkwatibwi. Chirichonse chikusawutsika ndi kubuula. Mwaona, pali chinachake chikukonzekera kuti chichitike.

353 Ndipo Mliri Wachisikisi uwu udzalilola ilo kuti lizipita. M'bale, chivomezi chidzaliphulitsa nkulitsegula, ndipo nyenyezi zidzagwedezeka, ziphala zamoto zidzatulukira, ndipo dziko lapansi lidzadzikonza lokha kukhala latsopano. Phala lamoto latsopano lidzafalikira kuchokera mkati mwa dziko lapansi. Ndipo ilo lidzasweka, lonse mozungulira ndi kuzungulira ndi kuzungulira, pamene ilo lizidzatembenuzika kumeneko.

354 Ndipo ine ndikukuwuzani inu, mmawa wina pamene Yesu ndi Mkwatibwi Wake azidzabwerera ku dziko lapansi, kudzakhala paradizo wa Mulungu kumeneko. Mwakuti, oh, mai, asilikali akale amenewo a nkhondo, adzayenda kudutsa mmenemo ndi abwenzi awo ndi okondedwa. Nyimbo zidzadzaza mu mlengalenga, za khamu la Angelo. "Oh, wachita bwino, wantchito Wanga wabwino ndi wokhulupirika. Lowa mu zisangalalo za Ambuye, zomwe zakhala zitakonzedwera iwe, zonga iwe ukanayenera kukhala nazo kumbuyo uko Eva asanayambitse kugudubuzika kwa mpira mu tchimo." Ameni! Psyii! Inde.

355 Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chidzachita chinachake. Inde, bwana. Moona dziko lonse likubuula ndi kumva kuwawa, chifukwa cha m'badwo wa Zakachikwi!

356 Tsopano, lomwe liripoli tsopano lanyowetsedwa ndi uve! Zimenezo ine ndinazilalikira kuno, osati kale kwambiri, ine ndikukhulupirira, ndinalalikira ku kachisi, *Dziko Likuphwasuka Pakati.* Ndizo ndendende. Penyani

zomwe zikuphwasuka pakati mdziko. Penyani, chirichonse chikuphwasuka, cha ilo. Ndithudi, ilo liri. Ilo—ilo liyenera kuphwasuka. Inde, bwana.

357 Penyani, chimango chake! Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chifukwa chimene dziko liyenera kuchita izo. Chimango cha dziko lino, chitsulo, ndi mkuwa, ndi zipangizo za dziko lapansi, zachotsedwamo mwa ilo, chimango chake, chifukwa cha nkhondo ndi mafakitare, mpaka ilo liri pafupi basi kukonzekera. . . Chabwino, ife sitinakhalepo nacho chivomezi mpaka tsiku lina, cha kuno mu gawo ili la dziko; basi tsiku lina kuno, inu mwaona, St. Louis ndi kumusi kudutsa kumeneko. Ilo likupyapyala kwambiri. Iwo asololamo chirichonse kuchotsa mmenemo. Mukuona?

358 Ndale zake zawonongeka kwambiri, palibe nkomwe woonamtima pakati pawo, mwaona, kachitidwe kake. Makhalidwe ake ndi otsika kwambiri, ilo basi liribe aliwonse. Ndizo zonse. Mukuona? Zedi. Chipembedzo chake ndi chovunda. Inde, bwana.

359 Ndi nthawi yoti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, posachedwapa, chitsegulidwe. Ndipo pamene ilo litero, oh, mai, ilo litha! Mkwatibwi wapita kale, iye wachita kale. . . Mfumukazi yapita kale kukatenga malo Ake; Iye wakwatiwa tsopano, kwa Mfumu, pamene izi zikuchitika. Ndipo otsalira a Israeli asindikizidwa ndipo akonzeka kuti azipita, ndiyeno chirengedwe chipita. Oh, ndi nthawi yotani!

360 Zindikirani ndime yotsiriza ya Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, chikutsegulidwa. Iwo amene anaseka pa kulalikira kwa Mawu, kwa Mawu otsimikiziridwa a Mulungu wamoyo; pamene aneneri amenewo anali atayima pamenepo ndi kumachita zodabwitsa, kutseka dzuwa, ndi china chirichonse, ndi monse mpaka mmusi kudutsa mu m'badwo. Mwaona, "Iwo analirira kwa mathanthwe ndi mapiri kuti ziwabise iwo," mwaona, kuti ziwabise iwo kwa Mawu omwe iwo anawaseka, chifukwa iwo anamuwona Iye akubwera. "Tibiseni ife kwa mkwiyo wa Mwanawankhosa." Iye ndi Mawu. Mukuona? Iwo anali atawaseka Mawu. Ndipo apa Mawu anali, mthupi. Ndipo iwo anali atawasereula Iwo; anawaseka iwo, ankawaserewula iwo. Ndipo Mawu osandulika thupi anali atatulukira!

361 Ndi chifukwa chiyani iwo sanalape? Iwo sakanakhoza kutero. Iwo anali patali kwambiri, nthawi imeneyo. Chotero, iwo ankadziwa chimenecho, chirango. Iwo anawamva Iwo. Iwo anali atakhala mmisonkhano monga chonchi ndipo ankadziwa za Iwo. Ndipo iwo ankadziwa kuti zinthu za aneneri amenewo, zomwe zinali zitanenedweratu, zinali zikuwayang'ana iwo mu nkhope mwawo momwe, chinthu chimene iwo anali atachikana. Iwo anali atakana chifundo kwa nthawi yotsiriza.

362 Ndipo pamene iwe ukana chifundo, palibe kanthu kamatsalira koma chiweruzo. Pamene iwe ukana chifundo; tangoganizani za zimenezo.

363 Ndipo iwo anali pamenepo. Iwo analibe malo oti apiteko, opanda kothawira. Ndipo Baibulo linanena apa, "Iwo anayitanira . . . Analirira kwa matanthwe ndi mapiri, kuti, 'Gwerani pa ife, ndipo mutibise ife kwa—kwa nkhope ya . . . ndi mkwiyo wa Mwanawankhosa.'" Iwo anayesera kulapa, koma Mwanawankhosa anali atabwera kudzatenga Ake Omwe, mwaona. Ndipo iwo analirira kwa matanthwe ndi mapiri. Anapemphera, koma mapemphero anali mochedwa kwambiri.

364 M'bale wanga, mlongo wanga, ubwino ndi zifundo za Mulungu, zinatambasulidwa kwa anthu. Pamene, Israeli anachititsidwa khungu kwa izi, kwa apa, basi pafupifupi zaka thuu sauzande, kuti atipatse ife mwayi woti tilape. Kodi inu mwachikana chifundo chimenecho? Kodi inu mwatero? Kodi mwachikana Icho?

365 Ndinu ndani, mulimonse? Nanga inu munachokera kuti? Ndipo kodi inu mukupita kuti? Inu simungakhoze kumufunsa dokotala, inu simungakhoze kumufunsa aliyense mdziko, ndipo palibe bukhu limene inu mungakhoze kuwerenga, lomwe lingakhoze kukuwuzani yemwe inu muli, kumene inu munachokera, ndi komwe inu mukupita, koma Bukhu ili.

366 Tsopano, inu mukudziwa, popanda inu kukhala nawo Magazi a Mwanawankhosa kuti achite mmalo mwanu, inu mukuwona komwe inu mwalunjika. Kotero, ngati—ngati Mulungu anakuchitirani icho, chinthu chaching'ono kwambiri chomwe ife tikanakhoza kuchita chikanakhala kulandira zomwe Iye anachita. Ndizo zonse zomwe Iye anatipempha ife kuti tizichita.

367 Ndipo pa maziko a izi, ngati ine ndingapitirire, Ine ndiyenera kubwera mpaka mu Mliri umenewo, zonse izo, ulaliki wa usiku wa mawa. Ndipo tsopano ine sindingakhoze kuchita zimenezo, sindingapitirire mulimonse. Ine ndalemba izo pansi apa, mtanda, "uyimire apa," mwaona. Kotero, ndiye, ine—ine ndiyenera kuyembekezera mpaka mawa.

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha.

368 Ngati iwe sunatero, mzanga wofunika, sunatero—sunalandire chikondi cha Mulungu uyu yemwe ine ndikumukamba! Ngati iwe sunatero . . . Mvetserani kwa izi mwatcheru tsopano. Ngati iwe sunalandire chikondi Chake ndi chifundo, iwe udzayenera kudzaima pa ziweruzo Zake ndi mkwiyo.

369 Tsopano, inu, usikuuno, muli pa malo omwewo pamene Adamu ndi Eva anali mmunda wa Edeni. Inu muli nawo ufulu. Ndinu mfulu wa kusankha kwanu. Inu mukhoza kupita ku Mtengo wa Moyo, kapena inu mukhoza kutenga dongosolo la

chiweruzo. Koma, lero, pamene inu mudakali woganiza bwino, mmalingaliro anu olondola, ndipo ndinu athanzi mokwanira kuti—kuwuka ndi kuvomereza izo, bwanji inu osachita izo ngati inu simunachitepo izo.

370 Kodi alipo anthu amenewo muno omwe, panobe, sanachitepo izo? Ngati izo ziri chomwecho, mungangokweza mmwamba dzanja lanu? Ndikuti, "Mundipempherere ine, M'bale Branham. Ine tsopano ndikufuna kuchita zimenezo. Ine sindikufuna kuti izi zidzabwere." Tsopano kumbukirani, amzanga . . . Mulungu akudalitseni inu. Izo nzabwino. Ine ndiri . . .

371 Awa si malingaliro anga a Ichi. Ine—ine . . . Izi si zomwe ine ndakhala ndikuganiza; izi zonse palimodzi kukhala zochokera kwa ine. Kotero mundithandize ine, Mzimu Woyera ukudziwa zimenezo. Ndipo inu mudikirire, ngati Ambuye alola, mawa usiku, Ine ndikufuna ndidzakuwonetseni inu chinsinsi chomwe chakhala chikudutsa nthawi yonseyi, momwe muno mu msonkhano uno. Ine ndikukayikira kwambiri ngati inu munachiwonapo icho kapena ayi, mwaona, chomwe—chomwe chakhala chikuchitika. Icho chakhala chiri chinachake chomwe chakhala chitayikidwa pomwe apa pamaso panu. Ndipo ine ndakhala ndikuchiyang'ana, usiku uliwonse, ichi, kuti icho chiwuke, kuti winawake anene kuti, "Ine ndachiwona icho." Mukuona?

372 Musati muchikankhire Icho kutali, chonde, ine ndikukupemphani inu; ngati simuli Mkhristu, ngati inu—inu simuli pansi pa Magazi, ngati sindinu wobadwa kachiwiri, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera.

373 Ngati simunapangepo kuvomereza kwa pagulu kwa—kwa Yesu Khristu, pa kubatizidwa mu Dzina Lake, kuchitira umboni imfa Yake, kuyikidwa mmanda ndi chiwukitsiro, kuti inu mwavomereza iyo, madzi ali okonzeka. Iwo akuyembekezera. Mikanjo imaperekedwa muno, ndipo chirichonse ndi chokonzeka.

374 Khristu akuyima wokonzeka, ndi nkono wotambasulidwa, kuti akulandireni inu. Mu ora limodzi kuchokera pano, chifundo chimenecho chikhoza kusatambasuliridwa kwa inu. Inu mukhoza kuchikankhira icho kutali kwa nthawi yotsiriza; icho sichidzakhudzanso konse mtima wanu. Pamene mungakhoze, pamene mungakhoze, bwanji inu osachita chimenecho? Tsopano pamene . . .

375 Ine ndikudziwa njira yanthawi zonse, yachizolowezi, imakhala kuwabweretsa anthu kuno ku guwa. Ife timachita zimenezo, ndipo ndizo zabwino mwangwiro. Pa nthawi ino, ife tadzazana kwambiri muno, pozungulira guwa pomwe, mpaka ine sindingakhoze kuchita zimenezo.

376 Koma ndikufuna kunena ichi. Mu tsiku la atumwi, iwo anati, "Onse omwe anakhulupirira anabatizidwa." Mukuona?

Basi ngati inu mungathe, kwenikweni, pansi mu mtima mwanu! Apa pali izo zonse. Izo si—izo si kutengeka, ngakhale kutengeka kumatsagana nazo izo. Basi monga ngati zimene ine ndinanena, kusuta ndi kumwa si tchimo; izo ndi zotsatira za tchimo; izo zimasonyeza kuti ndiwe sumakhulupirira. Mukuona? Koma pamene ukukhulupirira moona mu mtima mwako, ndipo iwe ukudziwa kuti pa maziko a, pomwepo pamene inu wakhalapo, iwe ukuvomereza izo ndi mtima wako wonse, chinachake chichitika pomwe apo. Icho chichitika.

377 Kenako iwe ukhoza kuyima monga mboni kwa icho, kuti chinachake chachitika. Kenako nkuyenda kupita ku madzi, kumati, "Ine ndikufuna kuwonetsera kwa osonkhana, ine ndikufuna kutsimikizira, ine ndikufuna kupanga umboni wanga kuyima, kuti ine ndidzatenga malo anga ndi Mkwatibwi. Ine ndayima apa tsopano kuti ndibatizidwe."

378 Ine ndikudziwa kuti alipo akazi ambiri mu dziko usikuuno, akazi abwino, koma ndine wosungulumwa moyipa kuti ndimuwone mmodzi. Alipo mmodzi wa iwo yemwe ali mkazi wanga. Iye amapita kunyumba ndi ine. Iye sanali mkazi wanga, kuyamba ndi kuyamba; koma momwe iye anadzakhalira mkazi wanga, iye anatenga dzina langa.

379 Iye akubwera. Alipo akazi ambiri, mipingo, mdziko, koma Iye akubwerera Mkazi Wake. Iye akutchedwa ndi Dzina Lake. "Iwo omwe ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi ndi Iye." Ife timalowa chotani mwa Ilo? "Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzilo."

380 Tsopano pamene ife tikupemphera, inu muzipemphera, nanunso. Mkati kapena kunja, alipo magulu aakulu a anthu mu zipinda, kunja, ayimirira pozungulira, kunja mmisewu. Koma tsopano pamene—pamene inu muli. . . Ife sitingakhoze kukuyitanirani inu kuno ku guwa. Koma, mtima wanuwo, upangeni iwo kukhala guwa. Ndipo mu mtima mwanu momwe, muziti, "Ambuye Yesu, ine ndikukhulupirira Izi. Ine ndinayima kunja kuno mu mpweya wa usiku uno. Ine ndakhala ndikubanika, mchipinda chaching'ono chino. Ine ndakhala muno, pakati pa anthu awa. Ine—ine—ine—ine—ine sindikufuna kukhala. . . ine sindingakhoze kuphonya; ine sindingakhoze kukwanitsa izo."

381 Chirichonse, monga ine ndinakuuzirani inu usiku watha, ndipo, kotero ndithandizeni ine, Ambuye akudziwa kuti ine ndikunena Choonadi. "Ine sindikunama ayi," monga Paulo ananenera. Masomphenya aja, kapena chirichonse chimene chinali; ine ndinayima kumeneko, ndinayang'ana, ndi kuwagwira anthu amenewo omwe anapita kale, zenizeni basi monga ine ndayimira pomwe apa. Musachiphonye icho, m'bale wanga wosauka kapena mlongo; musachite zimenezo. Ine ndikudziwa kuti inu mwamvapo kulalikira, inu mwamvapo

izi, *izo*, ndi nkhani, zonse izo. Koma mulole. . . Ingomvetserani. Kwa ine, ichi ndi. . . Ine ndikudziwa kuti icho ndi Choonadi, mwaona. Inu basi. . . Ine—ine—ine sindingakhoze kuzipanga izo kumveka bwinoko mulimonse, mwaona. Musaziphonye zimenezo. Zonsezo ndi zanu.

Tsopano tiyeni tipemphere.

382 Ambuye Yesu, apa patsogolo pa ine pali bokosi la mipango yomwe ikuyimira anthu odwala. Pamene ine ndikuyipempherera iyo, ndikuyika manja pa iyo, monga Baibulo linati, "Iwo ankatenga kuchokera mthupi la Paulo, mipango ndi zovala, mizimu yoyipa inkatuluka mwa anthu, ndipo zizindikiro zazikulu zinkachitika."

383 Chifukwa, iwo anamuwona Paulo, yemwe iwo ankadziwa kuti Mzimu wa Mulungu unali mwa iye. Iwo ankadziwa kuti iye anali—iye anali munthu wachirendo, mwa, zinthu zomwe iye ankaziyankhula, zokhudza Mawu. Iye ankakhoza kupita kukatenga mawu akale a Chihebri a mpingo wa Chihebri, ndi kuwabweretsa iwo ku moyo, ndi kudzawayika iwo mwa Khristu. Iwo ankadziwa kuti Mulungu anali mwa munthu ameneyo. Kenako iwo ankawona Mulungu akuchita ntchito zachirendo ndi zamphamvu mwa iye, kulosera zinthu ndipo izo nkudzachitika mwanjira imeneyo, ndipo iwo ankadziwa kuti iye anali wantchito wa Mulungu.

384 Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mulemekeze anthu awa chifukwa cha kulemekeza kwawo kwa Mawu, ndipo achiritseni iwo chifukwa cha Yesu. Kuchokera muno mwa omvetsera, Ambuye, mwakhala anthu, chimodzimodzi monga zinakhalira kwa iwo omwe ankamvetsera kwa mtumwi Petro pa Tsiku la Pentekoste. Momwe iye anabwerera mu Mawu, ndi kukatenga Mawu! Ndipo iye anati, "Yoweli anati, mmasiku otsiriza zinthu izi zidzachitika. Ndipo Ichi ndi chimenecho." Ndipo firii sauzande anakhulupirira Icho, ndipo anabatizidwa.

385 Ndipo, Atate, lero ife tikuyima pano mwa chisomo Chanu. Ndipo si chifukwa chakuti—kuti iwo ndi anthu apadera, koma ndi chifukwa chakuti (monga ngati tsiku la mkango, kapena la ng'ombe, kapena la munthu) iyi ndi nthawi ya mphungu. Ndiko kudzoza kwa orali. Ndi nthawi yomwe ife tikukhalamo. Ndi kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera pa nthawi iyi, kudzatsimikizira kuti Yesu si wakufa. Zinthu zomwe Iye ananena kuti Iye akanadzachita basi Kuwala kwa kumadzulo kusanazime, ndipo pano ife takhala tikumuwona Iye akuchita zimenezo, pomwe pano kutsika mkanjira. Ife tawuwona Iwo ukubwera uko mu kufufuza kwa sayansi ndipo anadzajambulitsa chithunzi Chake; Lawi la Moto lalikulu Yemwe anatsogolera ana a Israeli; Yemwe anakumana naye Paulo pa msewu.

386 Ndipo ife tikudziwa, Lawi la Moto lomweli lomwe linamutsogolera Mose kumusi uko mu chipululu, mwa Lawi la Moto lomwelo iye analemba Mabuku angapo a Baibulo, pakuti iye anali wodzozedwa ndi Mawu.

387 Lawi la Moto lomweli litabwera pa Paulo, akupita ku Damasiko, iye analemba Mabuku ochuluka a Baibulo, otchedwa Mawu a Mulungu.

388 Ndipo tsopano, Ambuye, Lawi la Moto lomwelo, mwa umboni wa chitsimikizo cha Mawu, ndi mwa kufufuza kwasayansi, ife tikuliwona Ilo pano likuwulula Mawu a Ambuye.

389 Mulungu, mulole kuti anthu adzutsidwe mwaliwiro, Ambuye, mwamsanga! Iwo omwe ali nawo maina awo atalembedwa pa Bukhu la Moyo; pamene Ichi chiwalira modutsa njira yawo, lolani kuti iwo awone. Monga mkazi wamng'ono, wa mbiri-yoyipa pa chitsime tsiku lija, iye anazindikira mwamsanga, ndipo iye anadziwa kuti Ilo linali Lemba.

390 Ndipo tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti onse amene ati akulandireni Inu pa nthawi ino, mmitima mwawo, akhazikitse icho kwa nthawizonse, pa ora ili, kuti iwo athana nalo tchimo; kuti adzuke ndi kupanga kukonzekera tsopano kwa kuvomereza kwa pagulu, kwa ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo awo; kuwonetsera kuti iwo akukhulupirira kuti Mulungu wawakhululukira iwo, ndipo iwo akutenga Dzina la Yesu Khristu.

391 Kenako, Atate, mudzatsanulire Mzimu Woyera, wa Mafuta, pa iwo, kuti iwo akakhoze kuyikidwa mu utumiki wa Ambuye Mulungu, kuti iwo akakhoze kukhala ogwira ntchito mu tsiku lotsiriza ili, loyipa, pakuti ife tikuzindikira kuti ife tiri nayo nthawi yayifupi. Ndipo Mpingo ukhoza kupita nthawi iliyonse.

392 Mwanawankhosa akhoza, pa nthawi iliyonse, kuchoka pa malo wopatulika kumwamba Kumeneko, kapena Mpandowachifumu wa nsembe, kutulukira kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu kumene nsembeyo ikukhala, ndiyeno izo zidzakhala zitatha; apo sipadzakhalanso ziyembekezo kwa dziko; ilo latsirizika. Ndiye ilo lidzalowa mu zokhumudwitsa, za kudzidzimutsa kwakukulu kwa zivomezi, ndi—ndi kugwedezeka kwakukulu konga kunalipo pa chiwukitsiro. Ndipo—ndipo, a—a . . .

393 Monga Khristu anawuka kuchokera ku manda, pamene oyera mtima anawuka, chinthu chomwecho chidzachitika. Ambuye, izo zikhoza kuchitika pa miniti iliyonse. Ife tikuyembekezera tsiku ilo la chisangalalo kuti lifike.

394 Atengereni ana Anu pansi pa nkono Wanu, Atate, tsopano. Muwakokere ana ankhosa aang'ono Anu ku chifuwa Chanu. Perekani izi. Ndipo muziwadyetsa iwo pa Mawu, mpaka iwo

atakhala mu mphamvu ya utumiki. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, Ambuye. Yankhani pemphero ili.

395 Inu munanena, Atate, uko mu Marko, mutu wa 11, "Pamene mupemphera, mukaima kumapemphera, mukhulupirire kuti inu mwalandira zomwe inu mwapemphazo, ndipo inu mudzakhala nazo izo."

396 Ndipo ndi mtima wanga wonse kwa Iye yemwe wakhala akuwulula zinthu izi monse kudutsa mu zakazi, ndi Zisindikizo izi apa mu sabata yathayi; ine ndikukukhulupirirani Inu, Ambuye Mulungu, kuti ndi oralo, layandikira tsopano, kuyandikira kuposa momwe ife tikuganizira kwenikweni, la kudza Kwanu.

397 Chonde mulole kuti pemphero langa liyankhidwe. Ndipo mulole kuti mwana aliyense woyitanidwa wa Mulungu, yemwe akumvetsera patali kuchokera pano, kapena yemwe tepi iyi iti idzamukhudze, mulole kuti pa nthawi imeneyo. . . Ine ndikuwatengera iwo ku Ufumu wa Mulungu, pamaziko odziwa kuti awa ndi Mawu omwe akuwululidwa. Mulole kuti Kuwala kwa kumadzulo kuwale, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu. Ameni.

398 Tsopano, nonse, mkati kapena kunja, omwe mukukhulupirira, ndipo simunapangepo kwanu—kuvomereza kwanu kwa pagulu, kuti inu mwathana nalo tchimo; ndipo inu—inu mukufuna zifundo za Mulungu, ndipo inu mwazilandira izo mwa Yesu Khristu. Dziwe. . . Iwo akhala okonzeka kubatiza aliyense yemwe akufuna kubatizidwa, lero kapena mawa, pakali pano kapena nthawi iliyonse yomwe ingakhale.

399 Kodi inu mwasangalala nacho Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Inu mwaona kumene Icho chatsegulidwa tsopano? ["Ameni."] Kodi inu mwachikhulupirira Icho? ["Ameni."]

400 Izo zinanenedwa kuti, "Ndani wakhulupirira uthenga wathu? Ndipo ndi kwa ndani yemwe nkono wa Ambuye wawululidwirako?" Mukuona? Mukhulupirire uthenga, ndiye nkono wa Ambuye uwululidwa. Nkono, Mawu a Mulungu, awululidwa.

401 Ambuye akalola tsopano, mawa mmawa, ine ndidzayesetsa mwakukhoza kwanga kuyankha mafunso amenewo. Ine ndidzakhala mwinamwake usiku wonse, ndipo, kapena kwakukulu kwa iwo, mu pemphero, pa iwo. Ine ndikumatenga pafupifupi ora limodzi mpaka atatu usiku. Ine sindinapite kukagona konse usiku wathawu mpaka kufika wani koloko, ndipo pa firii koloko ine ndinali mu kuwerenga. Mukuona? Mukuona?

402 Ine ndiyenera kudzayankhira pa izi. Uko nkulondola. Ife tiri pafupi kwambiri kwa chirichonse, kupusa kulikonse, kapena kupenekera kulikonse, kapena kukhulupirira kwa

theka. Ine ndiyenera kuziwona izo, poyamba. Ndipo kenako, pamene ine ndaziwona izo, izo ziyenera kukhala mu Mawu, nazonso. Ndipo mpakana apa, mwa chisomo cha Mulungu, izo ziri mwangwiro. Ine ndazitenga izo kuchokera njira yonse nkuzidutsitsa, inu mukudziwa zimenezo, ndipo ndi—zalumikizana pamodzi kumene.

403 Izo ziyenera kukhala PAKUTI ATERO AMBUYE. Chifukwa, osati kokha pamene zinena Izo kuchokera pakuzidziwa ine Izo, inemwini, koma Mawu a Ambuye ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo apa pali Mawu, kutenga zomwe Iye wandipatsa ine, ndi kuzilumikiza Izo pamodzi ndi kukuwonetsani inu. Kotero inu mukudziwa, inueni, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona?

404 Apa pali Mawu, akunena chomwecho. Ndiponso vumbulutso lomwe Iye akundipatsa ine, lomwe liri losiyana kwa zomwe aliyense wa ife anayamba waganizapo konse; bwanji, losiyana ndi zomwe ine ndinkaganiza, chifukwa ine sindinalowepo mwa Iwo monga chomwecho. Koma tsopano, ife tikupeza kuti, izo zikukomana pamodzi kumene. Ndipo Iwo ndi chiyani? Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Ndizo ndendende. Awa akhala ali malo otsegulidwa, atakhala pamenepo, kufikira ora lino, ndiyeno Ambuye abwera ndipo adzakankhiramo Iwo mkati momwe monga chomwecho. Kotero, inu mukuona, apo Izo ziri. Izi, ndi—ndi Ambuye. Oh, ine ndimamukonda Iye! Ine ndimamukonda Iye ndi mtima wanga wonse.

405 Tsopano kumbukirani, inu. . .Ife sitinakwanitse kubwera ku guwa. Angapo anakweza manja awo mmwamba. Tsopano, mwaona, ndi chinthu cha aliyense payekha, ndi inu. Ndicho chirichonse chimene inu mukufuna kuchita. Mukuona?

406 Ora layandikira pafupi kwambiri, inu muyenera kukanikiza molimba momwe inu mungathere, osati kumachita kukokedwa. Mwaona, kumangokanikiza, kuyesetsa kulowa mkati, "Ambuye, musandisiye ine panja. Musandisiye ine panja, Ambuye. Zitseko zikutsekedwa; ngati ine nditangolowa mkati!" Mukuona?

407 Mulungu adzatseka chitseko tsiku lina. Iye anatero mu tsiku la Nowa, ndipo iwo anamenya pa khomo. [M'bale Branham akugogoda pa guwa kangapo—Mkonzi]. Nkulondola uko?

408 Tsopano kumbukirani, Baibulo linanena, kuti, "Mu ulonda wachisanu ndi chiwiri." Nkulondola uko? Ena anagona mu ulonda woyamba, wachiwiri, wachitatu, wachinayi, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, wachisanu ndi chiwiri. Koma, mu ulonda wachisanu ndi chiwiri, kunadzabwera kulengeza, kufuula, "Mkwati akubwera! Tulukani mukakumane naye Iye."

409 Anamwali ogona anati, "Ndikuti, ndikuwafuna ena a Mafuta amenewo tsopano."

410 Mkwatibwi anati, “Ine ndangokhala nawo ondikwanira ndekha; ndangokhala nawo okwanira. Ngati inu mukuwafuna Iwo, inu mupite mukapemphere Iwo uko.”

411 Kodi inu simukumuwona namwali wogona tsopano? Tayang’anani pa a Episcopalia, Apresbateria, Achilutera, ndi chirichonse, akuyesetsa kutero. Ndipo vuto lake ndi lakuti, mmalo moyesetsa kuti apeze Mzimu Woyera, iwo akuyesetsa kuti aziyankhula mmalirime.

412 Ndipo ambiri a iwo akumayankhula mmalirime, ndipo akumachita manyazi kubwera ku mpingo uno kuti adzapemphereredwe; amafuna kuti ine ndipite kunyumba kwawo ndi kukawapempherera iwo. Inu mumawutcha umenewo Mzimu Woyera? Uko ndi kuyankhula mmalirime, koma osati Mzimu Woyera. Mukuona?

413 Tsopano, ine ndimakhulupirira kuti Mzimu Woyera umayankhula mmalirime. Inu mukudziwa kuti ine ndimakhulupirira zimenezo, mwaona. Koma pali chokopera kwa Icho, nachonso. Inde, bwana. A—zipatso za Mzimu, ndi zomwe zimatsimikizira chomwe Iwo uli. Zipatso za mtengo zimatsimikizira mtundu wa mtengo umene iwo uli. Osati khungwa; chipatso!

414 Tsopano zindikirani, ndiye, pamene iye anabwera, ilo—ora lotsiriza lija. Ndipo apo, pamene iwo anabwera mkati, ndiye iwo anapita ndipo anakanena kuti, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndiri nawo Iwo tsopano. Ine ndikukhulupirira ine ndiri nawo Iwo. Eya, ife tikuwulandira Iwo.”

415 Ine—ine—ine kulibwino ndisanene izi, mwaona, chifukwa izo zikhoza kuyambitsa chisokonezo. Pamene ine ndinanena tsiku lina, za Mkwatulo, momwe Iwo uti udzabwerere, ine—ine... Tsopano, ngati inu mukuti inu—inu muzitenga izo, chabwino. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Yang’anani. Yang’anani. Chabwino, izo ziri kwa inu.

416 Pamene namwali wogona, mwaona, yemwe ankaganiza kuti iye anali atapemphera mokwanira, kuti abwerere, Mkwatibwi anali atapita kale. Iwo unapita, ndipo iye sanadziwe izo; monga wakuba mu usiku. Ndiye iwo anayamba kugogoda pa zitseko. Ndipo kodi chinachitika ndi chiyani? Ndi chiyani chomwe chinachitika? Iwo anaponyedwa mu nthawi ya Chisautso. Baibulo linati, “Uko kudzakhala kulira, ndi kubuula, ndi kukukuta kwa mano.” Nkulondola uko?

417 Izo zidzachitika liti, m’bale, mlongo, ine sindikudziwa. Koma, ine—ine, ine, izo zikhoza kungokhala ine pano, tsopano, mwaona. Izi, izi ndi zomwe...Ili ndi lingaliro langa. Mukuona? Ine—ine—ine ndikukhulupirira kuti ziri pafupi kwambiri, ine—ndiri...Tsiku lirilonse ine—ine ndikufuna... Ine ndikungoyesetsa kuyenda mofewa momwe ine ndingathere.

Mukuona? Ndipo tsopano pamene, inu mukudziwa, pamene a. . .

418 Chinachake chinachitika lero, ndipo ine ndinawona chinachake chikubwera chokwera. Ine—ine basi. . .Ine sindinakhoze kukoka mpweya wanga nkomwe, mwaona. Apo Iye anali, atayima pamenepo, Kuwala kwakung'ono kuja kutayima pomwe apo. Ndipo apa Iko kunali. Ine ndikudziwa kuti ndicho Choonadi.

419 Ine ndinaganiza, "O Mulungu, ine sindingakhoze kunena zimenezo. Ine—ine sindingakhoze kunena izo. Ine sindingakhoze." Ine ndinangotuluka mchipindamo, kupita kunja, ndinakayendayenda. M'bale, ine ndinaganiza, "Mai! Ndingachite chiyani ine? Oh!" Mukuona? Ndipo ine—ine ndiyenera kupita kukawedza, kapena chinachake, kapena ine. . .Mnyamata, iwe ukanati. . .iwe. . .ine sindingakhoze kukuuzani inu. Mukuona?

420 Kotero, ife tiri nayo nthawi yabwino. Sichoncho ife? Ambuye alemekezeke! Ameni! Mukuona? Ife tiri mu—ife tiri mu nthawi yopambana, mwaona, pakuti mtima wanga wasefukira nacho chisangalalo ndi chimwemwe.

421 Koma pamene ine ndiganiza za dziko lino ndi masauzande omwe ine ndikuwadziwa amene atayika, ophimbidwa ndi mthunzi-wakuda, hum, ndiye mtima wako umangowukha magazi. "Iwe ungachite chiyani? Iwe ungachite chiyani?" Iwe umangomverera Mzimu Woyera ukulira mofuula, mu mtima wako. Monga momwe zinakhalira mwa Ambuye wathu, pamene Iye anayang'ana pa Yerusalemu, anthu Ake Omwe, mwaona, anati, "Yerusalemu, Yerusalemu, Ine ndakufungatira kochuluka bwanji iwe, monga thadzi likanachitira kwa mwanapiye wake, koma iwe sunafune ayi." Iwe umangowumverera Mzimu Woyera ukuti, "Ndi kangati Ine ndakusonkhanitsa iwe, mwaona, koma iwe sunafune." Mukuona?

422 Ndife, ife tiri pomwe apa pa chinachake, amzanga. Chirichonse chomwe icho chiri, Mulungu akudziwa. Palibe aliyense, palibe aliyense akudziwa pamene izo ziti zidzachitike. Ndicho chinsinsi. Palibe aliyense akudziwa pamene izo ziti zidzachitike.

423 Koma Yesu anatiwuza ife, "Pamene inu mudzawona zinthu izi, zinthu zonse izi." Monga ngati zomwe ine ndinapitamo, kufanizitsa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, kwa zomwe Iye ananena mu Mateyu 24. Tsopano kumbukirani zomwe Iye ananena, "Pamene inu mudzawona zinthu izi zikubwera, zikadzayamba kufika pokwaniritsidwa, ndiye kuti nthawi ili pakhomo." Yang'anani ndime yotsatira kumene, ya 30—ndime za 30 ndi ya 31 ndi kumapitirira mpaka mmusi, ya 32, ndi ya 33.

424 Iye anati, “Ndipo Iye adzatumiza angelo Ake ku ngodya zinayi za mmiyamba, ku mphepo zinayi, kukasonkhanitsa Osankhidwa Ake.” Nkulondola uko?

Anati, “Tsopano phunzirani a. . . ”

425 Tsopano kumbukirani, Iye anaimira pomwe apo. Iye sanapitirire nkomwe, atamaliza Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chimenecho. Iye sananene kalikonse kokhudza Chachisanu Ndi Chiwiri. Iye ananena Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinayi, Chachisanu, ndi Chachisanu Ndi Chimodzi. Koma Iye anayimira pomwepo, sanatchule chirichonse chokhudza Icho.

426 Penyani chinthu chotsatira chimene Iye ananena, “Tsopano phunzirani fanizo.” Mukuona? Kenako Iye akuyamba pa fanizo. Iye anati, “Zinthu izi zidzachitika.”

427 Iye akuyankha mafunso atatu amenewo. “Chidzakhala chiyani. . .zizindikiro izi? Ndipo chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu? Chidzakhala chiyani chizindikiro, cha mapeto a dziko lapansi?”

428 Ndipo Chachisanu Ndi Chimodzi Icho, pamenepo, chinali kutha kwa dziko lapansi. Ndi kuwomba kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri. . . “Anakweza mmwamba manja, ndipo analumbira pa Iye wokhala moyo kwa nthawi za nthawi, kuti sipadzakhalanso nthawi.” Dziko lapansi likubala lina latsopano. Izo zatha.

429 Ndipo apa ife tiri, pomwe apa pa khomo. Oh, ine ndikunjenjemera. “Ndipo kodi ine ndichite chiyani, Ambuye? Chiyani—ndi chiyani chinanso chomwe ine ndingakhoze kuchita?” Mukuona? Ndipo, ndiye, ingoganizani za kuwawona malo amenewo ndi anthu ofunikira amenewo! Ine ndinaima pamenepo, ndikudziyang’ana ndekha. Ndipo ndinaganiza, “O Mulungu, bwanji, iwo—iwo sangakhoze kuchiphonya ichi. Ine—ine—ine ndiyenera kuwakankha iwo. Ine ndiyenera kungofika mu chigulu ndi kuwatenga iwo, ndi kuwakankha.” Iwe sungakhoze kuchita zimenezo. Iwe. . .

430 “Ndipo palibe munthu angakhoze kubwera pokhapokha Atate Anga atamukoka iye.” Koma apa pali chitonthozo chimodzi chomwe ife tiri nacho, “Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzabwera.”

431 Koma ena onsewo, ndi mabungwe amenewo, akuwadalira iwo monga chomwecho, mwaona. “Ndipo iye anawanyenga onse omwe akukhala pa, akukhala pa dziko lapansi, amene maina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa limenelo, wophedwa kuyambira makhazikitsidwe a dziko lapansi.” Oh, mai! Kotero, inu mukuona, icho ndi chinthu chomvetsa chisoni.

[432] Chinthu chokhacho chomwe inu mungakhoze kuchita ndicho basi—basi—basi—kungokhala molondola ndi Mawu. Kumangoyang'ana chirichonse chimene Iye anena kuti muchite, ndiyeno nkumachita chimenecho. Mukuona? Chirichonse chimene Iye anena kuti muchite; nkumachita chimenecho.

[433] Ndipo iwe nkumayang'ana kunja uko, ndi kuti, "Oh, mai! Iwo amachita *izi*, ndiye . . . Oh!" Ndicho basi . . .

[434] Inu simumazindikira kufinya kwake! Tsopano ine ndikufuna kunena ichi. Ine ndikuganiza kuti matepi azimitsidwa. Anthu ambiri amanena kuti, "M'bale Branham, ali ndi utumiki wa mtundu umenewo . . . " (Ine ndimayenera kuyang'ana, chifukwa anthu amangotenga matepi amenewo ndi kumangoyesera kuwatengera iwo mzidutswa, inu mukudziwa.) Kotero pamene iwo anena kuti, "M'bale Branham, ife tikukhumba tikanakhala nawo utumiki," inu simukudziwa chomwe inu mukunena. Inu, moona mtima, inu simukudziwa chimene chimapita nawo iwo, m'bale, mlongo. Oh, mai! Ndi udindo, pamene uli nawo anthu amene amazendewera kwa zomwe iwe umanena! Kumbukirani, ngati iwe uwauza iwo zolakwika, Mulungu adzafuna magazi awo mmanja ako. Ndiye, iwe ukaganiza za zimenezo. Icho ndi chinthu chowopsya.

[435] Kotero, muzikhala okonda. Muzimukonda Yesu ndi mtima wanu wonse. Basi kuma- . . . Muzikhala ophweka. Musamayesere konse—kuyesera kuchiringalira chirichonse. Muzingokhala ophweka, pamaso pa Mulungu. Chifukwa, mochuluka momwe inu mukuyesetsa kulingalira, inu mumapita kutali kwambiri ndi Iye. Mukuona? Muzingomukhulupirira Iye mophweka.

Kumati, "Tsopano, chabwino, kodi Iye adzabwera liti?"

[436] Ngati Iye abwera lero, ziribwino. Ngati Iye adzabwera zaka twente kuchokera tsopano, ziri bwinobe. Ine ndizipitirira basi momwe ine ndikupitira tsopano, kumutsatira Iye. "Ambuye, ngati Inu mungandigwiritse ine ntchito kulikonse, ine ndiri pano, Ambuye." Ngati ziri zaka handiredi kuchokera lero, ngati zidzukulu-zidzukulu-zidzukulu-zidzukulu zidzakhalebe moyo kudzaliwona ilo likubwera, mulole . . . "Ambuye, ine sindikudziwa kuti izo zidzachitika liti, koma mundilole ine kuti ndizingoyenda molondola lero, basi ndi Inu." Mukuona? Ine—ine ndikufuna . . . Chifukwa, ine—ine ndidzawuka pa tsiku limenelo, chimodzimodzi basi monga ine ndinakhalira ndi kugona kwapang'ono kwinakwake.

[437] Ndikubwera mmusi kumeneko, nyumba yachifumu yaulemelero iyo kutsidyako, Ufumu wa Mulungu uwo kumeneko, kumene onse okalamba adzakhala achinyamata, kumene mikanjo yoyera yavekedwa kale! Amuna ndi akazi atasintha, mu kukongola, luso lomwe la—la m—mwamuna wokongola ndi a—mkazi wokondeka! Atayima pamenepo mu kukongola konse ndi thunthu la mkazi wamng'ono ndi mwamuna wamng'ono,

atayima pamenepo! Ndipo sadzakhozanso kukalamba, sangakhoze kukhalanso ochimwa nkomwe, sikungakhale chirichonse cha nsanje, kapena udani, kapena chirichonse! Oh, mai!

438 Ine ndikuganiza kuti matepi azimitsidwa tsopano. Ndipo ine—ine ndangokhala nawo pafupifupi maminiti atatu kapena anayi. Ine ndikufuna ndikuyankhule ndi inu. Ziri bwino kutero? Tsopano, ichi ndi basi cha kwa munthu payekha, mwaona. Chifukwa, mawa, ine—ine . . . Lidzakhala lopambana kwambiri! Ine ndikuganiza kuti kulibwino ndingonena izo tsopano, mwaona, zomwe ine nditi ndinene. Ine . . . Izi ndi za ife tokha tsopano. Ine ndinali basi . . .

439 Inu mukudziwa, ine—ine ndiri naye mkazi yemwe ndimamukonda, ndipo ameneyo ndi Meda. Ndipo ine—ine sindikanati ndimukwatire iye nkomwe, chifukwa cha chikondi changa pa mkazi wanga woyamba. Ndipo komabe, mochuluka monga ine ndinkasamalira za iye, ine—ine sindikanamukwatira iye chikapanda Mulungu kundiuza ine kuti ndichite zimenezo. Ndipo inu mukuidziwa nkhani ya zimenezo; momwe iye anapitira kukapemphera, ndi momwe ine ndinachitira. Ndiyeno Iye anandiuza ine ndendende choti ndichite, ndikuti, "Pita, ukamukwatire iye," ndi nthawi yeniyeni yokachitira izo. Iye ndi mkazi wokondeka. Ndipo iye akundipempherera ine usikuuno. Ndipo kotero tsopano ndi eyiti koloko, kwathu, iye mwinamwake akupemphera tsopano.

440 Tsopano zindikirani. Tsiku lina iye ananena kwa ine, iye anati, "Bill," iye anati, "Ine ndikungofuna ndikufunse iwe funso lokhudza Kumwamba."

Ine ndinati, "Chabwino, Meda, ndi chiyani ilo?"

Iye anati, "Iwe ukudziwa kuti ine ndimakukonda iwe."

441 Ndipo ine ndinati, "Eya." Izo zinachitika izi zitangochitika kumene kuno.

Iye anati, "Iwe ukudziwa kuti Hope ankakukonda iwe, nayenso."

Ine ndinati, "Eya."

442 Ndipo iye anati, "Tsopano," iye anati, "Ine sindikuganiza kuti ndingakakhale wansanje," iye anati, "koma Hope anali." Ndipo iye anati, "Tsopano, pamene tikafike Kumwamba . . . Ndipo iwe unati iwe unakamuwona iye kumeneko."

443 Ine ndinati, "Iye anali kumeneko. Ine ndinamuwona iye. Ine ndinamuwona iye kawiri, kumeneko." Iye ali kumeneko. Iye akundiyembekezera ine kuti ndibwere. Chimodzimodzinso ali . . . Chimodzimodzinso ndi Sharon. Ine ndinamuwona iye, mofanana basi monga ine ndikupenyera pa inu. Ine ndinamuwona iye kumeneko. Ndipo ine ndinati . . .

444 Iye anati, "Chabwino, tsopano, pamene ife tikafika kumeneko," anati, "ndi uti ati akakhale mkazi wako?"

445 Ine ndinati, "Awiri nonse a inu. Uko sikukakhala aliyense, waona, komabe nonse a inu mungakakhale muli."

Iye anati, "Ine sindikutha kumvetsa zimenezo."

446 Ine ndinati, "Tsopano, wokondedwa, khala pansi, undisiye ine ndifotokoze chinachake kwa iwe." Ine ndinati, "Tsopano, ine ndikudziwa kuti iwe umandikonda ine, ndipo iwe ukudziwa momwe ine ndimakukondera iwe, ndi kulemekeza ndi ulemu. Tsopano, mwa chitsanzo, bwanji ngati nditavala, nkupita kumusi kwa mzinda; ndipo hule wina wamng'ono, wokongola kwenikweni, nkubwera ndi kudzandikumbatira ine, ndi kudzati, 'Oh, M'bale Branham, ine ndikutsimikiza ndimakukondani inu,' nkuyamba kuyika mikono yake mondizungulira ine ndi kumandikumbatira ine. Kodi iwe ungaganize chiyani?"

Iye anati, "Ine sindikuganiza kuti ndingazikonde zimenezo mwabwino kwambiri."

447 Ndipo ine ndinati, "Ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake. Kodi iwe...Kodi ndi ndani yemwe iwe ungamukonde kwambiri, ngati patati pakhale chiwonetsero, ine kapena Ambuye Yesu?" Tsopano, ilo ndi banja chabe, kuyankhulana.

448 Ndipo iye anati, "Ambuye Yesu." Anati, "Inde, Bill, mochuluka momwe ine ndimakukondera iwe, koma, ine ndisanati ndimusiye Iye, ine ndingakusiye kaye iwe."

449 Ine ndinati, "Zikomo iwe, wokondedwa. Ine ndiri wokondwa kukumva iwe ukunena izo tsopano." Ine ndinati, "Tsopano, nanga bwanji ngati mkazi wamng'ono yemweyo atabwera kwa Yesu ndi kudzaponyera mikono yake momukumbatira Iye, nkudzati, 'Yesu, ine ndimakukondani inu,' iwe ungaganize chiyani za zimenezo?"

Iye anati, "Ine ndingasangalale nazo izo."

450 Mwaona, izo zikusintha kuchokera ku filiyo kupita ku agapao. Mwaona, ndi Chikondi chapamwamba. Mukuona? Ndipo kulibeko chinthu choterocho chonga mwamuna ndi mkazi wake, monga...ndi kulera ana. Izo zonse zidzakhala zitatha, a—ziwalo zogonana zachikazi ndi zachimuna. Zofunitsana zonse zidzakhala...Iwo onse ndi ofanana, kumeneko. Mukuona? Uko kulibe chirichonse cha izo, nkomwe. Mwaona, uko kulibe zofunitsa kugonana nkomwe, ayi nkomwe. Mukuona? Iwe umangokhala basi...Inde, bwana. Tangoganizani za inueni wopanda zofunitsa kugonana. Chifukwa chomwe izo zinayikidwa mwa ife ndi chakuti tizichulukana mdziko lapansi, inu mwaona. Koma, Kumeneko, uko sikukakhala chirichonse Kumeneko. Uko sikukakhala ngakhale chofunitsa chachimuna kapena chachikazi. Ayi.

451 Koma thunthu la luso la Mulungu lidzakhala liripo. Ndiko kulondola ndendende. Koma ife mowona tikakhala enieni. Ayi—kopanda filiyo, nkomwe; zonse agapao. Mukuona? Chotero, mkazi akakhala wosaposa basi wokondedwa winawake yemwe ali—ali wako, ndipo iye . . . Inu mukakhala wa wina ndi mzake. Uko kulibe chinthu chonga . . . Ayi, ayi, uko kulibe ngakhale . . . Mwaona, gawo la filiyo silikakhalako nkomwe kumeneko. Mwaona, uko sikungakhale chirichonse chonga nsanje; kulibe chinthu chochitira nsanje. Sikukakhalako chinthu choterocho kumeneko. Inu simukadziwa nkomwe chinthu choterocho chonga icho. Mukuona? Ndi basi mwamuna wamng'ono wokondedwa ndi mkazi wamng'ono, kumakhala moyo.

Ndiyeno, nditatsiriza, iye anati, "Ine ndachiwona icho tsopano, Bill."

Ine ndinati, "Eya."

452 Ine ndikufuna ndikuuze iwe kanthu kakang'ono komwe kanachitika. Ili linali loto. Ine ndinali kugona. Ndipo ine sindinazinenepo izi pagulu mmbuyomu. Ine ndinazinenapo izo kwa anthu angapo, koma osati kwa gulu mmbuyomo, monga ine ndikudziwira.

453 Ine—ine ndinalota, pafupifupi mwezi zitatha kuchitika zijazi, kuti ine ndinali nditayima, tsiku lina, ndipo ndinali ndikuipenya nthawi yaikulu yomwe . . . Osati chiweruzo, tsopano. Ine sindikukhulupirira kuti Mpingo ukafika konse kwa icho, (ine ndikutanthauza, Mkwatibwi), kupita ku chiweruzo. Koma, ine ndinali pamenepo pamene makorona anali kuperekedwa, mwaona. Ndipo waukulu—Mpandowachifumu waukulu utayikidwa pamwamba *apa*. Ndipo Yesu ndi Mngelo wolembera, ndi onse, anali atayima pamenepo. Ndipo kunali masitepe opita mmwamba, monga, akutsikira pansi mbali *iyi*, a mnyanga woyera; kumapita pansi, chozungulira, anapanga chowoneka monga *chonchi*, ndipo amatuluka panja, kotero kuti khamu lonse lalikulu ili litayima pamenepo limakhoza kuwona chimene chinali kuchitika.

454 Ndipo ndimakhoza kuimirira cha kumbuyo uko, kumbuyo kutali ku mbali imodzi. Ndipo ndinali nditangoima pamenepo, wopanda lingaliro la momwe ine ndikanayenera kuyendera mmasitepe amenewo. Ine ndinali nditaima pamenepo. Ine ndimakhoza kuwona . . .

455 Mngelo wolemberayo amakhoza kuyitana dzina linalake; ndipo ine ndimakhoza kulidziwa, kulizindikira dzina limenelo. Ine ndinayang'ana, ndipo kumbuyo kutali cha uko, apo panabwera m'baleyo, akuyenda ndi mlongo, anadzayenda mpaka kwa iwe, monga choncho. Mngelo wolemberayo atayima pamenepo pambali ya Khristu, (loto chabe tsopano), ndipo anali kuyang'ana. Ndipo dzina lawo linali pamenepo, ilo linapezeka mu Bukhu la Moyo; Iye amakhoza kuyang'ana pa iwo, ndi

kumati, "Unachi—unachita bwino, wantchito Wanga wabwino ndi wokhulupirika. Tsopano lowa mkati."

456 Ine ndinayang'ana kumeneko, kumene iwo anali kupita. Uko kunali dziko latsopano, ndi zisangalalo. Ndipo anati, "Lowa mu zisangalalo za Ambuye, zomwe zakhala—zomwe zakhala ziri zanu chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi." Mukuona? Ndipo, oh, ine ndinaganiza . . . Iwo amakhoza kudutsa kupyola pamenepo, ndi kumakumana wina ndi mzake, ndipo akungosangalala, ndi kumapita kudutsa mmapiri ndi malo aakulu opambana.

457 Koma ndinaganiza, "Oh, kodi zimenezo si zodabwitsa! Ulemelero! Aleluya!" Kumangolumpha chokwera ndi chotsika!

458 Ndiye ine ndimakhoza kumva dzina lina likuyitanidwa. Ine ndinaganiza, "Oh, ine ndikumudziwa iye. Ine ndikumudziwa iye. Ine . . . Uko, apo iye akupita, kumeneko." Ndikumuwona iye monga chomwecho.

"Lowa mu zisangalalo za Ambuye, wabwino Wanga ndi . . . "

"Oh," ine ndimakhoza kunena kuti, "Mulungu alemekezeke! Mulungu alemekezeke!"

Kumangoti, mwachitsanzo, monga iwo amati, "Orman Neville," mwaona.

459 Ndiyeno ine nkumati, "Ameneyo ndi M'bale Neville wakale uja. Ndi ameneyo apo." Mukuona? Ndipo apa iye akubwera, kuchokera mu unyinji, akupita mmwamba.

460 Tsopano Iye nkuti, "Lowa mu zisangalalo za Ambuye, zomwe zakhala zitakonzedwera iwe maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Lowani mkati." Ndipo M'bale Neville wachikulire uja nkungosintha, ndipo nkungoyambiranso kubwerera mmenemo, akungofuula ndi kukuwa.

461 Mnyamata, ine ndikungofuula ndi kumati, "Ulemelero kwa Mulungu!" Nditayima cha apa ndekha ndekha, ndikukhala ndi nthawi yodabwitsa, ndikuwawona abale anga akulowa mkati.

462 Ndipo Mngelo wolemberayo anayima pamenepo, ndipo anati, "William Branham."

463 Ine sindinaganize nkomwe kuti ndimayenera kuyenda mmenemo. Kotero ndiye ine ndinachita mantha. Ine ndinaganiza, "Oh, mai! Kodi ine ndiyenera kuchita zimenezo?" Kotero ine ndinapita ndikuyenda kumusi uko. Ndipo basi aliyense akundisisita ine pa—pa . . . [M'bale Branham akudzisisita yekha nthawi zambiri—Mkonzi]. "Moni, M'bale Branham! Mulungu akudalitseni inu, M'bale Branham!" Akundisisita ine pamene ndinkapita motsatira, kudutsa mu unyinji wawukulu wopambana wa anthu. Ndipo onse a iwo akufikira ndi kumandisisita ine monga *choncho*. "Mulungu akudalitseni inu, m'bale! Mulungu akudalitseni inu, m'bale!"

464 Ine ndinali kupita. Ine ndinkati, "Zikomo inu. Zikomo inu. Zikomo inu." Monga kutuluka kuchokera mu msonkhano, kapena chinachake, inu mukudziwa.

465 Ndipo ine ndinali kupita kukayenda mmasitepe a minyanga aakulu opambana awo. Ine ndinayamba kuyenda kudutsa pamenepo. Ndipo nditangoponda sitepe yoyamba, ine ndinayima. Ndipo ine ndinaganiza . . . Ine ndinayang'ana pa nkhope Yake. Ine ndinaganiza, "Ine ndikufuna ndimuyang'ane Iye bwinobwino mbali iyi." Ndipo ine ndinayima.

466 Manja anga anali monga *chonchi*. Ine ndinamva chinachake chikukoleka mu nkono mwanga *apa*. Iwo unali nkono wa winawake. Ine ndinayang'ana pozungulira, ndipo apo panayima Hope; maso aakulu akuda amenewo, ndi tsitsi lakuda ilo likulendewera pansi kumbuyo kwake, atavala mkanjo woyera; akuyang'ana mmwamba pa ine monga choncho. Ine ndinati, "Hope!"

467 Ine ndinamverera chinachake chitagunda nkono *uwu*. Ndinayang'ana pozungulira, ndipo apo panali Meda; maso akuda awo akuyang'ana mmwamba, ndipo tsitsi lakuda ilo likugwera mmusi, atavala mkanjo woyera. Ndipo ine ndinati, "Meda!"

468 Ndipo iwo anayang'anana wina ndi mzake, inu mukudziwa, monga choncho. Iwo anali . . . Ine ndinawagwira iwo mmikono yanga, ndipo apa ife tinapita, tikupita Kwathu.

469 Ine ndinadzadzuka. Oh, ine ndinadzadzuka. Ndipo ine—ine ndinadzuka ndi kukhala pansi pa mpando, ndipo ndinalira, inu mukudziwa. Ine ndinaganiza, "O Mulungu, ine ndikuyembekeza kuti izo zidzabwera monga chomwecho." Onsewo anayanjana nane mu moyo, ndi kubala ana, ndi zinthu monga chomwecho; ndipo ndi ife apa, tikuyenda kulowa mdziko latsopano, oh, mai, kumene ungwiro ndi chirichonse. Ayi, palibe kanthu . . .

470 Oh, icho chidzakhala chinthu chodabwitsa! Musati muchiphonye icho. Musati muchiphonye icho. Mwa chisomo cha Mulungu, muchite chirichonse chomwe inu mungathe kuchita, ndipo izo zikakhala kwa Mulungu kusamalira zina zonsezo kumeneko.

Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda
Nandigulira chipulumutso changa
Pa Kalvare . . .

471 Tiyeni tiyimbe iyo kachiwiri, ndi mtima wathu wonse. Tsopano tiyeni tikwezere maso athu kwa Mulungu.

Ine ndinkonda Iye

[M'bale Branham wachoka pa guwa kuti akapempherere mlongo, mawu ake sakumveka—Mkonzi].

. . . nkonda Iye

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

472 Chabwino, tsopano. Iye samayembekezeredwa kuti akhala moyo mu msonkhano wonse. Uko nkulondola. Apo iye ali, manja onse ali mmwamba mu mlengalenga, akulemekeza Mulungu. Ndi chifukwa chake ine ndimachedwa pano nthawi yaitali, ndipo ine ndikukuuzani inu zomwe ine ndimachita: Ine ndinali kuyankhula za Meda ndi iwo, ndi kuti ine ndinali kuyang'ana, kuti ndiwone chimene. . . Ine ndimapitirira kumayang'ana mkombero wa Kuwala uwo ukuzungulira mmbuyo ndi mtsogolo, ndipo unapita ndi kukapachikika pa iye. Ine ndinaganiza, "Ndi chimenecho." Oh, kodi sizodabwitsa zimenezo?

Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

473 Tsopano, ndi mitima yathu. . . [M'bale Branham akung'ung'udza *Ine Ndinkonda Iye*—Mkonzi]. Tangoganizani za ubwino Wake ndi chifundo.

. . . Ine ndinkonda Iye (Ameni!)
. . . Iye anayamba kundikonda. . .

474 Tsopano mwaona momwe ubwino wake uliri? Ameni! Ndi zimenezotu. Tsopano. . . ?. . . Pitani ndipo mukakhale bwino. Ameni! Chisomo cha Mulungu chawonekera kwa inu, kukupangani inu wabwino. Ameni.

. . . pa mtengo wa Kalvare.

Oh, ulemelero kwa Mulungu!

Ine ndinkonda Iye, . . .

Chabwino, abusa anu.

Ine. . .

475 [Winawake akuti, "M'bale Branham, mawa udzayamba pa hafu pasiti-naini?"—Mkonzi]. Naini mpaka hafu pasiti-naini. Naini koloko, penapake pamenepo. ["Titatha kudya kadzutsa? Naini koloko?"] Inu mudzayambe pa naini. Ine ndidzayamba pa hafu pasiti-naini.

63-0323 Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chivumbulutso Cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org